CHIKONDI

CHA

MULUNGU

Monga momwe chinaonetsedwa mu Moyo, Imfa ndi Kuukanso kwa akufa kwa Ambuye Yesu Khristu.

Wolemba

I.A. Sadler

CHIKONDI CHA MULUNGU

Wolemba

I.A. Sadler

Losindikiziwda ndi mlembi:

1 Payne Close, Chippenham,

Wiltshire, SN15 3FX, England.

Copyright I.A. Sadler 2006

Lachingerezi linasindikizidwa ndi Cromwell Press, Trowbridge, Wiltshire.

Lasindikizidwa ndi ……..Blanytre, Malawi.

M,malo mwa Free Grace Evangelistic Association.

1 Payne Close, Chippenham,

Wltshire, SN15 3FX, England.

Ndi ulamuliro wa wolemba bukhuli.

Lamasulidwa kupita mu Chichewa ndi: Pastor Elwyn E E Maliwa,

PO Box 502,

Balaka,

Malawi.

Mobile: +265 888332761

E-mail: eeemaliwa@yahoo .com.

Mabuku ena olembedwa ndi Dr I.A. Sadler.

"Chinsinsi, Babulo Wamkulu" – Mpingo wa ku Roma ndi European Union zionetsedwa mu kuwala kwa choonadi.

"Yesu Ndiye Njira" Kuyenda mu njira ya chipulumutso, osatembenukira ku dzanja la manja kapena la kumanzere.

"Jesus, El Camino" Bukhu la Yesu ndiye Njira la chilankhulo cha chi Spanish.

MAU OTSOGOLERA.

Wolemba ndi Pastor G D Buss.

Old Baptist Chapel, Chippenham, England.

Palibe phunziro lalikulu kapena lokoma lomwe likuyenera kudzala m'malingaliro a okhulupirira kuposa la chikondi cha Mulungu. Ichi ndicho chidzalo cha chimwemwe cha kumwamba, ndipo chiyenera kukhala chokondweretsa cha oyera mtima pa dziko la pansi.

Wolemba wafuna kuti akhazikitse mosavuta zina za zinthu zomwe ndi chikondi chozamachi, kutsatira mitsinje yoyenda kuchokera kwa aliyense wa Utatu wa Mulungu, maka maka monga momwe chaonetsedwera mu ntchito ya Ambuye Yesu Khristu monga Muomboli. Ili ndi vumbulutso la Uzimu ndi chidziwitso chopulumutsa cha choonadi cha umulungu chimene chimabweretsa chidwi chokoma cha ziphunzitso za chisomo mu mtima wa munthu wochimwa yemwe wapulumutsidwa. Pomuthangatira kuti agwirizane ndi ndakatulo iyi:

'Chifukwa chiani ndinapangitsidwa kuti ndimve liu lake,
Ndiponso kulowa nthawi yomwe malo alipo;
Pomwe zikwi za anthu akupanga chisankho choononga
Ndi kuti akhale opanda chakudya m'malo mobwera?'

'Chinali chikondi chomwecho chimene chinamwaza phwando.
Chimene chinatikakamiza kulowa mokoma;
Kapena tikadakanakanabe kulawa,
Ndi kuonongeka mu uchimo wathu.

(Watts)

Zikomere Mzimu Woyera, kuti ambiri a iwo omwe awerenge bukhu ili mwa chiphunzitso chake athe kulankhulanso chilankhulo chomwecho kuchokera m'mitima yawo.

ZA MKATIMU.

MUTU 1. Chikondi cha Mulungu Chagwiro ndi Choyera…… 7

Chikondi ndi chiyani? – Chikondi chosatha ndi chosakanidwa cha Mulungu – Chiyero cha Mulungu chomwe chili mu chikondi Chake – Mulungu ndi wokhulupirika – Chipangano Chatsopano – Mwana wa Nkhosa wa Mulungu.

MUTU 2. Yesu, Kuunika kwa Dziko lapansi…… 16

Emmanuel, Mulungu nafe – Chisomo ndi kudzichepetsa kwa Ambuye Yesu – Chitsanzo cha chikondi cha Muomboli wathu – Yeserolo – Njira ya Mchipululu – Zozizwazo – Muthange mwafuna Ufumu Wakumwamba –Zozizwa za Chisomo – Chikondi cha Mulungu chovumbulutsidwa mwa Uzimu – Wansembe Wamkulu wathu.

MUTU 3. Getsemane…… 28

Chidziwitso – Yesu apempherera anthu Ake – Yesu asenzera anthu Ake Machimo awo – Kumva Zowawa kwa Yesu M,munda wa Getsemane – Ameneyo Ndine – Yesu pa bwalo la Akulu – Kukana Yesu kwa Petro ndi chikondi cha mphamvu cha Ambuye – Yesu pa bwalo la Pilato.

MUTU 4. Palibe munthu yemwe ali ndi Chikondi chachikulu chotere…… 38

Mphamvu ya Mzimu – Yesu alamulidwa kuti Aphedwe, Mpingo upatsidwa Ufulu – Yesu Anakwapulidwa – Chisoti cha Minga – Tsiku Lotetezera – Chikondi cha Mphamvu ndi chokondetsa cha Ambuye – Chipatso cha Mzimu – Chikondi cha Umulungu ndi kupindula m,Mipingo.

MUTU 5. Kupachikidwa pa Mtanda…… 48

Yesu yekha – Kalvari – Yesu Wansembe Wamkulu – Wachifwamba Akumwalira – Mdima – Chokhumba cha Ambuye kwa Anthu Ake – Kwatha – Munthiti Mobaidwa mwa Yesu.

MUTU 6. Muwomboli Wouka kwa Akufa ndi Wopatsidwa Ulemerero……. 63

Yesu Adzivumbulutsa Yekha – Kufunikira kwa kuuka kwa Akufa – Kukwera kwake kwa Kumwamba – Mpulumutsi wopatsidwa Ulemerero – Zotsatira mu Moyo wa Okhulupirira – Tamandani Ambuye Waulemerero.

MAU OTSOGORERA.

Kuyambira pomwe bukhu la *"Yesu Ndiye Njira"* linasindikizidwa ambiri a omwe awerenga bukhuli amafunsa ngati tili kulemba bukhu lina. Komabe, wolemba akuona kufunikira kwa chitsimikizo chochokera kwa Ambuye mu ntchito yotereyi. Ngati pangakhale kuti pakhoza kukhala dalitso lina lake, likhoza kubwera kudzera mu ntchito yamphamvu ya Mzimu Woyera mu mtima ndi moyo wa owerenga. Kuzindikira izi ndi chinthu chabwino. Mau a Ambuye amamveka bwino lomwe: "pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu." (Yohane 15:5). Koma pali lonjezo lodabwitsa ili, "Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo" (Afilipi 4:13).

Pakhala ma umboni ambiri kuchokera ku dziko la kwathu ndiponso ku maiko a kunja, kuti Ambuye mwa chisomo chake wayankha mapemphero osweka mtima okhudzana ndi bukhuli la *"Yesu Ndiye Njira".* Popempherera nkhani izi ndi kuzitula pamaso pa Ambuye, tinamva kukhazikitsidwa kwa lonjezo la Uzimu; "Ndi Aseri anati, Aseri adalitsidwe mwa anawo; Akhale wovomerezeka mwa abale ake, Aviike phazi lake m,mafuta. Nsapato zako zikhale za chitsulo ndi mkuwa; Ndipo monga masiku ako momwemo mphamvu yako" (Dueteronomo 33:24-25). Kotero kuti, tikulembanso bukhu lina pofunafuna ulemu ndi ulemerero wa Mulungu.

Katundu wa pa mizimu yathu, ndi kulemba zokhudza chikondi cha Mulungu, makamaka monga chaonetsedwa potumiza Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye Yesu Khristu, kupereka moyo Wake pa mtanda. "Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake kwa ife chikondi chake cha mwini yekha m,menemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu adatifera ife." (Aroma 5:8). Chikondi cha Umulungu chimasungunula mtima wouma ndi kubweretsa kulapa ndi chiyanjanitso ndi Mulungu. Ngakhale kungoyang'ana mwachidule mwa chikhulupiriro za chikondi cha Yesu zimatsitsimutsa moyo wolemetsedwa ndi uchimo ndi mavuto a moyo uno. Kutsutsana komvetsa chisoni komwe kumakhalapo pakati pa okhulupirira kumatha mwa nthawi yochepa, pomwe Mzimu Woyera watsika ndi mphamvu mu mpingo ndi kuvumbulutsa chikondi cha Muomboli.

Bukhu ili likhoza kukhudza phunziro lozama ili ndi la ulemerero; komatu pali uthunthu mwa Ambuye Yesu Khristu, mutu wamoyo wa Mpingo. "Chifukwa mwa kudzala kwake tinalandira ife tonse chisomo chosinthana ndi chisomo" (Yohane 1:16). Mwa Yesu Khristu ndi momwe chiyembekezo chathu chigonera. Pempho ndi lakuti wowerenga atsogozedwe ndi Mzimu Woyera kuti apemphere moona mtima kwa Ambuye chifukwa dalitso lomwe lalankhulidwa ndi wolemba Masalmo Davide; "mudzandidziwitsa njira ya moyo: Pankhope panu pali chimwemwe chokwanira: Mdzanja lanu la manja muli zokondweretsa zomka muyaya. (Masalmo 16:11).

Bukhu ili laperekedwa mwapadera kwa abale aku Africa. Ena mwa abale omwe tiwadziwa pawokha ndipo tinamva kumangiririka kwa ubale wa chikondi mwa Ambuye Yesu Khristu,

komanso pali ena ambiri omwe sakudziwika. Ngakhale ziri choncho, kaya akudziwika kapena sakudziwika kwa ife, aliyense amadziwidwa ndi Mulungu; ndipo tipemphera kuti bukhu ili likhale mdalitso mwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

Baibulo lomwe mavesi olembedwa mbukhuli atengedwa.

Mavesi a Mau a Mulungu omwe agwiritsidwa ntchito atengedwa mu Baibulo la Chichewa lotchedwa "Buku Lopatulika Ndilo Mau A Mulungu" losindikizidwa mchaka cha 1997.

MUTU 1

CHIKONDI CHANGWIRO NDI CHOYERA CHA MULUNGU

Chikondi ndi Chiyani?

Chikondi ndi chochitika chomwe chionetsedwa ku dziko lakugwa ndi lochimwali lomwe milomo ndi malingaliro a anthu ndizodzazidwa ndi mau akuti "chikondi". Koma ndi angati omwe amadziwa tanthauzo lake lenileni? Tikamawona zochitika za nyengo ino, dziko lapansi likuoneka kuti likufanana ndi zochitika za nthawi ya Nowa pomwe "dziko lapansi linadzaza ndi ziwawa", (Genesis 6:11). Kwa diso lomwe likukhulupirira lomwe liyang'ana ndi chikhulupuriro, zinthu izi ndi zizindikiro za masiku omaliza. Yesu analankhula za kubweranso Kwake kwachiwiri mu ulemerero; "Ndipo monga kunakhala masiku a Nowa, momwemo kudzakhalanso masiku a Mwana wa munthu. Anadya, anamwa, anakwatira, anakwatiwa, kufikira tsiku lija Nowa analowa m'chingalawa, ndipo chinadza chigumula, nichiwaononga onsewo. Momwemo kudzakhala tsiku la kuvumbuluka Mwana wa munthu" (Luka 17:26-27,30).

Chofunikira kwambiri pa phunziro lathu ndi kumvetsetsa kuti "chikondi" chitanthauza chiyani. Bukhu la Mtanthauzira Mau likhoza kufotokoza bwino lomwe kuti tanthauzo lake ndi kukhudzika kwabwino kwakukulu komwe munthu amakhala nako pa wina"; komanso timawerenga kutanthauza kwa mitundu ina komwe sikumafotokoza za chikondi choona, koma za chilakolako chonyansa. "Chikondi" chomwe dziko lapansi limalankhula sichifanana ndi cha m,Baibulo, Mau Oyera a Mulungu.

Pa nthawi ino tiyeni tifike ku Mau a Mulungu, chifukwa ndi kumeneko kumene choonadi chimapezeka. Tipemphe Mzimu Woyera kuti atsegule kumvetsetsa kwathu kwa Mau a Mulungu ndi kukhazikitsa dalitso lolemera losatha pa ife. Mwa njira iyi tingathe kupeza chithunzithunzi chabwino cha Mulungu ndi machitachita Ake omwe amachita kwa anthu. Tiyeni potero titenge

mwakusamalitsa ndi kuchita zomwe Ambuye wazivumbulutsa mu Mau a Mulungu zokhudza chikondi.

Mtumwi Yohane, wophunzira yemwe mwapaderadera anadziwa za chikondi cha Ambuye Yesu, analemba motere." Okondedwa, tikondane wina ndi mnzake: chifukwa kuti chikondi chichokera kwa Mulungu, ndipo yense amene akonda, abadwa kuchokera kwa Mulungu, namzindikira Mulungu. Iye wosakonda sazindikira Mulungu: chifukwa Mulungu ndiye chikondi. Umo chidaoneka chikondi cha Mulungu mwa ife, kuti Mulungu anatuma Mwana wake wobadwa yekha alowe m'dziko lapansi kuti tikhale ndi moyo mwa Iye. Umo muli chikondi sikuti ife tinakonda Mulungu, koma kuti Iye antikonda ife, ndipo anatuma Mwana wake akhale chiombolo chifukwa cha machimo athu. Okondedwa, ngati Mulungu anatikonda ife kotero, ifenso tiyenera kukondana wina ndi mzake. Palibe munthu adamuona Mulungu nthawi iri yonse; tikakondana wina ndi mnzake, Mulungu akhala mwa ife, ndi chikondi chake chikhala changwiro mwa ife. (1 Yohane 4:7-12).

Apatu tikuona tanthauzo lozama,"Mulungu ndiye Chikondi". Chionetsero chabwino cha chikondi chiyenera kupezeka mwa Mulungu yekha, ndi Umulungu womwe Iye ali, ndi kutuma kwa Mwana wake Wobadwa yekha, Ambuye Yesu Khristu.

Chikondi chosatha ndi chosakanizidwa cha Mulungu.

Tafunsa kuti, chikondi ndi chiyani? Apa tikutengegeredwa ku funso loposa mafunso onse; lakuti Mulungu ndi ndani? Kuti timvetsetse yankho la funso lofunika kwambiri ili, tiyenera kuti tifufuze Mau a Mulungu. Pokhapokha titamudziwa Iye, monga mwa vumbulutso la Mzimu Woyera kwa ife payekha payekha, sitingakhale ndi chiyembekezo choona kapena maziko a chipulumutso. Yakobo akutichenjeza kuti; "Ukhulupirira iwe kuti Mulungu ali m'modzi; uchita bwino ziwanda zikhulupiriranso, ndipo zinthunthumira." (Yakobo 2:19) Izi zikhoza kukhala bwino kuti ndi zomwe ambiri omwe amangotchula ndi pakamwa dzina la Ambuye, koma miyoyo yawo imasonyezeratu kuti samudziwa Iye ndi njira ya umulungu yokonzedweratu ya chipulumutso.

Mulungu yemwe ali Atatu mwa M'modzi, Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera analipo chiri chonse chisanakhale. Baibulo limayamba ndi Mau akuti, "Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi" (Genesis 1:1). Pamenepa anali kulankhula za Mau, amene ali Mwana wa mwamuna wamuyaya wa Mulungu, komanso Yohane Mtumwi akuyamba Uthenga Wabwino ndi mau omwewo, "Pachiyambi panali mau ndipo mau anali kwa Mulungu". (Yohane 1:1) Ambuye Mulungu sikuti anangokhalapo china chiri chonse chisanakhale kokha, komanso Ali wachikhalire ndiponso wamuyaya. Dzina lake ndi "Ine yemwe ndiri Ine" (Ekzodo 3:14).

Monga Ambuye Mulungu ali wa muyaya, chomwechonso chikondi chake chichokera ku nthawi zosayamba kufikira nthawi zosatha, chopanda chiyambi kapena chopanda mathero. Izi zafotokozedwa bwino ndi mneneri Yeremiya, "Yehova anaonekera kwa ine kale, ndi kuti Inde,

ndakukonda iwe ndi chikondi chosatha; chifukwa chake ndakukonda iwe ndi kukukomera mtima (Yeremiya 31:3). Chotero tiwerenga kuti chikondi chake chiri patsogolo pa chikondi china chiri chonse chomwe mpingo uli nacho kwa Mulungu. “Tikonda chifukwa anayamba ndiye kutikonda.” (1 Yohane 4:19).

Ambuye sali wamuyaya kokha ai, komanso wamphamvu yonse, Mulengi yemwe amakwaniritsa kuchita zonse zolinga Zake zamuyaya. (Yesaya 14:27 ndi 46:9-11, Daniel 4:34-35). Kotero kuti chikondi cha Mulungu ndi cha mphamvu zonse ndiponso sichingakanizidwe. “Anthu anu adzadzipereka eni ake tsiku la chamuna chanu” (Masalmo 110:3)

Tiyeni tisiyanitse izi ndi chikondi cha munthu, chomwe nthawi zambiri chimafooketsedwa komanso kugwiritsidwa ntchito mosapindulitsa. Bambo akhoza kukonda mwana wake, koma mwanayo ndi kukana chikondi cha bambo wake, bambowo akhoza kukonda mai, koma maiyo ndi kusabwezera chikondi kwa bamboyo. Komabe, siziri choncho ndi Mulungu yemwe amakhala ndi chikondi chake cha mphamvu yonse. Ambuye Yesu ananena, “Kulibe m’modzi akhoza kudza kwa Ine koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomariza’. (Yohane 6:44). Kotero kuti mpingo umalira mwa chikhulupiriro, “Undikoke tikuthamangire”. (Nyimbo ya Solomo 1:4).

Pokoka wochimwa kumubweretsa kwa Iye mwini, Ambuye Mulungu amawala mu mtima. Mtumwi Paulo analemba kuti, “Pakuti Mulungu amene anati, Kuunika kudzawala kuturuka mumdima, ndiye amene anawala m’mitima yathu kutipatsa chiwalitsiro cha chidziwitso cha ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Khristu” (2 Akorinto 4:6). Sipakhala mdima pamane chikondi cha Mulungu chatsanulidwa mu mtima mwathu. “Mulungu ndiye kuunika, ndipo mwa Iye milibe mdima” (1 Yohane 1:5). Ndi pokhapo pomwe Mulungu atiwalitsira chikondi, pamane wochimwa amaona ndi kumvetsetsa za chikondi cha Mulungu. Wolemba Masalmo akutamanda Ambuye motere, “Pakuti chitsime cha moyo chiri ndi Inu; M’kuunika kwanu tidzaona kuunika; Tanimphitsani chifundo chanu pa iwo akudziwa inu”, (Masalmo 36:9-10).

Chiyero cha Mulungu chomwe chili mu chikondi chake.

Kodi tinene kuti Ambuye amawalitsira mu mtima ndi kuunikira anthu onse omwe akhala ndi moyo? Kodi Mulungu amakonda anthu onse mofanana? Kwa anthu ambiri awa ndi mafunso ovuta, koma Ambuye sanatisiye popanda yankho m,Mau a Mulungu.

Ambuye analankhula motero mu chiphunzitso cha pa phiri; “Kondanani nawo adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu; kotero kuti mukakhale ana a Atate wanu wa Kumwamba; chifukwa Iye amakwezera dzuwa lake pa oipa ndi pa abwino namavumbitsira mvula pa olungama ndi osalungama. “ (Mateyu 5:44-45). Mulungu monga Mulengi amaonetsa ukoma

mtima, chisamaliro ndi kukwaniritsa zosowa kwa onse, koma ichi sichikondi chopulumutsa chomwe sichidzathera muyaya.

Chikondi cha munthu chikhoza kusayang'anira zolakwika ndi kulephera kuzindikira chomwe chiri cha uchimo mwa iwo omwe ali owakonda. Komabe, Mulungu ndi Woyera mwangwiro ndipo ayenera kulanga chimo lomwe liri kusayeruzika. "(1 Yohane 3:4). Kuonjezera apo, Mulungu ndi woona (Dueteronomo 32:4), wolungama (Ezra 9:15), Woyera (Habakuk 1:13, 1 Yohane 3:3) ndi wachiyero. (Levitiko 11:44) (1 Petro 1:15-16). Ali Mulungu wansanje ya chiyero. (Eksodo 34:14) Wolemba Masalmo Davide analemba kuti, "Pakuti Inu sindinu Mulungu wakukondwera nacho choipa, Mphulupulu siikhala ndi Inu. Opusa sadzakhazikika pamaso panu, Mudana nawo onse akuchita zopanda pake" (Masalmo 5:4-5).

Kukadakhala kuti wolemba Masalmo adalekezera pamanepa, pakadakhala popanda chiyembekezo kwa wina aliyense, popeza "Palibe m'modzi wolungama, inde palibe m'modzi" ndipo " onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu." (Aroma 3:10,23). Koma Davide akupitiririabe kulankhula za chifundo cha Mulungu ndi chilungamo chomwe sichili cha munthu mwini yekha. "Koma ine, mwa kuchuruka kwa chifundo chanu ndidzalowa m'nyumba yanu: Ndidzagwada kuyang'ana Kachisi wanu woyera ndi kuopa Inu. Yehova, munditsogolere m'chilungamo chanu, chifukwa cha akundizondawo," (Masalmo 5:7-8). Chimodzimodzinso mu Salmo lina timawerenga kuti, "Ndikwatuleni m'chilungamo chanu, ndi ndikundilanditsa." (Masalmo 71:2).

Zoonadi izi ndi zomwe zinali dalitso loposa kwa Martin Luther m'nyumba ya A bambo a chi Katolika. Anaphunzitsidwa za chiyero cha Mulungu, anaona kukhumba kuchita zoipa mu mtima mwake, ndi chiweruzo cha imfa chomwe chinafikira pa anthu onse kuyambira pa kuchimwa kwa Adamu. (Genesis 2-3) Martin Luther anayesetsa kwambiri kuti akonze zolakwika ndi kukhazikitsa chiyero chake, pafupifupi kufika pa muyeso odzipha ndi zinthu zomwe amadzipweteka nazo yekha. Komabe, sizinatheke kuti adziphe mpaka pomwe Mzimu Woyera anamuvumbulutsira iye kuti chilungamo chomwe iye amachifunafuna chimapezeka mwa Mulungu mwa chikhulupiriro. "Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chiri mphatso ya Mulungu; chosachokera ku ntchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense. Pakuti ife ndife chipango chake, olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo." (Aefeso 2:8-10).

Chikondi cha Mulungu sichingaonetsedwe popanda kukwaniritsa chilungamo cha umulungu ndi chilango chomwe chimaperekedwa chifukwa cha uchimo. Mulungu akadatha kuchita chilungamo, akadaweruza mtundu wa anthu onse ochimwa nawaponya ku chilango chosatha ku Gahena. Koma lidalitsike dzina Lake, wakwaniritsa zolinga zake kuti apulumutse iwo omwe Mau a Mulungu akuwatchula "osankhika" (1 Petro 1:2, Tito 1:1, Marko 13:27). Izi sizitengera

ubwino wina uli wonse mwa iwo osankhidwawo, koma chifukwa cha Ambuye m'chikondi akhoza kusankha wochimwa woipitsitsa kuti awaonetsere chifundo chake chachikulu. (1 Timoteo 1:15) Pomwe Ambuye adalengeza dzina lake kwa Mose, anakhazikitsa motere; "Ndipo Yehova anapita pamaso pake, napfuula, Yehova, Yehova, Mulungu wachifundo ndi wachisomo, wolekereza, ndi wa ukoma mtima wochuruka, ndi wa choonadi; wakusungira anthu osawerengeka chifundo, wakukhulukuira mphulupulu ndi kulakwa ndi kuchimwa; koma wosamasula woparamula; wakulanga ana ndi zidzukulu chifukwa cha mphulupulu ya atate ao, kufikira mbadwo wachitatu ndi wachinayi." (Eksodo 34:6-7).

Paulo analembanso za chikondi cha Mulungu ku mpingo wa ku Aroma, kwa anthu ake a Mulungu osankhika, pomvetsa bwino lomwe za machitachita a Mulungu ndi ena a mtundu wa anthu "Koma Rabekanso, pamene anali ndi pakati pa m'modzi, ndiye kholo lathu Isake; pakuti anawo asanabadwe, kapena asanachite kanthu kabwino kapena koipa, kuti kutsimikiza mtima kwa Mulungu monga mwa kusankha kukhale, si chifukwa cha ntchito ai, koma chifukwa cha wakuitanayo, chotero kumanenedwa kwa uyo, Wamkuru adzakhala kapolo wa wang'ono. Inde monga kunalembedwa, Ndakukonda Yakobo, koma ndinamuda Esau. Ndipo tsono tidzatani? Kodi chiripo chosalungama ndi Mulungu? Msatero ai. Pakuti anati ndi Mose, Ndidzachitira chifundo amene ndimchitira chifundo, ndipo ndidzakhala ndi chisoni kwa iye amene ndikhala naye chisoni. Chotero sichifuma kwa munthu amene afuna, kapena kwa iye amene athamanga, koma kwa Mulungu amene achitira chifundo." (Aroma 9:10-16),

Monga chili choonadi chovumbulutsidwa mwa umulungu kuti chikondi cha Mulungu chili ndi mphamvu zoposa, kotero ndi lamulo la umulungu ku mpingo kuti uthenga wabwino wa chipulumutso wa Yesu Kristu uyenera kulalikidwa (koma osati kuperekedwa) kwa onse, kaya amva kapena ayi. Tsoka kwa munthu yemwe angafune kuletsa kulalikira kwa uthenga wabwino kwa ochimwa, chifukwa ndi njira yokhazikitsikidwa ndi Mulungu! "Woyang'ana mphepo sadzafesa; ndi wopenya mitambo sadzakolola. Monga sudziwa njira ya mphepo, ngakhale makulidwe a mafupa m'mimba ya mkazi ali ndi pakati momwemo sudziwa ntchito za Mulungu amene achita zonse. Mamawa fesa mbeu zako, madzulonso osapumitsa dzanja lako; pakuti sudziwa ziti zidzalola bwino ngakhale izizi, ngakhale izozo, kaya zonse ziwiri zidzakhala bwino." (Mlaliki 11:4-6).

Mulungu ndi Wokhulupirika.

Monga momwe Ambuye ali wa mphamvu yonse mu chikondi chake, koteronso ali wosasintha mu pangano Lake lomwe tilipeza m'Baibulo. Pangano losatha la chisomo cha Mulumgu lomwe Mulungu wakhazikitsa ndi munthu liri lokhazikika. Ambuye analankhula kudzera mwa wolemba Masalmo, "Sindidzaipsa chipangano changa, kapena kusintha mau oturuka m'milomo yanga." (Masalmo 89:34). Chimodzimodzinso kwalembedwa; "Pakuti ine Yehova sindisinthika, chifukwa chake inu ana a Yakobo simudzathedwa." (Malaki 3:6). Pomangika pa choonadi cha umulungu

ichi ndi pomwe pali kukhulupirika kwa Mulungu. “Chifukwa cha kusathedwa ife ndicho chifundo cha Yehova, pakuti chisoni chake sichileka; Chioneka chatsopano m’mawa ndi m’mawa; mukhulupirika ndithu.” (Maliro 3:22-23). Monga kuti Ambuye sasintha, momwenso chikondi chake sichisintha.

Chifundo chotani ichi pomwe choonadi ichi chagwiritsidwa mu mtima mwa Mzimu Woyera mkati mwa mayesero ndi zowawa! Zoonadi izi ndi maziko a chiyembekezo cha okhulupirira cha chipulumutso chamuyaya. Pamene kudzera mu chimo ndi kusakhulupirira kawirikawiri timakankhidwira m’mwamba ndi pansi m’maganizo athu, monga anthu akumva zambiri mwa ife. Mayasero ndi zotiyesa zomwe nthawi zina zimabweretsa chikayiko pa chiri chonse; komatu Ambuye sasintha. Timafuna titapemphera kuti chikhulupiriro chikule kuti tikhoza kufikira pa malonjezano akulu ndi a mtengo wapatali, kuti tipatsidwe maonekedwe abwino auzimu a ndakatulo iyi.

Mulungu amayendetsa mwazinsinsi

Zozizwa zake kuti achite

Amaponda mapazi ake mnyanja

Nakwera pamwamba pa funde.

Mozama M’migodi

Za ukadaulo osalephereka

Amasamalira luso la mapangidwe ake

Ndi kugwiritsa chifuniro cha mphamvu yake yaikulu.

Inu, Okhulupirika a mantha

Mitambo yomwe mumaiopa kwambiri,

Ndi yaikulu ndi chifundo, idzasweka

Mdalitso pa mutu wanu.

Musaweruze Ambuye ndi malingaliro ofooka,

Koma dalirani Iye pa chisomo chake;

Kumbuyo kwa kukwaniritsa kosavomereza

Amabisa nkhope yomwetulira.

Zolinga zake zidzapsya msanga,

Kumasulidwa ora liri lonse;

Mphukira ikhoza kulawa zowawa,

Koma duwa lidzakhala lokoma.

Kusakhulupirira kumalakwitsitsa ndithu.

Ndi kugwira ntchito ya mosapindula;

Mulungu ndi wodzitanthauzira mwini.

Ndipo adzaiwonetsera.

(Cowper)

Chipangano Chakale ndi Chatsopano.

Tiyenera kuti tibwererenso kuti tiganizire moposera za "pangano losatha, lolongosoka mwa zonse ndi losungika." (2 Samuel 23:5). Izi zikutitsogolera mwapaderadera ku mutu omwe uyenera kukhala chimwemwe cha okhulupirira aliyense, womwe ndi kubwera kwa Ambuye Yesu Khristu monga Mwana wa Nkhosa wa Mulungu.

Mtumwi Paulo akulankhula za mapangano awiri akulu omwe Mulungu anapangana ndi munthu (Agalatiya 4:24-26); loyamba ndilochokera pa phiri la Sinai, lodziwika bwino ndi dzina lakuti Chilamulo cha Mose ndipo limafotokozedwa mwachidule mu Malamulo Khumi a Mulungu. Mose "Ndipo anatenga bukhu la Chipangano nawerenga m'makutu a anthu; ndipo iwo anati, zonse zimene Yehova walankhula tidzachita, ndi kumvera." (Eksodo 24:7) Tawerenga kuti "Pakuti Mose walemba kuti munthu amene achita chilungamo cha m'lamulo adzakhala nacho ndi moyo. (Aroma 10:5 kukamba Levitiko 18:5).

Komatu ndi choonadi chachikulu chakuti palibe munthu wochimwa yemwe angathe kutsatira lamulo la Mulungu; ndipo kusayeruzika ndiye uchimo. (1 Yohane 3:4). Ichi ndi chopangitsa

kufufuza momwe munthu alingaliririra ngakhale kuti “Maganizo opusa ndiwo chimo.” (Miyambo 24:9). Kudzera mu chilamulo timadziwa kuti chimo ndi chiyani. Komabe, Ambuye wakhazikitsa pangano latsopano ndi lamoyo. “Ndidzaika chilamulo changa m’kati mwao, ndipo m’mtima mwao udzachilemba; ndipo ndidzakhala Mulungu wao, nadzakhala iwo anthu anga; ndipo sadzaphunzitsa yense mnansi wake, ndi yense mbale wake, kuti, Mudziwe Yehova; pakuti iwo onse adzandidziwa kuyambira wamng’ono kufikira wamkuru wa iwo, ati Yehova; pakuti ndidzakhululukira mphulupulu yao ndipo sindidzakumbukira chimo lawo.” (Yeremiya 31:33-34 ndipo zalembedwanso mu Ahebri 8:10-12).

Pangano latsopano silidalira pa ntchito zabwino koma ndi la chikhulupiriro. Mtumwi Paulo analemba kuti, “Chifukwa kuti pamaso pake palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo; pakuti uchimo udziwika ndi lamulo. Koma tsopano chilungamo cha Mulungu chaoneka chopanda lamulo, chilamulo ndi aneneri achitira ichi umboni; ndicho chilungamo cha Mulungu chimene chichokera mwa chikhulupiriro cha pa Yesu Khristu kwa onse amene akhulupirira; pakuti palibe kusiyana; pakuti pa onse anachimwa naperewera pa ulemerero wa Mulungu; ndipo ayesedwa olungama kwaulere, ndi chisomo chake, mwa chiombolo cha mwa Khristu Yesu; amene Mulungu anamuika poyera akhale chotetezera mwa chikhulupiriro cha m’mwazi wake, kuti aonetse chilingamo chake, popeza ulungu m’kulekerera kwake analekerera machimo achitidwa kale lomwe.”(Aroma 3:20-25).

Oyera mtima a chipangano chakale adayang’anira kwa Messiah ndi chikhulupiriro. Yesu ananena kuti, “ Atate wanu Abrahamu anakondwera kuona tsiku langa; ndipo anaona nasangalala.” (Yohane 8:56). Nsembe ndi zochita zonse zokhudza chilamulo zinali chithunzi cha Ambuye Yesu ndi Nsembe ya ngwiro. (Ahebri 9-10). Komabe, mpingo wa chipangano chatsopano ndi wamwayi kuti uli ndi vumbulutso lenileni la uthenga wabwino. (1 Petro 1:10-13).

Pangano latsopano la chisomo liri ndi lonjezo lodabwitsa ili kwa ochimwa osauka, “Koma pokwaniridwa nthawi, Mulungu anatuma Mwana wake wobadwa ndi mkazi, wobadwa wakumvera lamulo, kuti akaombole iwo akumvera lamulo, kuti ife tikalandire umwana. Ndipo popeza muli ana, Mulungu anatumiza Mzimu wa Mwana wake alowe m’mitima yathu, wofuula Abba, Atate. (Agalatiya 4:4-7). Kusunga kwa malamulo kumachitika ndi chikondi kudzera mu kupezeka kwa Mzimu Woyera mwa munthu. Mayendedwe owongoka akunja ndi chitsimikizo chooneka ndi maso chomwe ndi umboni kuti Ambuye Yesu walandiridwa monga Mpulumutsi. “Ndipo umo tizindikira kuti tamzindikira Iye, ngati tisunga malamulo ake.” (1 Yohane 2:3). “Koma iye wakupenyerera m’lamulo langwiro, ndilo laufulu. “ (Yakobo 1:25)

Mwana wa Nkhosa wa Mulungu.

Chilamulo cha Mose chidakhazikitsa nsembe zomwe zimayenera kukhetsa mwazi, popeza popanda kukhetsa mwazi panalibe kumasuka. (Ahebri 9:22). Nsembe izi zinali chithunzi ndi chifaniziro cha Mwana wa Nkhosa wa Mulungu, Ambuye Yesu Khristu, wophedwa kuchokera ku chiyambi cha dziko lapansi. Iyeyo si wina koma Mwana wamuyaya wa Mulungu, yemwe anatenga chiyanjano cha umunthu mu Umulungu wake, wopangidwa mwa umunthu weniweni wokhala ndi thupi la munthu ndi moyo, ndipo anabadwira ku Betelehemu namutcha dzina lakuti Yesu (kutanthauza kuti "Mpulumutsi") dzina loperekedwa ndi mngelo wa Mulungu. (Mateyu 1:21). Iye ndi yemwe amene analengeza kwa Mulungu Atate "Pamenepo ndinati, Taonani, ndadza; Mbukhu mwalembewa za Ine; kuchita chikondwerero chanu kundikonda, Mulungu wanga; ndipo malamulo anu ali m'kati mwamtima mwanga(Masalmo 40:7-8).

Mtumwi Paulo akukhazikitsa kuti Ambuye Yesu Khristu ndi chifaniziro chenicheni cha vumbulutso la Mulungu. " Kale Mulungu analankhula ndi makolo mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyanasiyana, koma pakutha pake pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe; ameneyo pokhala ali chinyezimiro cha ulemerero wake, ndi chizindikiro chenicheni cha chikhalidwe chake, nanyamula zonse ndi mphamvu ya Mau ake, m'mene adachita chiyeretso cha zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la Ukulu m'Mwamba. " (Ahebri 1:1-3).

Mulungu Atate mu Umuyaya wake anaona mpingo woomboledwa ndi Ambuye Yesu, Mwana wamuyaya wa Mulungu, pangano lamuyaya, kotero kuti ndi mu kupulumutsa wochimwa woipitsitsa palibe kusintha mu chikondi chake, koma chionetsero ndi vumbulutso chabe la chikondi ndi Mulungu Mzimu Woyera. "Wolemekezeka Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, amene anatidalitsa ndi dalitso lonse la mzimu m'zakumwamba mwa Khristu, monga anatisankha ife mwa Iye, lisanakhazikike dziko lapansi, tikhale ife oyera mtima, ndi opanda chirema pamaso pake m'chikondi. Tiri ndi maomboledwe mwa mwazi wake, chikhululukiro cha zochimwa, monga mwa kulemera kwa chisomo chake." (Aefeso 1:3-4,7).

Mwa Yesu Khristu ndi momwe chikondi ndi chifundo, chilungamo ndi chikhalidwe choyenera zimakwaniritsidwa. "Chifundo ndi choonadi zakomanizana; chilungamo ndi mtendere zapsyopsyonana." (Masalmo 85:10). Kotero kuti Ambuye Yesu, moyo wake, ndipo makamaka imfa yake ndi kuukanso kwa akufa kwake ndilo mutu ndi chandamale cha kulingalira kwathu. Wolemba ndakatulo akutiwonetsera ichi.

Chikondi ndi chiyani, Moyo wanga ukhoza kuyankha,

Wopanda kanthu ayanera kulandira dzina lokondweretsa.

Koma Mulungu Wachikondi, Mpulumutsiyo.

Yemwe mtima wake ndi moto woyaka mosasintha.

Yang'anani Iye, ali mgetsemane,

Tsitsi lake lonyowetsedwa ndi mame ausiku,

Atagwiritsitsa mphamvu za mdima ndi kulimbana nazo

Akukhetsa thukuta la mwazi, kuoneka modabwitsa!

Imvani kubuula Kwake, mpaka Iye, pomaliza,

Alira mwachipambano, Zotheka;

Atasenza mkwiyo wonse

Umene ife unatiyenera wokhawo.

Chikondi nchiyani? Moyo wanga ukadabwezera kunena,

Pamodzi ndi oyera mtima m'mwamba,

Omwe, kudzera mwa Yesu, anapita ku ulemerero,

Yimbani pamodzi, "Ichi ndi chikondi".

(Zion's Trumpet 1838).

Uwu ndiye uthenga wabwino wa Yesu Khristu, womwe uyenera kulalikidwa pa dziko lonse la pansi (Marko 16:15). Kwa Yesu ndiye komwe owomboledwa Ake ndiponso okondedwa akuchitira umboni za chipulumutso chachikulu chotere. Kotero kuti, tiyeni tilingalire pa za chikondi cha Mulungu monga choonetseredwa mwa Ambuye Yesu Khristu, popempherera mwa chikhulupiriro kuti Mzimu Woyera awale mwamphamvu m'mitima yathu. "Pakuti Mulungu anakonda dziko la pansi kotero kuti yense wokhulupirira iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha." (Yohane 3:16).

MUTU 2

YESU KUUNIKA KWA DZIKO LA PANSI.

Emmanuel – Mulungu nafe.

Mwa chitonthozo cha oyera mtima a Chipangano Chakale, Mzimu Woyera anapereka umboni m'Mau a Mulungu kwa Messiah, Mpulumutsi wa dziko lapansi. Kubwera kwa Ambuye Yesu kunaonetsedwa ndi mneneri Yesaya. "Pakuti kwa ife mwana wankhanda wabadwa, kwa ife mwana wamwamuna wapatsidwa; ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lake, ndipo ndipo adzamutcha dzina lake Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha, Kalonga wa Mtendere." (Yesaya 9:6). Kotero kuti pomwe mngelo wa Ambuye anaonekera kwa Yosefe m'maloto, analengeza, "usaope kudzitengera wekha Mariya mkazi wako; pakuti icho cholandiridwa mwa iye chiri cha Mzimu Woyera. Ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo adzamutcha dzina lake Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo." Tsopano izi zonse zinachitika kuti zikwaniritsidwe, zomwe zinalembedwa ndi mneneri (Yesaya 7:14), kunena kuti, "Taonani namwali adzaima, nadzabala mwana wamwamuna, namutcha dzina lake Imanueli ndilo losandulika, Mulungu nafe." (Mateyu 1:20-23).

Mwana wamuyaya wa Mulungu, yemwe ndi wachiwiri pa Utatu wa Mulungu, adatenga umunthu nauyanjanitsa ndi umulungu wamuyaya. Kotero kuti anali Mwana wa munthu ndiponso Mwana wa Mulungu. Anabadwa mu ndondomeko ya fuko la Mfumu Davide; kotero kuti anali mwana wa Davide, komatu ndi yemwe Davide amamuyembekezera mwa chikhulupiriro monga Ambuye ndi Mpulumutsi wake.

Chisomo ndi kudzichepetsa kwa Ambuye Yesu.

Ngakhale kuti Ambuye Yesu anabadwa kuchokera kwa mbadwo wa Mfumu Davide, sanabadwire m'malo aumfumu, koma m'malo odyetsa ng'ombe. Munalibe malo m'nyumba yogona alendo akuti Ambuye Yesu abadwiremo. Ngakhale kuyambira pa kubadwa Kwake, Ambuye Yesu anayenda mu njira yakukanidwa kuti akwaniritse uneneri; "Anali m'dziko lapansi, ndi dziko linalengedwa ndi Iye, koma dziko silinamzindikira Iye. Anadza kwa zake za Iye yekha, ndipo ake a mwini yekha sanamulandira Iye." (Yohane 1:10-11).

Taonani chikondi ndi kudzichepetsa kwa Ambuye Yesu! Ngakhale Iye mwini ndi Mulengi, "Mulungu Wamphamvu" (Yesaya 9:6), Anabwera kudzabadwa mwa umphawi mu Betelehemu. Amadziwa dziko la uchimo chisomo ndi lokhumudwitsa lomwe Iye akanabweramo. Anagonjera ku makolo akuthupi (Luka 2:51) ndipo anakhala m'malo osadziwika bwino masiku ambiri a moyo wake.

Chisomo chodabwitsa chotani chomwe Mwana wamuyaya wa Mulungu, Ambuye Yesu Khristu kuti akhoza kukhala m'moyo wosamuyenera kukhala pamodzi ndi munthu wochimwa! Chifukwa Yesu ndi "amene ali fanizo la Mulungu wosaonekayo, wobadwa woyamba wa chilengedwe chonse; pakuti mwa Iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za pa dziko, zooneka ndi zosaoneka, kapena mipando yachifumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro;

zinthu zonse zinalengedwa mwa Iye ndi kwa Iye. Ndipo Iye ali woyamba wa zonse , ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa Iye." (Akolose 1:15-17). Yesu kubwera kwake sikunali kodzangokhala pa dziko lapansi ai, anadzakhala pa dziko lapansi podziwa imfa yomwe anayenera kufa kumapeto kwa moyo wake, kufera anthu ake akondedwa! Mtumwi Paulo akulengeza za Yesu "Yesu, ameneyo, chifukwa cha chimwemwe choikidwacho pamaso pake, anapirira mtanda, nanyoza manyazi, nakhala pa dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Mulungu." (Ahebri 12:2).

Chitsanzo cha chikondi cha Muomboli.

Chikondi cha Muomboli ndi chitsanzo chaulemelero kwa mkhristu aliyense. Tikuyenera kudzifufuza tokha, kuti tisakhale achinyengo ndi kudzinamiza tokha. Kodi timalolera mwa chimwemwe kutenga malo apansi mu ntchito yake? Kodi timanyamula gori la Ambuye Yesu yemwe anali wodzichepetsa ndi wofatsa mu mtima? (Mateyu 11:29). Komabe, ife timaonetsera momvetsa chisoni za kuuma mtima kwa mitima yathu. Popanda mphamvu, sitingathe kugonjetsa kunyada kwa uchimo komwe tiri nako. Kawiri kawiri timakhumba kudziwerengera oposa anzathu, ndipo timayesetsa kusungitsa ndi kuyesetsa kuchita bwino kuposa m'mbuyo pa zomwe timadziwika kuti timatha kuchita. Koma Ambuye Yesu Mwana wamuyaya wa Mulungu, anadzichepetsa yekha mwa chikondi ndi kumvera pamaso pa Mulungu Atate.

Pomwe ife mwa chikhulupiriro titsatira chitsanzo chake, ndi chimwemwe ndi mtendere wotani womwe umakhala m'miyoyo yathu! Ndi chuma cha kumwamba ndi chikondi chotani chomwe chimavumbulutsidwa ku miyoyo yathu mwa Mzimu Woyera! Koma chotsatira chake ndi chiyani pomwe tamvetsa chisoni Mzimu, natisiya tokha mu mizimu yathu kuti tichite chifuniro chathu m'mipingo? Ndi chionongeko chotani chomwe chimachitika m'mipingo ndi anthu omwe amakonda kudziika apamwamba kuposa ena. Kotero kuti umboni wa atumiki, akulu a mpingo ndi mipingo yonse umachititsidwa manyazi. Pomwe akhristu afuna kuonongana wina ndi mzake, akamayenda mu njira yonyozana ndi manong'onong'o, kodi ndiye kuti akuyenda ndi Ambuye Yesu? Pomwe maso athu akuyang'ana zolakwa za ena, kapena pomwe tisangalala pomva kuti mtumiki akuononga mwa mau amphamvu maina a akhristu, kodi tingatsitsimutsidwe ndi chisangalalo mu chiyanjano ndi Muomboli?

Woipayo amasangalatsidwa kuona Akhristu akuyambana wina ndi mzake ndi kuipangitsa mipingo kuti isanduke bwinja , zomwe zimabweretsa umphawi wauzimu. Mtima wochimwa ukhoza kukhala ndi zinthu zambiri zodzilungamitsira ndi zifukwa zochitira zomwe iye akuchita, monga ngati kuimitsitsa mu choonadi ndi kuteteza miyambo ya mpingo. Komabe, tiyenera kukumbukira modekha kuti tikhoza kulakwitsa njirayo. Mzimu Woyera sadzatsogolera mkhristu ku kunyada komwe kuli kotsutsana ndi Mau Oyera a Mulungu. Ngati tikuganiza kuti tikhoza kukhala ndi chitsogozo cha uzimu ku njira zomapikisana, tidziwe kuti chitsogozo cha uzimu

chotero sichili cha Mulungu Mzimu Woyera, koma ndi mayesero ochokera kwa woipayo ofuna kutifikitsa ku chitamando chachabe.

Tiyeni tisiyanitse izi ndi Ambuye Yesu. Mtumwi Paulo analemba kuti; “Ngati tsono muli chitinthozo mwa Khristu, ngati chikhazikitso cha chikondi, ngati chiyanjano cha mzimu, ngati phamphu ndi zisoni, kukwaniritsa chimwemwe changa, kuti mikalingalire mtima zomwezo, akukhala nacho chikondi chomwe, a moyo umodzi, olingalira mtima umodzi, musachite kanthu monga mwa chotetena, kapena monga mwa ulemelero, wopanda pake, komatu ndikudzichepetsa mtima, yense ayese anzake oposa iye mwini; munthu yense asapenyererenso za mzake. Mukhale nao mtima mkati mwanu umene unalinso mwa Khritsu Yesu, ameneyo pokhala nao maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofanana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala m’mafanizidwe a anthu; ndipo popezedwa m’maonekedwe ngati munthu, anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda.” (Afilipi 2 1-8).

Pomwe mtima uli wonse watengedwa ndi Yesu, nkhwidzi ndi mipatuko zidzatha. Wolemba ndakatulo akuonetsera choonadichi mwachidule koma momveka bwino.

Ndi nthawi iti yomwe akhristu onse angagwirizane,

Ndi kulola kusiyana konse kuti kuthe?

Pomwe, mwa iwo okha waona,

Kuti Khristu ndi zonse mu zonse.

Koma nkhwidzi ndi kusiyana kudzakhalabe koma mochepa,

Pamene anthu adzayerekeza chinthu,

Aloledwe mwakuyimba kuyang’ana kwa Khristu.

Ndipo onse ali amodzi mwa Iye.

(Hart)

Polemba ichi sitikutanthauza kuti Akhristu azinyengerera chooonadi, kapena kuti kusunga mwambo kwa mipingo kusakhalepo. Komabe, ngakhale kusunga mwambo kuyenera kuchitika

mwa chikondi. Chokhumba cha mpingo komanso Mkhristu aliyense chikhale chakuti mbale kapena mlongo yemwe walakwa abwezeretsedwe. (2 Akorinto 2 ndi 7).

Yeserolo.

Tiyenera kuti tsopano tibwererenso ndi kusinkhasinkha za kulowa mu utumiki wa dziko la pansi kwa Ambuye Yesu. Patatha zaka zambiri ali mobisika, nthawi inakwana yakuti adzionetsere yekha mu Israeli ndiponso kuti abatizidwe ndi Yohane Mbatizi." Ndipo panali pamene anthu anali kubatizidwa, ndipo Yesu anabatizidwa, nalikupempherera, kuti panatseguka pathambo, ndipo Mzimu Woyera anatsika ndi maonekedwe a thupi lake ngati nkhunda, nandza pa Iye; ndipo munaturuka mau m'thambo, kuti, Iwe ndiwe Mwana wanga wokondedwa, mwa Iwe ndikondwera. Ndipo Yesu wodzala ndi Mzimu Woyera, anabwera kuchokera ku Yordano, natsogozedwa ndi Mzimu kunka kuchipululu kukayesedwa ndi mdierekezi masiku makumi anayi, Ndipo Iye sanadya kanthu masiku awo; ndipo pamene anatha anamva njala" (Luka 3:21-22, 4:1-2).

Tiyeni tionetsetse chikondi cha Yesu mwa kuti anali ololera kuti ayesedwe ndi woipayo, kuti akhoza kumasula anthu ake ku mayesero a woipayo. Ngakhale kuti Yesu anapangidwa kukhala ngati abale ake, Anali wopanda chimo. Analibe bambo wa chibadwidwe cha thupi, chifukwa Mzimu Woyera anaphimba Mariya namwaliyo (Luka 1:35). Sanayenera kuona chivundi cha fuko la Adamu, koma mwana wake wa Mulungu wobadwa yekha. Ngakhale mwana wa Mulungu, Yesu "anali wakutha kumva zofooka zathu" ndiponso "anayesedwa m'zonse monga momwe ife," (Ahebri 4:15).

Chitonthozo chotani chotere chomwe chiri kwa anthu Ake! Yesu anapita patsogolo pawo mu mayesero ndipo anapambana mdaniyo, Satana. Pomwe tigwa mu zomwe Satana amatiringaliritsa ndi kukodwa m'misampha yake, poganiza kuti ndi mitima yathu yochimwa tiyenera kugonjera ndi kugwa ndithu mu uchimo wakathithi ndi chitonzo, pamenepo tiyeni mwa chikhulupiriro tiyang'ane kwa Yesu. Mwa mphamuvu ya chiyanjano pakati pa Yesu ndi anthu ake okondedwa, pamapeto pake tidzagonjetsa Satana.

Tiloleni tikudandaulireni choonadi chamuyaya ichi ndi kumudandaulira Mzimu Woyera kuti apereke kudzoza kwatsopano. Tiloledwenso kupatsidwa, mu ng'anjo ya zovuta, mayesero ndi zowawa, kuti tiwone bwino lomwe momwe wolemba Masalmo Davide adaonera chikondi chosatha cha Mulungu, ndi chifukwa cha ichi kuti timudalire. "Ndikweza moyo wanga kwa Inu, Yehova. Mulungu wanga, ndakhulupirira Inu, Ndisachite manyazi; Adani anga asandiseke ine. Inde, onse akuyembekezera Inu sadzachita manyazi; Adzachita manyazi iwo amene achita monyenga kopanda chifukwa. Mundidziwitse mayendedwe anu. Munditsogolere m'choonadi chanu, ndipo mundiphunzitse; Pakuti Inu ndinu Mulungu wa chipulumutso changa; Inu

ndikuyembekezerani tsiku lonseli. Kumbukirani, Yehova , nsoni zanu ndi chifundo chanu; pakuti izi ndi za kale lonse.” (Masalmo 25:1-6).

Kotero kuti ndi chifukwa chake taitanidwa kuti tivale zida zonse za Mulungu. Sitinaitanidwe kuti tiimirire kamodzi kokha, koma kuti tiimirire kawirikawiri pomwe tiri m’moyo uno. Nkhondo idzakhala yaikulu, Satana sadzapereka mpata, koma potenga chishango cha chikhulupuriro “Tidzazimitsa mivi yonse yoyaka moto ya woipayo. Mutengenso chisoti cha chipulumutso, ndi lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu; mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu,” (Aefeso 6:16-18). Chipambano chathu chili chokhazikika, popeza Yesu m’chikondi sanagonjere ku ziwawa za Satana m’malo mwa anthu ake akondedwa. Wolemba ndakatulo akuwonetsera chiyembekezo cha mpingo, ngakhale m’mayesero amene sitikuwamvetsa bwino.

Mwa umodzi ndi Mwanawankhosa,

Ku chilango kumasulidwa,

Oyera mtima anali kuyambira pachiyambi;

Nadzakhala kwa muyaya.

Mu pangano lakalero,

Ana a Mulungu nakhala,

Mwana wa nkhosa wofooketsetsa mkhola la Yesu

Anadalitsidwa mwa Yesu m’menemo

Zomangira zake zosaduka,

Ngakhale zakale za dziko zigwada;

Wamphamvu, woyesedwa, ndi wofooka,

Onse ali amodzi mwa Yesu tsopanno.

Pomwe mafunde ndi mphepo zidzuka,

Kapena machimo pa mtendere alimbana nawo mwamphamvu kawirikawiri,

Chiyembekezo chanu Yesu sichifa;

Chimatayidwa mkati mwa chophimba.

Apa olema onse apume,

Omwe akonda dzina la Mpulumutsi;

Ngakhale ndiwodalitsidwa,

Pangano ili likhalabe chimodzimodzi.

(Kent)

Njira ya Mchipululu.

Tiyeninso tionenso ungwiro wa ndondomeko ya Mulungu. Ambuye Yesu anayesedwa m'chipululu asanayambe utumiki wake wa dziko la pansi. Palibe wa ntchito yemwe amaposa mbuye wake; chotere iwo omwe aitanidwa kutsata Ambuye ayenera kudzera njira imeneyi.

Baibulo limatilangiza za momwe ana a Israeli sanaloledwere kudzera njira ya chindunji kuchokera ku Egypt kupita ku dziko la Kanani. Amayenera kudzera mu chipululu choopsya cha Sinai ndipo patapita zaka zambiri ndi pomwe anaoloka Yordano. Mose analengeza kwa iwowa m'malire a Kanani kuti; "Ndipo mukumbukire njira yonse imene Yehova Mulungu wanu anakuyendetsani m'chipululu zaka izi makumi anai, kuti akuchepetseni, kukuyesani, kudziwa chokhala mumtima mwanu, ngati mudzasunga malamulo ake, kapena iai. Ndipo anakuchepetsani, nakumvetsani njala, nakudyetsani mana, amene simunawadziwa, angakhale makolo anu sanawadziwa; kuti akudziwitseni kuti munthu sakhala moyo ndi mkate wokha, koma munthu akhala wamoyo ndi zonse zakuturuka m'kamwa mwa Yehova." (Duetoronomo 8:2-3).

A Israeli ndi chifanizo cha mpingo wa chikhristu. Akatulutsidwa mu ukapolo wa uchimo, mkhristu ayenera kuyenda monga mlendo ndi wogonera mu dziko ili la uchimo, kudalira pa chakudya cha uzimu cha Ambuye Yesu Khristu, yemwe ndi Mkate wochokera kumwamba wotumizidwa kuchokera kumwamba. Ndipo pa nthawi ya imfa okhulupirira aliyense amatengedwa bwino lomwe ku dziko lolonjezedwa la kumwamba. Koma mdziko ili

timatsimikiza kuti “tiyenera kulowa m’ufumu wa Mulungu ndi zisautso zambiri.’(Machitidwe 14:22).

Timaonanso kuti pamakhala nthawi yapadera ya mayesero ndi mazunzo zomwe zimakhala poyambirira pa maitanidwe ku ntchito ina ili yonse yaikulu mu kutumikira Ambuye. Zinachitika motero ndi Yosefe, yemwe sanalakwe kanthu anagulitsidwa ku ukapolo naikidwanso mundende, asanaitanidwe mwadzidzi kuti afe pamaso pa Faraoh. Chimodzimodzinso pomwe Mose asadawombole aIsraeli, chifuniro cha Ambuye chinali chakuti Mose ayambe wakhala zaka makumi anai m’chipululu cha Midiani asanaitanidwe kuti atsogolere anthu a Ambuye. Koma pomwe nthawi yangwiro inakwana, mapiri onse a zakutsutsana nazo anachotsedwa. Mau amayenda mu mphamvu: “Ndiwe yani, phiri lalikulu iwe? Pamaso pa Zerubabele (yemwe ali chifanizo cha Ambuye Yesu) udzasanduka chidikha;’ (Zakariya 4:7).

Mu zolawa zathu za uzimu, tikhoza kuganiza kuti tikudziwa chifuniro cha Ambuye ndipo timafuna kupita patsogolo ndi kulowa mu ntchito yake; koma njira za Ambuye ndi zangwiro, ndipo tiyenera kuyamba tayesedwa ndi kuchepetsedwa kuti tikhoza kupangidwa kukhala woyenera wogwiritsidwa ntchito ndi Ambuyeyo. Apo timaona bwino lomwe kuti mayankho ku mapemphero amachitika mu chisomo cha Mulungu, osati kuchita mwa kochokera mwa ife.

Zozwizwazo.

Atatha mayesero, Ambuye Yesuyo anapitapita kulalikira Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu. Iye sanali mlaliki wamba, kapena mneneri chabe. Izi zikuchitidwa umboni ndi zozizwa zamphamvu zomwe Iye anachita, zomwe zinaposa kopambana zomwe anachita aneneri a Chipangano Chakale. Zozizwa zomwe Yesu anachita zinasonyeza kuti Iye ndi Mulungu komanso munthu. Zozizwazo zimachitiranso umboni za chikondi chake ndi kukhudzika kwake.

Panali zitsanzo zambiri mu Mau a Mulungu, koma poyamba tiyeni tione chitsanzo cha Lazaro, yemwe alongo ake anatumiza uthenga kwa Yesu, “ nanena Ambuye, onani amene mumkonda adwala.” (Yohane 11:3). Ambuye amadziwa zonse zakuti Lazaro akudwala: “Kudwala kumene sikuli kwa imfa, koma chifukwa cha ulemerero wa Mulungu, kuti Mwana wa Mulungu, kuti Mwana wa Mulungu alemekezedwe nako.” (Yohane 11:4). Komatu Ambuye anachedwa kufika ku Betaniya kufikira pomwe Lazaro anamwalira ndipo patatha masiku anayi ali m’manda.

Pomwe Yesu anafika ku Betaniya anasonyeza kukhudzika kwake kwenikweni, kwa chikondi ndi chisoni kwa Maria ndi Marita. Ambuye Yesu monga Mwana wa munthu analira pa manda. Keneka anaonetsera Umulungu wake, pomwe anaitana Lazaro kumuturutsa kuchokera ku imfa pamaso pa mboni zambiri.

Tiyeni tilingalire pa izi pang’ono. Ambuye nthawi zonse sayankha zopempha zathu zomwe zifunika mayankho a msanga komanso zopemphereredwa mwakhama mu njira zomwe ife

timaganizira. Kodi tinene kuti Ambuye wa kumwamba ndi wa dziko la pansi angathe kulakwitsa ndi kukhala wosasamalira pa zosowa zathu? Yankho lake liyenera kukhala kuti, ai. Izi zimachitika motere chifukwa cha kusowa kwa chikhulupiriro kuti timazunguzika nazo. Komatu kwa moyo wounikiridwa mwa uzimu, chikhulupiriro chimagwira za malonjezano ndiponso kukhulupirira kuti njira ndi nthawi za Mulungu ndi za ngwiro. "Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwachitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wake.' (Aroma 8:28). Chifundo chotani ichi kuti Ambuye amakhululukira machimo athu a kusakhulupirira ndi kutithangatira mu njira zomwe sitimaziyembekezera m'pang'ono pomwe! Mwa machitachita a Mulungu Mzimu Woyera, timapatsidwa chikhulupiriro kuti tikhulupirire. Pamanepo timatsimikiza kuti, timapatsidwa chikhulupiriro kuti Iye amakwaniritsa zosowa zathu zoona, pozionetsera izi mu njira yomwe imapereka ulemerero ndi matamando kwa Iye mwini. "Mulungu ndiye wangwiro m'njira zake, Mau a Yehova ngoyengeka; Ndiye chikopa cha onse okhulupirira Iye" (Masalmo 18:30).

Muthange mwafuna Ufumu wa Mulungu.

Zozizwa zina za machiritso zimationetsera chisamaliro chake mwa chikondi, chomwecho monga mwa Umulungu wake. Komabe, nkhani ya munthu wodwala manjenje imakhazikitsa mfundo yofunika ya maziko, kuti tifune poyamba "Ufumu wa Kumwamba ndi chilungamo chake. (Mateyu 6:33). Tiyeni tsopano tilingalire izi mwa chikhulupiriro. "Ndipo onani, anthu alikunyamulira pakama munthu wamanjenje; nafunafuna kulowa naye, ndi kumuika pamaso pa Iye. Ndipo posapeza polowa naye, chifukwa cha unyinji wa anthu, anakwera pamwamba pa chindwi, namtsitsira iye poboola pa chindwi ndi kama wake, namfikitsa pakati pomwe pamaso pa Yesu. Ndipo Iye, pakuona chikhulupiriro chawo, anati, Munthu iwe, machimo ako akhululukidwa." (Luka 5:18-20). Pomwe aFarisi amamuzenga Yesu mlandu wolankhula monyoza Mulungu ndi kulengezanso chikhulukukiro kwa ochimwa, zomwe ndi Mulungu yekha yemwe angachite, Ambuye Yesu anatsimikiza za Umulungu Wake ndi ulamuliro wakukhululukira machimo onse. "Koma kuti mudziwe kuti Mwana wa munthu ali nayo mphammvu pa dziko lapansi yakukhululukira machimo anati Iye kwa wamanjenjeyo, Ndinena kwa iwe, Tauka nusenze kama wako numuke kunyumba kwako. (Luka 5:24).

Kotero kuti, timaona ntchito yaikulu kusiyana ndi kungochiritsa kwa thupi, yomwe ili kuchiritsa kwa moyo kuchokera ku matenda akupha a chimo. Ichi ndi chomwe chidabweretsa Yesu kuti adzafe pa mtanda. Pamene Ambuye ali wachisomo kuti ayankhe pemphero la chikhulupiriro la kuchiritsa kwa thupi ndi kukwaniritsa kwa zosowa za dziko la pansi, tiyenera kusamala pongoyang'ana za zozizwa za ku zooneka kunja kuti tingangosangalaritsa moyo kapena zilakolako zonyansa za moyo uno. (Yakobo 4:3).

AFarisi anaona zozizwa zambiri pa dzanja lake la Yesu, koma anamugwira Iye. Ena anadyetsedwa mozizwitsa ndi mikate ndi nsomba, koma ankafuna zinthu za umunthu. Yesu

analankhula ndi iwo; “nati Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Mundifuna Ine, si chifukwa munaona zizindikiro, koma chifukwa munadya mkate, nimukhuta. Gwirani ntchito si chifukwa cha chakudya chimene chitayika koma cha chakudya chimene chitsalira ku moyo wosatha chimene Mwana wa munthu adzakupatsani inu; pakuti ameneyo Atate, ndiye Mulungu, adamlembera chizindikro.” (Yohane 6:26-27). Chimodzimodzinso, ana a Israeli anadyetsedwa manna mozizwitsa m’chipululu ndiponso anaona zitsimikizo za mphamvu zochitika ndi dzanja la Mose. “Koma mitembo yawo inagwa m’chipululu” ndipo sakadalowa mu dziko la malonjezano chifukwa cha kusakhulupirira. (Ahebri 3).

Tiyenera kuti tisamale ku chinyengo cha Herode “Ndipo Herode, pamene anaona Yesu anakondwa ndithu; pakuti anayamba kale kufuna kumpenya Iye, chifukwa anamva za Iye; nayembekeza kuona chizindikiro china chochitidwa ndi Iye.” (Luka 23:8). Koma pomwe Herode anaona Muomboli wonzunzidwa mwakachetechete, anamva kutsutsika nanena, “anampeputsa Iye” (Luka 23:11). Komabe, kwa mtima wokhulupirira ntchito zamphamvu za Mulungu m’mitima ndi m’mipingo yathu ndi chitsimikizo cha ubwino wa Ambuye wamuyaya. Kotero kuti, tiyenera kufunafuna mwa chikhulupuriro ntchito zochitika mkati mwathu za Mzimu. Tiyeni tikhumbe moona mtima zipatso za moyo wa kubadwanso kwatsapano mu miyoyo yathu. Mulungu amayang’ana ndi mtengo wapatali pemphero la wochimwa yemwe mwaumphawi akhuthula mtima wake mseri kwa Mulungu. “Koma wamsonkhoyo alikuima patali sanafuna kungakhale kukweza maso kumwamba, komatu anadziguguda pachifuwa pake nanena, Mulungu, mundichitire chifundo, ine wochimwa.” (Luka 18:13). Koma Yesu ananena kuti ndi wamsonkho uyu yemwe anatsikira kunyumba kwake woyesedwa wolungama wosati m,Farisi wodzikweza uja. Ambuye ndi wachifundo chakuti amayankha mapemphero a kulapa kwa wochimwa. Tiyeni tsopano tithange tafuna, “ufumu wa Mulungu ndi chilungamo chake. “ (Mateyu 6:33).

Zozwizwa za Chisomo.

Chifundo chachikulu ndi chimenechi, kuti pomwe Yesu analekanitsidwa ndi uchimo nakhala moyo wangwiro wachiyero, Iye ndi Bwenzi la wochimwa. Kotero kuti a Farisi odzikweza anamuzenga Yesu mulandu wokhala ndi anthu ochimwa. (Mateyu 11:19). Komabe, Yesu Sali bwenzi la ochimwa osalapa komanso odziyenereza. Monga momwe Mtumwi Paulo analembera kuti; “Koma ngatinso Uthenga Wabwino wathu uphimbika, uphimbika mwa iwo akutayika; mwa amene mulungu wa nthawi yino ya pansi pano unachititsa khungu maganizo awo a osakhulupirira, kuti chiwalitsiro cha Uthenga Wabwino wa ulemerero wa Khristu amene ali chithunzithunzi cha Mulungu chisawawalire.” (2 Akorinto 4:3-4). Koma dzina lake ndi Yesu, lomwe litanthauza kuti “Mpulumutsi”; chifukwa adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo,” (Mateyu 1:21). Ambuye Yesu anadza kudzafuna ndi kupulumutsa chotayikacho. Pomwe Mulungu anadziwonetsera yekha mu thupi, koma nthawi ino wadzionetsa mwa ntchito ya

mphamvu ya Mzimu Woyera, yemwe udindo wake wodalitsika ndiwo kuonetsera Ambuye Yesu Khristu wouka kwa akufa ku miyoyo ya anthu.

Mau a Mulungu ochuluka amafotokoza za momwe Ambuye Yesu amakhudzikira ndi anthu ochimwa, komatu sanakondwere ndi ntchito za uchimo. Chikondi cha Yesu chinasintha miyoyo ya anthu mwamphamvu, kuti ochimwa athe kubweretsa ulemu kwa Mulungu poyenda ndi kukhala m'moyo wa chiyero. Nkhani ya Zakeyu (wochimwa wokhometsa msonkho ndiponso wodziwika bwino mu makhalidwe ake oipa) ndi yochititsa chidwi kwambiri. "Ndipo m'mene anadza pamalopo Yesu anakweza maso nati kwa iye, Zakeyu, fulumira, nutsike; pakuti lero ndiyenera kukhala m'nyumba mwako. Ndipo anafulumira, natsika namlandira Iye mokondwera." (Luka 19:5-6). Ndipo Yesu anakhaladi ku nyumba kwake, komanso sipokhapo, komanso kuti Ambuye anakhala mu mtima wa Zakeyu mwa Mzimu Woyera. Ntchito ya chisomo iyi inabereka chipatso nthawi yomweyo mwa kuonetsera chikhulupiriro ndi kulapa kwake. "Ndipo Zakeyu anaimirira nati kwa Ambuye, Taonani, Ambuye, gawo limodzi la zanga zonse zogawika pakati ndipatsa osauka; ndipo ngati ndalanda kanthu kwa munthu monyenga ndimbwezera kanai. Ndipo Yesu anati kwa iye, Lero chipulumutso chagwera nyumba iyi, popeza iyenso ndiye mwana wa Abrahamu. Pakuti Mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa chotayikacho.' (Luka 19:8-10)

Chikondi cha Mulungu Chovumbulutsidwa mwa Uzimu.

Nthawi ino tiyang'anenso mfundo ina yofunikanso, yomwe imagwira ntchito ngati chenjezo. Chikondi cha Mulungu choonetsedwa mu moyo ndi imfa ya Yesu sichinavumbulutsidwe mu zithunzi, zifanizo, zikhumbitso, m'zisudzo kapena kanema, koma ndi chovumbulutsidwa ku mtima ndi kuzindikira kudzera mwa Mzimu Woyera. Ngati Akhristu amakhulupirira moona mtima za umulungu wa Ambuye Yesu Khristu, kuti ndi Mwana wa Mulungu, ndi pomwe zifanizo ndi zithunzithunzi za Yesu zimaonekaoneka? Choonadi ndi choncho! Ambuye akuletsatu zifanizo za Mulungu mu malamulo Khumi (Eksodo 20:4-5). Mose kenaka anafotokoza kwa ana a Israeli, "Potero dzichenjerani nao moyo wanu ndithu; popeza simunapenya mafanizidwe konse tsikuli Yehova ananena ndi inu m"Horebe, ali pakati pa moto; " (Deuteronomo 4:15).

Kwa mtima wa umunthu ndi wathupi, Ambuye Yesu ali "ngati mtengo wanthete, ndi ngati muzu womera m'nthaka youma; Iye alibe maonekedwe, pena kukongola; ndipo pamene timuona palibe kukongola kuti timkhumbe." (Yesaya 53:2). Ngati mpingo ufuna kukopa otsatira popanga zoinetsero zokongola zoimira Yesu, sipadzakhala kuzama kwa uzimu, Kapena mpingo kukhala monga uyenerera. Tiyenera "kuyenda mwa chikhulupiriro osati monga mwa maonekedwe' (2 Akorinto 5:7. Ambuye Yesu analakhula, atamuonetsera Tomasi wosakhulupirirayo, thupi lake lakuukitsidwa kwa akufa, "Odala iwo akukhulupirira, angakhale sanaona." (Yohane 20:29). Kuyang'ana mwa thupi osati mwa chikhulupiriro, sikupindula ai. Mpingo udzapezeka kuti uli ndi "okhulupirira" mwa umunthu, omwe alambira Khristu wonyenga, chifanizo chopanangidwa ndi

munthu chomwe sichili Mwana wa Mulungu wamuyaya. Zokondweretsa za dziko lapansi, m'malo mwa utumiki wa Uthenga Wabwino, ndi womwe ungasunge "wokhulupirira mwa umunthu kuti akhalebe membala ndi kukhazikika mu mpingo.

Mose anakhumba kuti adziwe kupezeka kwa Ambuye ndikuti aone ulemerero wa Mulungu. Komatu zokhumba zake zinali zosiyana ndi za aIsraeli omwe anaukira, omwe adangoona zizindikiro zakunja, pamodzi ndi kukwaniritsa mozizwitsa zosowa za m'matupi mwawo. Ambuye mwa chisomo anayankha Mose mupemphero lake lakuti moyo wake udalitsike; "Ndidzapititsa ukoma wanga wonse pamaso pako, ndipo ndidzatchula dzina la Yehova pamaso pako; ndipo ndidzachitira ufulu amane ndidzamchitira ufulu; ndi kuchitira chifundo amene ndidzamchitira chifundo. Ananenanso, Sungathe kuona khope yanga; pakuti palibe munthu adzandiona Ine ndikukhala ndi moyo. Ndipo Yehova anati, Taona pali Inepo pali malo, ndipo uime pathanthwe." Eksodo 33:19-22). Thanthwe ndi chiyerekezo cha Ambuye Yesu Khristu, yemwe kuchokera mu nthiti mwake munatuluka mwazi ndi madzi, mwazi kuti utetezere, ndi madzi kuti ayeretse. Tifunefune vumbulutso la mphamvu la umulungu la chikondi cha mulungu mu chiyanjano cha uzimu ndi Yesu Mpulumutsi. Ambuye walonjeza; "Pemphani ndipo chidzapatsiswa kwa inu; funani ndipo mudzapeza; gogodani ndipo chidzatsagulidwa kwa inu." (Mateyu 7:7)

Wansembe Wamkulu Wathu.

Tiyenera kuti tsopano timalize mutu uwu ndi udindo wa unsembe wa Yesu "Popeza tsono ana ndiwo a mwazi ndi nyama, Iyenso momwemo adalawa nao maonekedwe omwewo kuti mwa imfa akamuononge iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi; nakamasule iwo onse amene, chifukwa cha kuopa imfa, m'moyo wao wonse adamangidwa ukapolo. Pakuti ndithu salandira angelo, koma alandira mbeu ya Abrahamu. Potero kudamuyenera kukanizidwa ndi abale m'zonse, kuti akadzakhala mkulu wa nsembe wachifundo ndi wokhulupirika m'zinthu za kwa Mulungu, kuti apereke dipo la zoipa za anthu." (Ahebri 2:14-17).

Mwa Yesu timaona kukwaniritsidwa kwa uneneri wa Yesaya, "zoonadi Iye ananyamula zowawa zathu, ndi kusenza zisoni zathu; koma ife tinamuyesa wokhomedwa, wokanthidwa ndi Mulungu, ndi wovutidwa. Koma Iye analasidwa chifukwa cha mphulupulu zathu; chilango chititengera ife mtendere chinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yake ife tachiritsidwa. Tonse tasochera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse." (Yesaya 53:4-6). Uwu ndiye mutu womwe uyenera kukhala waukulu wa mitu yonse yotsatira, momwe tikukhumba kuti tilingalire pa Ambuye Yesu, yemwe anataya moyo wake pa Kalvari chifukwa cha machimo a anthu ake okondedwa.

Yesu anadza pomwe panali ochimwa, komatu Iye anali "woyera mtima, wopanda choipa, wosadetsedwa, wosiyana ndi ochimwa, wakukhala wopitirira miyamba." (Ahebri 7:26). Anayenda moyo wangwiro, nakwaniritsa chilamulo modzichepetsa mkumvera kwa Atate ake a

kumwamba. Monga Mwana wa munthu, Iye “monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wake dipo la anthu ambiri.” (Mateyu 20:28). Njira yomwe anayenda, inamtsogolera Iye ku Getsemane, ndipo keneka anafa monga Mwana wa nkhosa wa Mulungu. Ichi ndi chikondi choposa kumvetsetsa kwa umunthu, koma chinavumbulutsidwa modala ku mtima kudzera mwa Mzimu Woyera pakuyankha mapemphero anthu.

MUTU 3

GETSEMANE

Mau Otsogolera.

Tinamaliza mutu wapitawu polingalira mwachidule zokhudza Ambuye Yesu monga Wansembe Wamkulu woposa. Pokhala nawo mutu uwu m’malingaliro athu, tibwera ku nthawi yomalizira ya moyo wa dziko la pansi wa Yesu. Ngakhale zinatha tsiku limodzi, koma olemba Uthenga Wabwino amakamba za ichi, chifukwa ndi chochitika chofunika pokhudzana ndi chipulumutso chosatha. Ngati sitidziwa chiri chonse cha kukhudzika kwa Ambuye Yesu amadutsa mu Getsemane, mu nyumba yoweruzira milandu ndi kumalizira pa mtanda wa Kalvari, sitingakhale ndi chiyembekezo choona cha kumwamba. Komanso kungokhala nacho chidziwitso cha m’maganizo athu cha zomwe Yesu anatichitira sizingatipangitse kuti tipulumutsidwe. Kukhudzika ndi miyoyo yathu kwa Ambuye kwa Ambuye Yesu siziyenera kungoyang’anidwa wamba, monga momwe ambiri anachitira pa tsiku la kupachikidwa kwa Ambuye mu Yerusalemu, koma tisowekera kulandira kumvetsetsa mwa uzimu kuchokera kwa Mulungu. Tiyeni tidzifunse tokha funso lofunika ili: kodi tiwonetsedwa mwa chikhulupiriro kuti Yesu, anazunzidwa m’malo mwathu, iye wolungama m’malo wosalungama? Kodi taonetsedwa kuti ndi chifukwa cha machimo athu kuti Yesu anazunzidwa mosatha kuneneka ndiponso kukhetsa mwazi Wake wa mtengo wapatali? Tiyenera kupemphera moona mtima kwa Ambuye, kuti tikhoza kulandira mayankho a mtendere omwe angadalitse miyoyo yathu.

Pa nthawi ino tiyenera kupitirira kulingalira kuti Yesu sanali wansembe wamkulu monga omwe analipo pa nthawi ya chilamulo cha Mose, omwe anapereka mwazi wa nyama chifukwa cha machimo awo komanso a anthu; koma Yesu anadzipereka yekha monga Mwana wa nkhosa Woyera wa Mulungu. (Ahebri 7:27). Pakuti Mulungu Atate anamyesera Yesu, Mwana wa Mulungu wosandulika thupi, “Ameneyo sanadziwa uchimo anamyesera chimo m’malo mwathu; kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu kwa Iye.” (2 Akorinto 5:21). Kotero ndi momwe chiunikira chikondi cha Mulungu mu ulemerero wa chikondicho.

Yesu apempherera Anthu Ake.

Atatha kudya mgonero wotsiriza ndi ophunzira Ake, Ambuye anati: “Ndithu ndinena nanu, Sindidzamwanso chipatso cha mpesa, kufikira tsiku lijalo, limene ndidzamwa icho chatsopano mu Ufumu wa Mulungu. Ndipo atayimba nyimbo, anaturuka, namuka pa phiri la Azitona. Ndipo Yesu ananena nao, Mudzakhumudwa nonsenu; pakuti kwalembedwa, Ndidzakantha mbusa, ndi nkhosa zidzamwazika. Komatu nditadzauka ndidzatsogolera inu mu Galileya.’ (Marko 14:25-28).

Kufikira pomwe Mzimu wodalitsika anaperekedwa, ophunzira sanamvetsetse zinthu izi. Koma tiyenera tilingalire, mothandizidwa ndi Mzimu Woyera, pa za mphamvu ya umulungu yomwe ili mu pemphero la ulemerero la Ambuye Yesu lomwe limapambana kusakhulupirira konse. Timawerenga za Ambuye Yesu asanalowe mu Getsemane kuti, “Zinthu izi analankhula Yesu; ndipo m’mene anakweza maso ake Kumwamba, anati, Atate, yafika nthawi; lemekezani Mwana wanu, kuti Mwana wanu akulemekezeni Inu; monga mwampatsa Iye ulamuliro pa thupi liri lonse, kuti onse amene mwampatsa Iye, awapatse iwo moyo wosatha. Koma moyo wosatha ndi uwu, kuti akadziwe Inu Mulungu woona yekha, ndi Yesu Khristu amene munamtuma.” (Yohane 17:1-3). Momwemo ndi momwe Yesu anapempherera mpingo Wake wokondedwa mwakuti tsiku lotsatira lake ataya moyo Wake pa Kalvari. Pochita ichi Ambuye Yesu anadzikhuthula Yekha monga Wansembe Wamkulu wa anthu Ake: “Ndipo chifukwa cha iwo Ine ndadzipatula ndekha kuti iwonso akhale opatulidwa m’choonadi.’ (Yohane 17:19).

Pemphero la Ambuye Yesu lopempherera anthu Ake okondedwa limaonetseratu za chikondi cha Mulungu. Chikondi chodalitsika pakati Utatu wawo wa Umulungu, pakati pa Mulungu Atate ndi Mulungu Mwana zimaonetsedwa. Ambuye Yesu anapemphera kuti chimodzimodzinso izi ziperekedwe pakati pa zotengera zosankhika za chifundo ndi Mulungu mu Utatu wake. Pemphero lotere lochokera kwa Yesu, Mwana wamuyaya wa Mulungu, yemwe mwa Iye Atate akondweretsedwa, limamveka ndiponso kuyankhidwa. “Ndipo ulemerero umene mwandipatsa Ine ndapatsa iwo: kuti akhale amodzi monga ife tiri mmodzi; Ine mwa iwo ndi Inu mwa Ine, kuti akhale angwiro mwa mmodzi; kuti dziko la pansi lizindikire kuti Inu munandituma Ine, nimuwakonda iwo, monga momwe munakonda Ine. Atate, amene mwandipatsa Ine, ndafuna kuti kumene ndiri Ine, iwonso akhale pamodzi ndi Ine; kuti ayang’anire ulemerero wanga, umene mwandipatsa Ine; pakuti munandikonda Ine lisanakhazikike dziko lapansi. Atate wolungama, dziko lapansi silinadziwa Inu, koma Ine ndinadziwa Inu; ndipo iwo anazindikira kuti munandituma Ine; ndipo ndinazindikiritsa iwo dzina lanu, ndipo ndidzalizindikiritsa; kuti chikondi chimene munandikonda nacho chikhale mwa iwo, ndi Ine mwa iwo.” (Yohane 17:22-26).

Atatha kulankhula mau awa Yesu anadutsa mtsinje wa Kidroni kupita ku phiri la Azitona. Mwa chikhulupiriro tione kulowa kwa Ambuye Yesu mu Getsemane. Zoonadi mtumwi Yohane,

yemwe “Yesu anamkonda” analemba za Yesu kuti “m’mene anakonda ake a Iye yekha a m’dziko la pansi, anawakonda kufikira chimaliriziro.” (Yohane 13:1).

Yesu asenza Machimo a Anthu Ake.

Ambuye atalowa mu Getsemane, Mau a Mulungu amanena kuti katundu woipa wa machimo a osankhika anaikidwa pa Muomboli. “Ndipo iwo anadza ku malo dzina lake Getsemane: ndipo ananena kwa ophunzira ake, Bakhalani pano, kufikira ndikapempherera, Ndipo anatenga pamodzi ndi Iye Petro, ndi Yakobo, ndi Yohane, nayamba kudabwa kwambiri, ndi kusauka mtima ndithu. Ndipo ananena nao, Moyo wanga uli wa chisoni chambiri, kufikira imfa. Bakhalani pano, nimudikire.” (Marko 14:32-34). Poyamba tilingalire kuti dzina limeneli “Getsemane” likuonetsa bwino lomwe pomwe limasulidwa kuti, “Chofinyira Mpesa”. Wolemba ndakatulo akulemba kuti.

> “M’mundamo Yesu anadza,
>
> Getsemane dzina la tanthauzo lake,
>
> Lomwe litsimikiza za chofinyira mpesa.
>
> Ah! Pamenepo kupsyinjika kwa mtima wake kunayamba,
>
> Mafuta a chipulumutso nafinyidwapo,
>
> Kubweretsa thanzi ndi moyo ndi chimwemwe kwa ife!”
>
> (Hallgrimur Petursson, trans A Gook).

Kukoma kotani pomwe tilingalira za madalitso omwe amatuluka mu mkukhudzika kwa Ambuye, Pomwe kwavumbulutsidwa kudzera kwa Mzimu Woyera. Pansi pa chilamulo cha Mose ana a Israeli amalamulidwa kuti abweretse kwa Ambuye kuti pakhale kuwala mu Chihema, “mafuta a azitona oyera apera akuunikira, kuti aziwalitsa nyali nthawi zonse.” Levitiko 24:2). Izi sizilankhula za chifanizo cha kukhala opanda banga ndi kusadetsedwa kwa chiyero kwa Ambuye Yesu kokha, komanso mafuta oyenda kutsika kuchokera mu kufinya kwa mpesa zimasonyeza za dalitso loperekedwa kudzera mwa Mzimu Woyera ku mpingo wa Mulungu potengera kuzunzidwa kotitetezera kwa Yesu. Dzina ili lakuti Yesu “Khristu” litanthauza “wodzozedwa”, yemwe anadzozedwa kuti akhale mfumu ndi Wansembe Wamkulu wa anthu Ake okondedwa. Kudzera mu mphamvu ya mkudzoza kwa Ambuye ndi chitetezero cha mtengo wapatali, aliyense wa anthu Ake okondedwa amalandira m’miyoyo yawo, “kudzoza kochokera kwa Woyerayo, ndipo mudziwa zonse.” (1 Yohane 2:20).

Pamene Chihema chimawalitsika ndi mafuta a azitona, motero Ambuye amakwaniritsa fanizo ili. Yesu ananena, “Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; iye wonditsata Ine sadzayenda

mumdima, koma adzakhala nako kuunika kwa moyo.” (Yohane 8:12). Kuwala kochepa kwa kandulo mu Chihema cha dziko lapansi, m’malo mwake pafika kuwala kwa umulungu ndi ulemerero. Mtumwi Yohane anaona ichi mu masomphenya ake a Yerusalemu watsopano; “Ndipo pamzinda sipafunika dzuwa, kapena mwezi wakuuwalira; pakuti ulemerero wa Mulungu uunikira umenewu ndipo nyali yake ndiye Mwana wa Nkhosa.” (Chivumbulutso 21:23).

Kumva Ululu kwa Khristu m’Mundamo.

Machimo a osankhika omwe tsopano akuikidwa pa Ambuye Yesu mu umunthu wake, Ambuye anaweramitsidwa pansi pa uchimo waukuluwo, machimo a chotengera chonse cha chifundo kuyambira pa Adamu kufikira pa kubweranso kwachiwiri kwa Ambuye. Ambuye anapemphera, “Atate mukafuna Inu, chotsani chikho ichi pa Ine; koma si kufuna kwanga ai, komatu kufuna kwanu kuchitike. Ndipo anamuonekera Iye mngelo wa kumwamba namlimbikitsa Iye. Ndipo pokhala Iye m’chipsyinjo mtima anapemphera kolimba koposa ndithu: ndi thukuta lake linakhla ngati madontho akuru a mwazi alinkugwa pansi.” (Luka 22:42-44).

Umunthu wangwiro ndi wopanda chimo wa Ambuye unafinyika ndi machimo oopsya a anthu Ake omwe anaikidwa pa Iye; koma analimbikitsidwa kudzera mu umodzi wa ulemerero ndi umulungu wake. Ambuye Yesu yekhayo, yemwe anali Mulungu ndi munthu, umulungu ndi umunthu mwa Munthu m’modzi wa ulemerero, akadakhoza kutsutsa ndi kusenza katundu woipa kwambiriyu. Mtumwi Paulo akulimbikitsa okhulupirira aliyense kuti ayang’ane “kwa Yesu, ameneyo chifukwa cha chimwemwe choikidwacho pamaso pake, anapirira mtanda, nayoza manyazi, nakhala pa dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Mulungu.’ (Ahebri 12:2). Misonzi, kuzunzika ndi ululu wa Ambuye Yesu, pomwe anasenza machimo a anthu Ake, zabweretsa ku mpingo wake chimwemwe ndi mtendere wosatheka kuneneka. Polumikizidwa kwa Ambuye Yesu, mpingo wake wapangidwa kukhala wolandira paradaizo.

Tikuonanso kuchokera ku ndakatulo ya munthu wa ku Iceland yemwe ndi Hallgri’mur Pe’tursson, yemwe akulingalira mopindulitsa pa zoonadi izi.

Ndi katundu womvetsa chisoni anaweramitsidwa.

Pansi pa thambo loopsya la chiweruzo.

Umunthu wake, unazunzidwa mopweteka,

Pothawira sipanapezeke, mtendere panalibe, mpumulo panalibe.

“Ngakhale ku imfa Moyo Wanga,” Ananena,

“Waswanyidwa ndi kulemetsedwa ndi chisoni choopsya.”

Anayenda kuchoka pa iwo ka mtunda pang'ono,

Keneka, akuyenda mofooka, anagwa pa nkhope yake.

Ululu wake monga funde la nyanja ya mchere.

Kudutsa pa Iye, kuti apulumutse moyo wanga.

Palibe lilime linganene, kapena malingaliro kupeza mtengo wake.

Muyeso wa kuzunzika kwa Moyo wake.

Chikumbumtima changa chindiguguda ndi lingaliro.

Kuti apa ndi pomwe ufulu wanga unagulidwa.

'Ndi uchimo wanga womwe unazunza inu'.

Kuzunzika konseku kunali kwa ine.

Oh, momwe ndimvera chisoni ndi zichita zanga.

Zidzaze ndi ndulu chikho cha inu!

Chimo langa, zioneka kuti, linali ndi kulemera kwakukulu.

Kuposa china chiri chonse chomwe Ambuye anachilenga;

Iye, kudzera mwa Mau a mphamvu yake.

Anamasula chilengedwe kufikira lero.

Komatu, kusenza machimo anga onse m'chitonzo.

Anamizika m'khope Yake mu chisoni.

Kulimba mtima kotani, chimwemwe chotani,

Zoonadi izi zigwiritsidwa ntchito koposa kupereka –

Dipo loperekedwa kwa ine lomwe linayenera,

Koposa chuma cha kumwamba ndi dziko!

Kuzama kwa chisoni chake, zowawa Anasenza,

Zinapereka ufulu kwa moyo wanga kwa nthawi za nthawi.

{Hallgri'mur Pe'tursson. trans. A Gook).

Komatu, momvetsa chisoni, mkati mwa ululu wa Ambuye, timawerenga za kulephera kwa ophunzira Ake onse, chifukwa sadathe kukhala maso ndi kupemphera. Izi ndi zoona kwa ophunzira ndi ali yense mwa chibadwidwe; machimo athu ali monga kapezi. Koma taonani zipatso za Mzimu Woyera zomwe zimatsikira ku mpingo chifukwa cha ululu Wake ndi kupachikidwa pa mtanda! Mu mphamvu yathu sitingathe kuchita chiri chonse, koma pomwe mwa mphamvu zichitika kudzera mwa Mzimu Woyera ndi pomwe tikhoza kuchita zonse mwa Ambuye Yesu. (Afilipi 4:13).

Ameneyo Ndine.

Mwaliwiro loposa potsatira ululu womwe anamva m'mundamo, Yudasi Iskarioti ndi "gulu la asirikari ndi anyamata, kwa ansembe akulu ndi a Farisi, anadza komweko ndi nyali ndi zida. (Yohane 18:3). Kunali kumangidwa kwa Yesu komwe umulungu Wake monga Mulungu Mwana unawala mobisika. "Yesu , podziwa zonse zirinkudza pa Iye, anaturuka, nati kwa iwo, Mufuna yani? Anayankha Iye, Yesu Mnazarayo. Yesu anenana nao, Ndine. Koma Yudasi yemwe, wompereka Iye, anaima nao pamodzi. Ndipo m'mene anati kwa iwo, Ndine, anabwerera m'mbuyo, nagwa pansi. "(Yohane 18:4-6). Ngakhale mitima ya Yudasi ndi gulu la asirikari omwe anachokera kwa ansembe akulu inaumitsidwa kwambiri monga mwakuti asazindikire dalitso liri lonse mu mau awo, "Ameneyo Ndine", wolemba ndakatulo akuonetsera chitonthozo chomwe mwau awa akubweretsa kwa anthu osankhidwa ndi akondedwa a Mulungu.

Ambuye wathu anayankha, "Ameneyo Ndine!"

(Yudasi anali pafupi, kuti aone mphamvu yake).

Ndi pa kumvera pa kulankhula kwake mwamphamvu.

Onse pansi anagwa chafufumimba.

Chinthu chomwe chinawachititsa mantha,

Kwa moyo wanga ndi chondisangalatsa chachikulu.

Ndi kupukuta misonzi yomwe ikutsika.

Ngati thambo la kuda la chimo libwera msanga,

Ndi kundibisa ku nkhope ya Atate wanga,

Ah! Pamenepo ndimva liu la Mpulumutsi wanga,

Lomwe limaitana moyo wanga wofooka kuti usangalale.

“Taonani, wochimwa wosauka, Ameneyo ndine,

Yemwe anakhetsa mwazi pa mtanda,

Dipo ilo linali la onga iwe!”

Pomwe mopweteka anaponderezedwa ndi makhwekhwe a Satana,

Mwa kuluma kwa chikumbumtima ndi zolabadira za mkati,

‘Ndi pomwe ndimadziwa kuti ali pafupi,

‘Ndi pomwe liu la Mpulumutsi wanga ndimva,

Chifukwa “Ameneyo Ndine!” Ndidzamva akunena.

”Yemwe machimo anga onse anasenza’.

Mau Ake a mtengo wapatali mantha anga achoka.

Ndipo pomwe ndiri mu umphawi ndi ululu.

Ndimakhumba kuti mkufooka nditapumula,

Ndimamva Inu mukunena “Ameneyo Ndine”,

Amene chisomo chake chikwanira ngakhale kwa iwe.

Chuma changa, chidikirira iwe, mosungiramo Mwanga,

Pomwe mayesero onse a dziko lapansi atha,

Inde zisangalalo kumeneko ku nthawi za nthawi!”.

Ndipo pomwe ndiyitanidwa kuti ndinyamuke,

Kuti ndikakhale ndi Khristu, ndidziwa mtima wanga,

Usamvanso mau omwe ndiwakonda,

Kumveka pamwamba pa liu lina liri lonse:

“Mwana wanga, taona, chifukwa Ameneyo Ndine,

Yemwe wakukonzera malo;

Komwe wantchito Wanganso adakhala.”

(Hallgri’mur Pe’tersson, trans. A Gook).

Patatha apo Yesu analankhula mau a mtengo wapatali. Ngakhale analankhulidwa mwachindunji kwa nthawi iyo kwa gulu la asirikari lomwe lidabwera kudzamumanga, pali chitsimikizo chozama cha uzimu kwa okondedwa ake a Mulungu omwe Yesu amayenera kuwaombola,“ Yesu anayankha, Ndati, Ndine; chifukwa chake ngati mufuna Ine, lekani awa amuke; kuti akwaniridwe mau amene ati, Mwa iwo amene mwandipatsa Ine, sindinataya m’modzi.” (Yohane 18:8-9). Izi zikunena za Yesu kuima m’malo mwa anthu ake. Ndi munthu ameneyu Khristu Yesu, osati anthu ake opanda pake, yemwe amasenza mkwiyo wa chilungamo cha umulungu woperekedwa chifukwa cha zochimwa zawo. Chikondi cha umulungu ichi ku mbali ya Ambuye chimawamasula iwo ndiponso kuwakonzekeretsa ulemerero. Kukhumba kwathu ndi kwakuti Mzimu Woyera ativumbulutsire ambiri a madalitso a mtengo wapatali m’miyoyo yathu! “Ndipo Mzimu ndi mkwatibwi ananena, Idzani. Ndipo wakumva anene Idzani. Ndipo wakumva ludzu adze; iye wofuna, atenge madzi a moyo kwaulere. Iye wakuchitira umboni izi, anena, Indetu; ndidza msanga, Amen; idzani Ambuye Yesu.” (Chivumbulutso 22:17, 20).

Yesu pa bwalo la Oweruza.

Kuchokera ku Getsemane Yesu anamutengera kwa wansembe wamkulu nakhazikitsidwa pamaso pa bwalo la Oweruza. Pomwe anamunamizira milandu yambiri Iye, timawerenga kuti Yesu, “Koma anakhala chete, osayankhula kanthu. Mkulu wa ansembe anamfusanso, nanena naye, Kodi Iwe ndiwe Khristu Mwana wake wa Wolemekezeka? Ndipo Yesu anati, Ndine amene; ndipo mudzaona Mwana wa munthu alikukhala ku dzanja lamanja la mphamvu, ndi kudza ndi mitambo ya kumwamba. Ndipo mkulu wa ansembe anang’amba maraya ake, nanena, Tifuniranjinso mboni zina? Mwamva mwano wake; muyesa bwanji? Ndipo onse anamtsutsa Iye kuti ayenera kufa. Ndipo ena anayamba kumthira malovu Iye, ndi kuphimba nkhope yake, ndi kumbwanyula, ndi kunenanaye, Lota; ndipo anyamata anampanda Iye khofu.”(Marko 14:61-65).

Malangizo ndi a kuti tiyenera kuyang'ana pa udani womwe unaonetseredwa kwa Yesu kuchokera kwa iwo omwe anali pa ulamuliro. Ngakhale pa chiyambi cha moyo wa Yesu, mfumu Herode anafuna kumupha Iye yemwe anabadwa, mfumu yoona ya Israeli. Ngakhale kuti ufumu wa Yesu siunali wa dziko la pansi lino, koma wa ufumu wa ulemerero wakumwamba, mfumu ya dziko Herode anadana naye Ambuye wa Ulemerero, chifukwa Herode amaopa kuti Yesu alowa m'malo mwake. Momwemonso Kayafa, wansembe wamkulu wa dziko la pansi, anamugwira Yesu, yemwe ndi Wansembe Wamkulu wamuyaya woonadi.

Kayafa sanazindikire kuti Yesu amamkwaniritsa mafanizo ndi zithunzithunzi za chilamulo cha Mose, monga momwe maso ake anali akhungu ku zinthu zauzimu. Mau a Yohane Mbatizi anali osiyana, pomwe anamuona Yesu akubwera kwa Iye. "Onani Mwana wa Nkhosa wa Mulungu amene achotsa chimo lake la dziko la pansi!" (Yoane 1:29). Ananenanso kuti, "Iyeyo ayenera kukula koma ine ndichepe." (Yohane 3:30). Yohane Mbatizi anali mwana weniweni wauzimu wa Abrahamu, yemwe anakondwera kuona mwachikhulupiriro kubwera kwa Ambuye Yesu. (Yohane 8:56).

Poyanga'ana ndi diso la ku thupi tikhoza kuona kuti wansembe wamkulu Kayafa anapereka nsembe zolandirika mogwirizana ndi ndondomeko yonse ya chilamulo cha Mose: koma Mulungu anayanera kukhala ndi chikondi, choonadi ndi chifundo osati chinyengo (Yesaya 1:10-15, Malaki 2). Mosiyaniratu, Ambuye Yesu anadzipereka Iye yekha nsembe yolandirika mu zinthu zonse, wodzala ndi chisomo, choonadi ndi chikondi. Kotero kuti zakhala ziri motero kuti iwo, omwe ali ndi maonekedwe a umulungu namadzitukumula mokhudzana ndi chipembedzo chawo, adzazunza anthu a Ambuye amwe amachitira umboni mokhulupirika ku choonadi mwa Khristu Yesu. "Ndipo adzada inu anthu onse chifukwa cha dzina langa; koma iye wakupirira kufikira chimariziro, iyeyu adzapulumutsidwa. Wophunzira saposa mphunzitsi wake, kapena kapolo saposa mbuye wake. (Mateyu 10:22,24).

Kukana Yesu kwa Petro ndi Chikondi champhamvu cha Ambuye.

Pamene zochitika zoopsya izi zimachitika, Petro amatsatira Ambuye Patali nalowa m'nyumba ya mfumu. Apa ndi pomwe Petro anakumanizana ndi anthu omwe amaotha moto, pamene anakumana ndi chotsutsana nacho. "Ndipo popita kamphindi, anamuona wina, nati Iwenso ndi m'modzi wa awo. Koma Petro, anati, Munthu iwe, sindine. Ndipo patapita ngati ora limodzi wina ananenetsa, kuti, Zoonadi munthu uyunso anali naye, pakuti ndiye mGalileya. Koma Petro anati, Munthu iwe, sindidziwa chimene uchinena. Ndipo pomwepo, iye ali chilankhulire, tambala analira. Ndipo Ambuye anapotoloka, nayang'ana Petro. Ndipo Petro anakumbukira mau a Ambuye, kuti anati kwa iye, Asanalire tambala lero lino, udzandikana Ine katatu. Ndipo anaturuka, nalira misozi ndi kuwawa mtima." (Luka 22:56-62).

Taonani, momwe kuyang'ana kwa nkhope yokwapulidwa ya Ambuye Yesu kunabweretsera kusweka mtima kwa Petro! Polankhula za Ambuye mu uneneri, Yesaya analemba kuti; "Ndinapereka msana wanga kwa omenya, ndi masaya anga kwa iwo amene anakudzula tsitsi langa; sindinabisira nkhope yanga manyazi ndikulavulidwa." (Yesaya 50:6). Chosowa chomwe tiri nachotu ndi kuyang'ana Ambuye Yesu mwa chikhulupiriro, kuti tipatsidwe "kuunika kudzawala kuturuka mumdima, ndiye amene anawala m'mitima yathu kutipatsa chiwalitso cha ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Khristu.' (2 Akorinto 4:6). Mu chipangano chakale cha chilamulo, palibe m;modzi yemwe akadaona nkhope ya Mulungu ndi kukhala ndi moyo. Koma mu Uthenga Wabwino "ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyerera monga mwa kalilore ulemerero wa Ambuye, tisandulika m'chithunzithunzi chomwechi kuchokera kwa Ambuye Mzimu. (2 Akorinto 3:18).

Kuyang'ana kwa chikondi kuchokera kwa Yesu, yemwe anavutika m'malo mwa anthu Ake, ndi kosowekera koposa ku miyoyo yathu. Ichi chimapereka kulapa komwe palibe chilimbikitso ngakhale chilingaliro cha umunthu mwa iwo okha sizingapereke. Ambuye Yesu atafa, Petro anatha kuchitira umboni kuti Mulungu "ameneyo Mulungu anamkweza ndi dzanja lake la manja, akhale Mtsogoleri ndi Mpulumutsi, kuti apatse kwa Israeli kulapa, ndi chikhululukiro cha machimo. Ndipo ife ndife mboni za zinthu izi; Mzimu Woyeranso, amene Mulungu anapatsa kwa iwo akumvera Iye." (Machitidwe 5:31-32). Tiyeni potero tipemphere kuti Mzimu Woyera ativumbulutsire kenanso za kuyang'ana kotsitsimutsa kwa Mpulumutsi ndi Mkhalapakati wokonda, pomwe ife tiyang'ana mwa chikhulupiriro, yemwe nkhope yake yomenyedwa, imabweretsa kulapa kosakanizika ndi chikondi, chimwemwe ndi mtendere pakukhulupirira.

Yesu Anakhala chete pamaso pa Pilato.

Pamenepo Yesu anatsogozedwa womangidwa kwa Pilato. "Ndipo pakudza mmamawa, ansembe akuru ndi akuru a anthu onse anakhala upo wakumchitira Yesu, kuti amuphe; ndipo anamumanga Iye, namuka naye nampereka Iye kwa Pilato kazembeyo. Ndipo Yesu anaimirira pamaso pa kazembe, ndipo kazembeyo anamfunsa Iye kuti, Kodi Iwe ndiwe mfumu ya Ayuda? Ndipo Yesu anati kwa iye, Mwatero. Ndipo pakumnenera Iye sanayankha kanthu." (Mateyu 27:1-2,11-12).

Chifukwa chake ndi chiyani chakuti Ambuye wa ulemerero, Mulungu Mwana anakhalira chete? Uku kunali kukwaniritsa uneneri wa Yesaya wa zaka mazana ambiri isanafike nthawi iyi. "Tonse tasochera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse. Iye anatsenderezedwa koma anadzichepetsa yekha osatsegula pakamwa pake; ngati nkhosa yotsogozedwa kukaphedwa, ndi ngati mwana wa nkhosa amene ali du pamaso pa omsenga, motero sanatsegula pakamwa pake." (Yesaya 53:6-7). Kuvutika kwa kachete kwa Ambuye kunali kwa kuti aombole anthu ake okondedwa, omwe asokera monga nkhosa kuchoka pa njira ya chilungamo. Ambuye Yesu ndiye Mbusa wa anthu Ake ndipo

amawasamalira ndi chikondi chanthete. Amabwera pomwe anthu ali, anafika ngakhale ku nyumba yoweruzira milandu, naimirira m'malo mwa anthu ake, atasenza machimo awo, kulandira chilango chomwe chinayenera kugwera anthu ake.

Tiyeni tipemphere tsopano kuti Mulungu atipatse kuyang'ana bwino lomwe kwa Mpulumutsi wokonda, yemwe analankhula pa nthawi ya utumiki wake wapansi pano; "Ine ndine Mbusa Wabwino; mbusa wabwino ataya moyo wake chifukwa cha nkhosa." (Yohane 10:11). Pomwe Mzimu Woyera atipangitsa ife kuyang'ana kwa Yesu mwa chikhulupiriro, timanena monga Yohane Mbatizi, "Taonani Mwana wa Nkhosa wa Mulungu amene achotsa chimo lake la dziko la pansi." (Yohane 1:29). Mu umodzi ndi Yesu machimo athu sangapezekenso, chifukwa amatsukidwa ndi mwazi Wake wokhetsedwa pamodzi ndi nsembe yetetezera.

MUTU 4.

CHIKONDI CHACHIKULU KUPOSA ICHI PALIBE MUNTHU ALI NACHO.

Mphamvu ya Mzimu.

Mu tsiku limene chikondi cha anthu ambiri chazilala, ndi pomwe tisowa kuyang'ana kwa uzimu kwa chikondi cha Khristu kuti chitipatsenso moyo ife. Mu kuzunzika kwake kwa Muomboli, m'malo mwa anthu ake osankhika ndi momwe chikondi chake chiwalitsidwa kwambiri. "Palibe munthu ali nacho chikondi choposa ichi, chakuti munthu ataya moyo wake chifukwa cha abwenzi ake." (Yohane 15:13). Pofunafuna kulemba pa choonadi chozama ichi, wolemba akuzindikira bwino za kufunikira kwa mphamvu ya Mzimu Woyera yemwe ndi Nkhosweyo. Monga Ambuye Yesu ananena za Mzimu kwa akuphunzira ake "Iyeyo adzalemekeza Ine; chifukwa adzatenga za mwa Ine, nadzalalikira kwa inu." (Yohane 16:14). Popanda kukhala dalitso ili mau olembedwa adzangokhala zolembedwa wamba. Komabe, ngati Mzimu angatipangitse kuti tidziwe Yesu mwa chikoka chake chonse kwa wowerenga, pamenepo padzakhala chimwemwe ndi mtendere pakukhulupirira. Pamenepo tiyenera kulingalira za phunziro la kuchepetsedwa kwa Khristu pamaso pa asirikali a Chiroma, popemphera kuti pangathe kukhala kulingalira kopindulitsa pa za chikondi cha Yesu, "ameneyo, chifukwa cha chimwemwe choikidwacho pamaso pake, anapilira mtanda, nanyoza manyazi, nakhala pa dzanja la manja la mpando wachifumu wa Mulungu. Pakuti talingalirani Iye amene adapilira ndi ochimwa otsutsana naye kotere, kuti mungaleme ndi kukomoka m'moyo mwanu." (Ahebri 12:2-3).

Yesu alamulidwa Kuphedwa, Mpingo upatsidwa ufulu.

Tiyeni tsopano tiwerenge mau a Mulungu, amene analemba zochitika pamapeto a chigamulo cha Ambuye Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu. Pilato, atamuyesa Yesu ndi kupeza kuti palibe cholakwa chiri chonse mwa Iye, anafunsa a Yuda, "Nanga ndidzachita chiyani ndi Yesu, wochedwa Khristu? Onse anati, Apachikidwe pamtanda. Ndipo iye anati, Chifukwa ninji? Anachita choipa chotani? Koma iwo anafuulitsa kopambana, Apachikidwe pa mtanda. Koma Pilato poona kuti sanafitse, koma kuti linapambana phokoso, anatenga madzi, nasamba manja pamaso pa khamulo, nati Ine ndiribe kuchimwira mwazi wa munthu uyu wolungama, mudzionere nokha. Ndipo anthu onse anavomereza, ndi kuti, Mwazi wake uli pa ife ndi pa ana athu. Pomwepo iye anamasulira iwo Baraba, koma anakwapula Yesu, nampereka Iye kuti akampachike pamtanda. Pomwepo asirikali a kazembe anamuka naye Yesu ku bwalo la mirandu, nasonkhanitsa kwa iye kwamu lonse. Ndipo anavula Malaya ake, namveka Malaya ofiira achifumu. Ndipo analuka korona waminga, namveka pamutu pake, namgwiritsa bango m'dzanja lamanja lake; ndipo anagwada pansi pamaso pake, namchitira chipongwe, nati Tikuoneni, Mfumu ya Ayuda! Namthira malovu, natenga bango, nampanda Iye pamutu. Ndipo pamene anatha kumchitira Iye chipongwe, anavula malaya aja, namveka Iye malaya ake, namtsogoza Iye kukampachika pamtanda." (Mateyu 27:22-31).

Powerenga ndime iyi tikukumbutsidwa za mau a Kayafa nthawi ya m'mbuyo isanafike nthawi iyi yomwe amamuzenga mulandu Yesu. "kapena simuganiza kuti nkokoma kwa inu kuti munthu m'modzi afere anthu, ndi kuti mtundu wonse usaonongeke . Koma ichi sananena kwa iye yekha; koma pokhala mkulu wa ansembe chaka chomwecho anayenera kuti Yesu akadzafera mtunduwo; ndipo si chifukwa cha mtunduwo wokha ai, koma kuti akasonkhanitse pamodzi ana a Mulungu akubalalikawo." (Yohane 11:50-52). Kulira kwa a Yuda kuti mwazi wa Yesu ukhale pa iwo ndi pa ana awo, kunakwaniritsidwa ndi maweruzo oopsya omwe anawafikira pa nthawi imeneyo mpaka pano, kuyambira ndi kuonongeka kwa Kachisi ndi kupasuka kwa Yerusalemu mu chaka cha 70 AD. Koma palinso uneneri wa uzimu wozama mu mau awa, womwe umalankhula za kukwaniritsidwa kwake kwa mwazi woombola wa Khristu. Motero ambiri a aYuda eni anaitanidwa mwa chisomo, chifukwa timawerenga kuti pa Pentekoste (phwando la zoyambirira kucha) za anthu zikwi omwe "analanditsidwa m'mitima yawo." Ndipo analandira mokondwera Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. (Machitidwe 2:37).

Pilato wochimwayo, anavomerezanso kuti Yesu anali wopanda mlandu, wopanda chifukwa mwa Iye. Pilato mosazindikira anachitira umboni kuti imfa ya Yesu inakhala nsembe yangwiro ndi yovomerezeka ya chimo, Mwana wa nkhosa wopanda banga kapena chilema. Kumasulidwa kwa Barabba ndi chimodzimodzinso ndi chifanizo cha chipulumutso cha ochimwa. Chilango cha imfacho ndi kutsanulidwa kwa mkwiyo wa Mulungu Atate sunasenzedwe ndi ochimwa omwe anayenera kuusenza chifukwa cha chimo, koma unasenzedwa ndi Yesu Khristu Mwana wa Mulungu. Pomwe ichi chavumbulutsidwa kudzera mwa Mzimu Woyera, wochimwa yemwe wakhulupirira amamasulidwa pa ufulu wa Uthenga Wabwino.

Dzina limeneli lakuti Barabba, ndi lodzala ndi tanthauzo la uzimu, chifukwa mu Chingerezi litanthauza kuti “mwana wa atate”. Monga wachifwamba, Barabba amatsatira mapazi a Kaini, mwana wa Adamu atate wathu woyamba. Mwa chibadwidwe cha ku thupi okhulupirira onse ali ana a Adamu yemwe anagwa mu uchimo, ndipo tasanduka bwinja ndipo tayenera imfa. Koma taonani! Barabba wapatsidwa ufulu, ndipo Yesu wapachikidwa pa mtanda, “kuti akaombole iwo akumvera lamulo, kuti ife tikalandire umwana.” (Agalatiya 4:6). Wotanthauzira Baibulo wotchedwa Gill analemba “kuti Barabba” anali chifanizo cha osankhika a Mulungu monga mwa umunthu, womasulidwa ndi kupatsidwa ufulu pomwe Yesu anamangidwa. “(Ngakhale kuti tiyenera kumvetsetsa kuti Mau a Mulungu samafotokoza ngati Barabbayo pambuyo pake anayitanidwa mwa chisomo.) Kotero kuti ife, amene tachimwa kwakukulu ndi kulanda Mulungu ulemerero Wake, tapatsidwa kukhala ana a Atate wathu wakumwamba komanso abale a uzimu a Yesu. Mpingo woomboledwa wa Khristu unapatsidwa dzina lolondola lakuti Israeli wauzimu, chifukwa dzina lakuti Israeli litanthauza kuti “kalonga wa Mulungu”. Kalonga ndi mwana wa Mfumu.

Yesu Akwapulidwa.

Patatha apo Pilato analamula kuti Yesu akwapulidwe, ngakhale kuti anavomereza kuti ali wosalakwa. Koma ndi chifukwa chiyani waulamuliroyo anachita chosalungama mokwiya chotere? Kodi kapena ndi chifukwa chakuti anasamalira pang’ono za izi? Zikhoza kutheka kuti zinali choncho m’malingaliro a Pilato; koma mu zolinga za mphamvu za Mulungu anali kukwaniritsa uneneri wokamba za Messiah. “Ndinapereka msana wanga kwa omenya, ndi masaya anga kwa iwo amene anakudzula tsitsi langa; sindinabisira nkhope yanga manyazi ndi kulavulidwa.” (Yesaya 50:6). Wolemba Masalmo analembanso mu uneneri, “Olima analima pamsana panga; anatalikitsa mipere yawo.”(Masalmo 129:3). Koma taonani kudzichepetsa kwa kachete kwa Muomboli! “Iye anatsenderezedwa koma anadzichepetsa yekha osatsegula pakamwa pake; ngati nkhosa yotsogoleredwa kukaphedwa, ndi ngati mwana wa nkhosa amene ali du pamaso pa omsenga, motero sanatsegula pakamwa pake.” (Yesaya 53:7).

Zimakhala zopweteka pa kudzikweza kwathu pomwe tanamiziridwa! Timafuna mwamsanga kuti tichitepo kanthu, makamaka pomwe tachepetsedwa pa gulu la anthu kufikira ku imfa! Koma Ambuye Yesu anavutika mwakachete. Amadziwa yemwe amamuvutikira mu chikondi chamgwiro ndi chisomo. “Ndipo chimene chiri chonse mukafunse m’dzina langa,ndidzachichita, kuti Atate akalemekezedwe mwa Mwana.” (Yohane 14:13). “Umo chidaoneka chikondi cha Mulungu mwa ife, kuti Mulungu anamtuma Mwana wake wobadwa yekha , alowe m’dziko la pansi, kuti tikhale ndi moyo mwa Iye. Umo muli chokondi sikuti ife tinakonda Mulungu, koma kuti Iye anatikonda ife, ndipo anatuma Mwana wake akhale chiombolo chifukwa cha machimo athu.” (1 Yohane 4:9-10).

Zinthu izi ndi zoposa chidziwitso cha umunthu, koma tilole kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera kuti tipemphere kuti zoonadi izi zivumbulutsidwe kwa ife. Dalitso loposa lotani kuti tithandizidwe kunena pamodzi ndi Yohane, "Ndipo tidziwa kuti Mwana wa Mulungu wafika, natipatsa ife chidziwitso, kuti tizindikire Woonayo, ndipo tiri mwa Woonayo mwa Mwana wake Yesu Khristu. Iye ndiye Mulungu woona ndi moyo wosatha." (1 Yohane 5:20). Pempho langa ndi lakuti tilole kulimbikitsidwa mwa mtengo wapatali ndi lonjezo la Ambuye wouka kwa akufa loperekedwa ku mipingo; "Taona, ndaima pakhomo, ndigogoda; wina akamva mau anga nakatsegula pakhomo, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine." (Chivumbulutso 3:20).

Chisoti cha Minga

Atatha kumukwapula Ambuye Yesuyo, anatsogozedwa kuchoka pamenepo ndi asirikali a boma la Chiroma kuti akumane ndi ndondomeko ina ya zochitika zankhanza ndi zochititsa manyazi. Asirikali amakondweretsedwa nazo kwambiri, zonyoza ndi kupereka ululu wambiri. Komatu asirikaliwa, chimodzimodzinso a Yuda, amakwaniritsa zolingalira zokhazikitsidwa ndi Mulungu. Komabe, pang'ono amazindikira zomwe zimatsimikizidwa ndi zochita zawo zofuna kuvulaza zoomwe amachitira Muomboli. Poyamba tiyeni tilingalire za kuvekedwa "mkhanjo wa chibakuwa" womwe Ambuye anavekedwa, komanso pa Yohane 19 akufotokozanso "maraya achibakuwa". Mtundu uwu wa mkanjo umaimira, mu ulamuliro woipa wa dziko la pansi, monga timawerenga za Danieli, kuti Belisazala ndipo analengeza kuti "Pamenepo Balisazala analamulira, ndipo anaveka Daniele chibakuwa, ndi unyolo wagolidi m'khosi mwake, nalakira za iye kuti ndiye wolamulira wachitatu m'ufumumo." (Danieli 5:29). Kuonjezera apo, mikanjo yapadera ya Akazembe a Chiroma imafotokozeredwa ndi odziwa mbiri yakale kuti, cholinga cha asirikali chinali chakuti amuveke Ambuye Yesu monyoza mu mkanjo woyerekezera wa Mfumu kapena Kaesara, Posungitsa mulandu womwe anamuzenga wakuti Yesu anali Mfumu. Patatha apo anapitirira ndi kumuveka chisoti chomwe sichinali chopangidwa ndi golide, komatu minga!

Mwambo wankhanza umenewu umapangitsa diso la uzimu ndi la chikhulupiriro kukhazikika pa choonadi cha Mau a Mulungu, kuti Mulungu Atate anapanga Ambuye Yesu, "Ameneyo sanadziwa chimo anamyesera uchimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu mwa Iye." (2 Akorinto 5:21). Chinthu ichi ndichodzidzimutsa ku maganizo a umunthu polingalira za mtundu wa mkanjo, umene asirikali anamveka Yesu kuti unali wa mkazi wachigololo wa ku Babulo "anavala chibakuwa ndi mlangali," (Chivumbulutso 17:4). Zovuta kufotokozerekatu zinthu izi za mnyozo ndi kutukwanidwa komwe anamuchitira Mwana wa Mulungu wosachimwa ndi wodala! Komabe, pomuveka Ambuye Yesu chovala chimenechi zimayerekeza uchimo, kudetsedwa komanso udani ndi Mulungu, zomwe zikukhazikitsa chiphunzitso cha mtengo wapatali chakuti Ambuye Yesu anasenza machimo osakhumbika konse a anthu Ake, osankhika. Malo omwe anamusungiratu wachigololoyo, Satana ndi

womutsatira ake ndiwo chilango chamuyaya ku Gehena, “nyanjayo ya yamoto yakutentha ndi sulfure .“ (Chivumbulutso 19:20). Awo ndi malo omwe ali oyenera wina aliyense chifukwa cha chimo. Komabe, Ambuye Yesu anasenza chilango ichi m’malo mwa anthu Ake okondedwa. Temberero lomwe linafika chifukwa cha kuphwanya chilamulo linasenzedwa ndi Yesu. “Khristu anatiombola ku temberero la chilamulo, atakhala temberero m’malo mwathu; pakuti kwalembedwa, Wotembereredwa ali yense wopachikidwa pa mtengo.” (Agalatiya 3:13).

Chovala cha chiBabulo, chomwe asirikali anamuveka Yesu, chimayerekezera za chipembedzo chonama. Anthu a Ambuye ali nacho mwa iwo chikhalidwe cha uchimo chomwe chimatsatira chipembedzo cha Babulo wauzimu. Zonse zomwe zimatsutsana ndi malamulo a Mulungu zimakondweretsa munthu wakale wauchimo, zomwe zimakondwerera mu mafano ndi chigololo cha uzimu. Koma pomuveka Yesu mkanjo wa kapezi ndi wa chibakuwa, asirikali mosazindikira amatsimikiza kuti mkwiyo wa Mulungu womwe uyenera kuperekedwa chifukwa cha chimo umayenera kugwera pa Yesu, yemwe amayembekezera kuti apachikidwe kuti afe pa mtanda pa Kalvari. Ambuye Yesu anavekedwa mu manyazi kuti ife tivekedwe mu chilungamo!

Komabe, tiyeni tisiyanitse ndi mwazi wa mtengo wapatali wa Khristu womwe unakhetsedwa kwa ulele pa Kalvari, monga wolemba ndakatulo akufotokoza mokometsera.

Mulungu wamkulu! Kuchokera uko palibe chobisika.

Inu mumaona mkati mwanga;

Kwa Inu nthawi zonse ndimaima wovumbulutsidwa.

Ndendende monga momwe ndili.

Potero kuti, sindingathe kusenza.

Zomwe mwa Ine ndimaona;

Woipa ndiponso wakuda ndi momwe ndimaonekera,

Mulungu Woyera, kwa Inu.

Koma popeza Mpulumutsi wanga amaima pakati,

Mu zovala zodonthetsedwa mwazi,

Ndi Iyeyo, m’malo mwa ine, ndiye amaoneka.

Pomwe ndifika kwa Mulungu.

Kotero kuti, ngakhale wochimwa, Ndiri wotetezedwa,

Amadandaulira, pamaso pa mpando wa chifumu,

Moyo wake ndi imfa yake m'malo mwa ine,

Nanena kuti machimo anga ndi ake.

Chikondi chodabwitsa chotani chotere, zinsinsi zotani,

Kuwala mkukumana naye!

Zolakwa zanga za uchimo ndi Zake,

Ndi kumvera kwake ndi kwa ine.

(Newton)

Chisoti cha minga chimayerekeza kopambana za chotetezera cha uchimo kwa Khristu. Munga umafotokozeredwa poyamba mu bukhu la Genesis monga chotsatira cha kugwa kwa munthu; "nthaka ikhale yotembereredwa chifukwa cha iwe; mkusauka udzadyako masiku onse a moyo wako; minga ndi mitula idzakubalira iwe."(Genesis 3:17-18). Mtumwi Paulo akuonjezera kuti, "koma ikabala minga ndi mitungwi, itayika; nitsala pang'ono ikadatembereredwa; chitsiriziro chake ndicho kutenthedwa." (Ahebri 6:8). Chisoti cha minga chimayerekezera kuti Ambuye Yesu anapangidwa "kukhala temberero m'malo mwathu". Chikuonetseranso kukwaniritsidwa kwa uneneri wa Yesaya; "Iye ananyozedwa ndi kukanidwa ndi anthu; munthu wa zisoni." (Yesaya 53:3). M'malo mwa temberero ndi kukanidwa zomwe zinayenera kugwera anthu ake chifukwa cha chimo, zinagwera pamutu pa Muomboli. "Ndipo anayamba kuwaphunzitsa, kuti kuyenera kuti Mwana wa munthu akamve zowawa zambiri, nakakanidwe ndi akuru ndi ansembe akulu ndi alembi nakaphedwe, ndipo mkucha wake akauke."(Marko 8:31).

Tsiku la Chotetezera.

Kuvekedwa kwa chisoti cha minga pamutu pa Yesu ndi chikwaniritso cha chifanizo chomwe chidakhazikitsidwa pa tsiku la chotetezera, pomwe machimo a anthu mwa mwambo amachotsedwa pa anthu kuwapititsa pa mbuzi yomwe imapititsidwa ku chipululu. "Aroni aike manja ake onse awiri pamutu pa mbuzi yamoyo, ndi kuvomereza pa iyo mphulupulu zonse za ana a Israeli, ndi zolakwa zawo zonse; naike izi pamutu pa mbuziyo, ndi kuitumiza kuchipululu

ndi dzanja la munthu wompangiratu.” (Levitiko 16:21). Kotero kuti chisoti cha minga, choimira chipatso cha kugwa kwa Adamu, chinaikidwa pamutu pa Yesu, kutsimikizira kuti machimo a anthu a Mulungu aikidwa pa udindo wake. Monga mbuziyo pansi pa chilamulo imatumizidwa ku chipululu, chomwechonso Ambuye Yesu anakumana nazo m’malo mwa anthu ake okondedwa, pomwe anali pa mtanda, anamva kuwawa koopsya ndi kusiyidwa ndi Atate Wake. Izi zikufotokozedwa mu mau olasa awa. “Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji Ine.” (Mateyu 17:46). Zoonadi zake za izi zikufotokozedwa mokoma ndi wolemba ndakatulo iyi.

Osati mwazi wonse wa nyama,

Pa maguwa a Yuda zinaphedwa,

Zikanapereka chikumbu mtima chotsutsika mtendere.

Kapena kuyeretsa banga.

Koma Khristu, Mwana wa nkhosa wakumwamba,

Achotse machimo athu onse;

Nsembe ya dzina loposa,

Ndi mwazi wamtengo wapatali uwo.

Chikhulupiriro changa chikadagwira dzanja lake,

Pa mutu wokondeka wa Inu;

Mwakumva kulakwa kwanga ndiima.

Pamenepo ndi kulapa chimo langa.

Moyo wanga uyang’ana m’mbuyo kuti uone,

Katundu yemwe munasenza,

Pomwe munali pa mtengo wotembereredwa,

Ndi kuyembekezera kuti cholakwa chake chinali pamenepo.

Kukhulupirira, tikondwera,

Kuona temberero likuchoka;

Timadalitsa Mwana wa nkhosa ndi mau a chikondwerero,

Ndi kuimba chikondi chokhetsedwa chake.

(Watts)

Chikondi Champhamvu ndi Chokondetsetsa cha Ambuye.

Ngati tidzaza mitima yathu ndi chikondi kwa Mulungu, ndi chifukwa chakuti Mulungu ndiye anayamba kutikonda. (1 Yohane 4:19). Chikondi cha Mulungu ndi chomwe chimapangitsa kuti wochimwa aliyense apulumutsidwe, "Koma Mulungu wolemera ndi chifundo, chifukwa cha chikondi chake chachikulu chimene anatikonda nacho, tingakhale tinali akufa m'zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi Khristu (muli opulumutsidwa ndi chisomo), ndipo anatiukitsa pamodzi, natikhazikitsa pamodzi m'zakumwamba mwa Khristu Yesu.' (Aefeso 2:4-6). Chinthu chochititsa chidwi ndi chakuti mau akuti "pamodzi" akubwerezedwa, kutsindika za umodzi wodala wa Khristu ndi mpingo. Umodzi uwu unachitika chifukwa cha mphamvu ya nsembe yamngwiro yomwe Yesu anapereka chifukwa cha machimo a anthu ake okondedwa, pomwe Iye anazunzika kuchepetsedwa kotero, chifukwa chaiwo. Ndi chikondi ichi chomwe chimamukoka wochimwa wofunafuna chipulumutso. Timawerenga za mpingo ukulankhula za Yesu mu uneneri. "Chifukwa chake anamwali akukonda. Undikoke; tikuthamangire; Mfumu yandilowetsa m'zipinda zake: Tidzasangalala ndi kukondwera ndi iwe. Tidzatchula chikondi chako koposa vinyo. Akukonda molungama." (Nyimbo ya Solomo 1:3-4). Mu ubwino wa Mulungu, si mphenzi za chilamulo mu chikumbumtima, komwe kumatsogolera ochimwa ku kulapa. (Aroma 2:5).

Chomwe chiri cha mphamvu ndi chokondetsa kwa anthu a Mulungu ndi chakuti Yesu anadza komwe iwo ali. Povala chisoti cha minga Ambuye anasenza machimo awo ndi mphulupulu zawo. Mu Nyimbo ya Solomo Ambuye akulengeza kuti, "Ndine duwa lofiira la ku Saroni, ngakhale kakombo wa ku zigwa.' (Nyimbo ya Solomo 2:1). Duwa lofiira limatsimikiza za fungo lake lokoma la nsembe pomwe amakhetsa mwazi wake wa mtengo wapatali, ndipo kakombo wa mzigwa amayimira kudzichepetsa kwake pololera kutenga maonekedwe a umunthu monga munthu wangwiro. Komatu Ambuye amakamba za mpingo monga kakombo, wangwiro ndi wopanda chimo Iye akamamuona. "Ngati kakombo pakati pa minga. Momwemo wokondedwa wanga pakati pa ana akazi." (Nyimbo ya solomo 2:2). Monga izi si za ochimwa zokha, zomwe Akhristu amakhala pakati pa izo, komatu ndi mphulupulu zomwe ziri mwa ife zomwe anthu amazitengera kuchokera kwa munthu wakale wachimo. Koma taonani! Khristu yemwe ndi

“kakombo wa mzigwa” anavala chisoti cha minga kuti awombole iwo omwe anayenera kukondedwa ndi Iye. Anatenga chikhalidwe chawo pa Iye, (chimo lokha analibe), kuti iwo athe kukhala pamodzi ndi Iye kumwamba; “Wokondedwa wanga ndi wa ine, ine ndine wake: Aweta zake pakati pa akakombo.” (Nyimbo ya Solomo 2:16).

Chipatso cha Mzimu.

Pomwe pali machitidwe a mphamvu a Mzimu Woyera ovumbulutsa za chikondi cha Khristu mu mtima wa okhulupirira, padzakhala chipatso chauzimu chochuluka m’moyo wawo ndi makhalidwe. “M’malo mwa mithethe mudzaturuka mtengo wa mlombwa; ndi m’malo mwa lunguzi mudzamera mtengo wa mchisu; ndipo chidzakhala kwa Yehova ngati mbiri, ngati chizindikiro chosatha, chimene sichidzalikhidwa.” (Yesaya 55:13). “Chotero, abale anga, inunso munayesedwa akufa ku chilamulo ndi thupi la Khristu; kuti mukakhale ake a wina, ndiye amene anaukutsidwa kwa akufa, kuti ife timbalire Mulungu zipatso.” (Aroma 7:4). Mphatso za uzimu izi, monga chikondi, chimwemwe ndi mtendere.” (Agalatiya 5:22-23), ziri zofunika koposa m’moyo wa mkhristu ndipo zizikhala ndi ntchito zenizeni, chifukwa “chikhulupiriro chopanda ntchito nchakufa.” (Yakobo 3:26).

Ngakhale ziri choncho, Ambuye anaona kuti ndi koyenera kulola mayesero ndi chiwawa cha Satana. Chivuto chomwe chilipo sichikhala cha kunja kokha kudzera kwa ochimwa, chomwe chiyenera kupiriridwa nthawi ndi nthawi, koma pali nkhondo yosatha pakati pa munthu wakale wa uchimo ndi munthu watsopano wa chisomo. Mtumwi Paulo anakamba za “munga m’thupi, ndiye mngelo wa Satana kuti anditundudze, kuti ndingadzikwezeke koposa.” (2 Akorinto 12:7). Chomwe chiri chokhumudwitsa koposa kwa okhulupirira ndi munga wa chimo lokhala mwa munthu. Koma Ambuye anapita patsogolo pa anthu Ake. Yesu anavala chisoti cha minga chomwe anachimenyera m’mutu Wake, anavutika kwambiri kosatheka kuyezeka, koposa kuvutika kwa ife, Kudzera mu izi anapambana Satana ndi antchito ake, anauka kwa akufa namasula anthu Ake ku mphamvu ndi chilango cha chimo.

Pomwe mtumwi Paulo analemba za “munga “ sakunena za munga umodzi waung’ono chabe, womwe okhoza kukhala cholasa china chake chongosowetsa mtendere. Mau omwe akugwiritsa ntchito ochokera mu chilankhulo cha chi Griki akadakhoza kutanthauzanso “ndodo ya mtengo yolimba kapena ndodo ya chitsulo yosongola mbali imodzi”, ndipo ndi yosiyana ndi yomwe ikugwiritsidwa ntchito kwina kulikonse pokamba za munga. Kotero kuti, mu kalata yake ku mpingo wa ku Akorinto, Paulo akugwiritsa ntchito mau omwe akutsimikiza kuti ndi chida chachikulu chopweteka chomwe amabaila thupi. Chimo silimangobaya pang’ono pokha, koma ndi yesero lopweteka kwa okhulupirira yemwe mwachisomo waphunzitsidwa. Monga Paulo, Mkhristuyo analira mkwati mwa iye mwini, “Munthu wosauka ine; adzandipulumutsa ndani m’thupi la imfa iyi?” Koma pomwe chikhulupiriro cha mtengo wapatali chaperekedwa kwa munthu, amaona chikondi cha Muomboli ndipo atha kunena pamodzi ndi Paulo, “Ndiyamika

Mulungu, mwa Khristu Yesu Ambuye wathu. Ndipo chotero ine ndekha ndi mtimatu nditumikira chilamulo cha Mulungu; koma ndi thupi nditumikira lamulo la uchimo." (Aroma 7:24,25).

Chikondi cha Umulungu ndi Kupindula mu Mipingo.

Kuchokera mu chikondi cha Khristu muli chikoka chomwe wochimwa amachimva. Chikoka ichi cha Muomboli wodalitsika ndi chofunikira kwambiri ku thanzi la mipingo ndi utumiki. Popanda ichi, pamakhala kusabereka kwakukuru komanso kuzizira kwa uzimu. Kuchokera mu chikoka cha Ambuye Yesu kumatsika chikoka cha zisomo za Akhristu anzathu. Pomwe chikondi cha Khristu sichikhazikitsidwa mu uthunthu wake mu utumiki, chikondi chomwe okhulupuirira amakhala nacho pakati pa wina ndi mnzake chimazilala. Martin Luther anachenjeza Akhristu oona za kumuona Yesu ngati Woweruza waukali, chifukwa motsutsana ndi ichi Ali Mpulumutsi wokonda ndi wachifundo kwa anthu Ake. Ngati Khristu akhazikitsidwa ndi nkhanza ndiponso mwamphamvu, zikhoza kupangitsa kuti anthu akhoza kukhala ndi mtima wakuti mu Chikhristu muli nkhanza ndi chiweruzo mu mipingo. Lamulo la Yesu silidzasamalidwa, "Ndikupatsani inu lamulo latsopano, kuti mukondane wina ndi mnzake. (Yohane 13:34).

Pali zizindikiro zoonjezera zomwe zimatsatira kunyozera kwa anthu ku chikondi ndi chikoka cha Yesu Khristu mu mipingo. Tiyeni tilingalire za fanizo la matalente lomwe lipezeka pa Luka 19. Iwo omwe anapindula ndi matalente omwe anapatsidwa udindo wakuwapindulitsa, sanabweretse chipatso cha kulemekeza Mulungu chokha m'miyoyo yawo, komanso panali kukula kwa machitachita a kufikitsa kwa choonadi. Potsutsana ndi ichi, munthu yemwe anakulunga talente m'nsaru, anamuona Ambuye kuti ndi munthu "wouma mtima" ndipo anabwezera mbuye wake yosapindulitdsidwa. (Luka 19:20-21). Ili ndi chenjezo kwa iwo omwe amamutenga Mulungu m'modzi mwa Atatu, makamaka Ambuye Yesu Khristu monga munthu "wouma mtima", pomwe chiweruzo ndi chilango cha uchimo zitchinga chisomo cha chikondi chotetezera cha Mpulumutsi. Pansi pa chikhalidwe chotere kapena utumiki wotere sipakhala chikhumbo choyaka chochokera mu mtima chopangitsa kuwauza ena za Uthenga wabwino wa chipulumutso, popeza sipakhala Mpulumutsi wokonda wakuti alankhule za iye. Uthenga Wabwino umabisika m'nyumba zopempherera, ndipo siumveka m'dziko lonse la pansi.

Zinali zosiyaniranatu ndi mpingo wa ku Atesalonika. Paulo analembatu za zochitika zamphamvu za mau a choonadi mwa Yesu Khristu. "Kuti Uthenga Wabwino wathu sunadza kwa inu m'mau mokha, komatunso mumphamvu, ndi mwa Mzimu Woyera, ndi m'kuchuruka kwakukuru; monga mudziwa tinakhala onga otani mwa inu chifukwa cha inu. Ndipo munayamba kukhala akutsanza athu, ndi a Ambuye, m'mene munalandira mauwo m'chisautso chambiri, ndi chimwemwe cha Mzimu Woyera: kotero kuti munayamba kukhala inu chitsanzo kwa onse akukhulupirira m'Makedoniya ndi m'Akaya. Pakuti kuturuka kwa inu kudamveka mau a Ambuye, osati m'Makedoniya ndi Akaya mokha, kumatu m'malo monse chikhulupiriro chanu cha kwa Mulungu chidaturuka; kotero kuti sikufunika kwa kulankhula kanthu." (1 Atesalonika

1:5-8). Paulo akulemba za mphamvu za Uthenga Wabwino m'mitima ndi miyoyo yawo, chitsimikizo cha chipulumutso chawo, chimwemwe cha Mzimu Woyera mkati mwa masautso, komanso kutumiza kwa Uthenga Wabwino kuchokera ku mpingo wa ku Atesalonika. Kodi zimenezi zikhoza kunenedwanso kwa ife monga mpingo komanso ali yense wa ife payekha payekha. Komabe, tiyenera kusamala za ntchito za thupi zomwe amachita munthu; koma tiyeni tifunefune mphamvu ya Mzimu Woyera yakugwira ntchito kudzera mwa anthu a Ambuye.

Ophunzira a Yesu, omwe anali mboni chifukwa anaona ndi maso awo za chikondi chodabwitsa cha Ambuye Yesu, komanso anachitira umboni za kuzunzika kwake ndi imfa yake, analandira utumiki waukulu: "Mukani ku dziko lonse la pansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse." (Marko 16:15). Ntchito iyi siinaperekedwe kwa ophunzira okha, komanso kwa mpingo wa Khristu mpaka kubwera kwake kwa Ambuye kwachiwiri. Onse a ana a Mulungu sanaitanidwe kukhala atumiki; koma onse aitanidwa kuti aonetsere Khristu wamtengo wapatali mu malankhulidwe ndi chikhalidwe chawo, komanso kuti apempherere antchito a Mulungu pomwe akugwira ntchito mu Uthenga Wabwino.

Taonani chokhumba chachikulu cha ophunzira chomwe anali mchikakamizo cha Mzimu Woyera kuti achenjeze, osati za chiweruzo chomwe chikubwera chokha, komanso kuti alengeze ndi chimwemwe za chipulumutso cha ulemerero ndi Uthenga Wabwino wa Ambuye Yesu wouka kwa akufa. Pomwe palibe kukhudzika kochitachita kokhudza chipulumutso cha iwo omwe ali kunja kwa gulu lathu la okhulupirira, pali choopsya chakuti talente lasungidwa mkansaru ndipo chifukwa cha chimenecho pali moyo wauzimu wochepa.

Kotero kuti, tilole chikoka cha Khristu mu chikondi chake chitikwanire m'miyoyo yathu ndi m'mipingo yathu, podziwa lonjezo la mtengo wapatali kwa auzimu; "Maso ako adzaona mfumu m'kukongola kwake; iwo adzaona dziko lakutari." (Yesaya 33:17). Tiyeni tipemphere kuti Mzimu Woyera athe kutivumbulutsira ife chikondi cha Khristu mu kuzunzika ndi imfa yake, kuti zipatso za Mzimu Woyera zichuluke. Pakhale chikondi cha zinthu zachisomo, chikondi cha pa abale ndi kudana ndi chimo. Mipingo imasulidwe kuchoka ku mzimu wosakhululuka wa ukali, ndi wosamva chisoni, komatu tiyeni tikhululukirane moona mtima kuchokera pansi pa mtima, monga Yesu anakhululukira zochimwa zathu. "Okondedwa, tikondane wina ndi mnzake: chifukwa kuti chikondi chichokera kwa Mulungu, ndipo yense amene akonda, abadwa kuchokera kwa Mulungu, namzindikira Mulungu. Iye wosakonda sazindikira Mulungu chifukwa Mulungu ndiye chikondi." (1 Yohane 4:7-8).

MUTU 5

KUPACHIKIDWA PA MTANDA

Yesu Yekha.

Panopa tafika pa kupachikidwa kwa Yesu pa mtanda, pachimake pa mabuku okamba za Uthenga Wabwino. Mu ichi tikuona kukwaniritsidwa kwa zifanizo za tsiku la chotetezera. Kupachikidwa kwa Yesu pa mtanda ndiye pakatikati pa Uthenga wa chipulumutso. Mtumwi Paulo analembera mpingo wa ku Akorinto, "Pakuti ndinatsimikiza mtima kuti ndisadziwe kanthu mwa inu, koma Yesu Khristu wopachikidwa.' (2 Akorinto 2:2). Yesu ananena za kupachikidwa kwake; "Ndipo Ine, m'mene ndidzakwezedwa kudziko, ndidzakoka anthu onse kwa Ine ndekha." (Yohane 12:32).

Satana amakhumba kuti mtumiki atembenuzidwe kuti asiye kulalikira Yesu, kuti utumiki waukulu wolalikira ku dziko la pansi, usiyidwe pambali. Momwemonso, Satana amayesa membala aliyense wa mpingo kuti njala yawo yauzimu ya Khristu ichepetsedwe. Tiyeni tichenjezedwe ndi kukhala atcheru ku makhwekhwe a Satana. Tiyeni tisamalitse za momwe tiyenera kufikira kwa Ambuye podzamulandira ndiponso kumva mau akulalikidwa. Kodi tiri pa maondo athu kumupempha Ambuye kuti apereke kutsanulira kwa Mzimu Woyera, kuti atumiki athe kulalikira Khristu Yesu kudzera mu mphamvu ya umulungu komanso mu ulamuliro? Kodi timapemphera kuti makutu amve ndi kuti mtima udziwe? Kapena timangopita pokhumba kuti tikalandire chokoma china chake cha dziko la pansi chokha, kapena kukangosangalatsidwa? Ambuye Yesu analengeza kuti, "Muthange mwafuna ufumu wake ndi chilungamo chake, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu." (Mateyu 6:33). Panali pa mtanda pomwe mwazi wa Yesu unakhetsedwa kwathunthu kuti ateteze machimo; ndiponso ndi kudzera mu moyo wake wolungama ndi kukhetsa mwazi kuti okhulupirira woona aliyense amayesedwa wolungama.

Kalvari.

Kuchokera ku malo omwe anamunyozera ndi kumuchititsa manyazi Yesu, omwe ife tawalingalira mu mutu wapitawo, ndi komwe anamtengera Yesu kuti akapachikidwe. "Ndipo pamene anafika ku malo dzina lake Bade anampachika Iye pamtanda pomwepo, ndi ochita zoipa omwe, m'modzi ku dzanja la manja ndi wina ku la manzere. Ndipo Yesu ananena, Atate, muwakhululukire iwo, pakuti sadziwa chimene achita. Ndipo anagawana zovala zake, poyesa maere." (Luka23:33-34).

Kupachikidwa pa mtanda ndicho chilango chankhanza ndi chopweteka kwambiri chomwe chinkaperekedwa. Atakhomera manja ndi mapazi ku mtengo, wozengedwa mulandu amalendewera pa mtanda ndi mabala ake akukha mwazi pang'ono pang'ono kuti afe. Kumatu mu zonsezi Ambuye ananena kuti, "Atate muwakhululukire iwo." Ngakhale kuti asirikali a chi Roma ndi omwe anampachika Yesu, komatu zinachitika choncho chifukwa cha machimo a munthu aliyense wa anthu osankhidwa a Ambuye kuti misomali inakhomedwa m'manja ndi mapazi a Muomboli.

Uchimo umaoneka woipa kwambiri kwa okhulupirira yemwe waomboledwa, pomwe Mzimu Woyera avumbulutsa chiyero cha chilungamo ndiponso chikwapu choopsya (chochititsa mantha) cha chilingamo cha umulungu chomwe chidagwera pa Ambuye Yesu, yemwe "adakhala chimo m'malo mwathu kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu mwa Iye." (2 Akorinto 5:21). Komatu anthu a Mulungu amadabwa pa chikondi cha chisomo cha Utatu wa Mulungu choperekedwa kwa anthu ochimwa chomwe sichinawayenera. Maziko a chipulumutso chawo ali mu chikondi chosafanana ndi china chiri chonse. Yesu anapemphera. "Atate amene mwandipatsa Ine, iwonso akhale pamodzi ndi ine; kuti ayang'anire ulemerero wanga, umene mwandipatsa Ine , pakuti munakonda Ine lisanakhazikike dziko la pansi. Atate wolungama, dziko la pansi silinadziwa Inu; ndipo iwo anazindikira kuti munandituma Ine; ndipo ndinazindikiritsa iwo dzina lanu, ndipo ndidzalizindikiritsa; kuti chikondi chimene munandikonda nacho chikhale mwa iwo, ndi Ine mwa iwo." (Yohane 17:24-26).

Motero ndi momwe chikondi chamuyaya cha Mulungu Mwana chinavumbulutsidwa mu Mau a Mulungu; ndiponso pali ponse pomwe Mulungu Mzimu Woyera agwira ntchito mu mtima wa okhulupirira, padzakhala chikondi ichi chochitachita mwa muyeso umodzimodzi. Mau a mtumwi Paulo ayenera kulandira kukhulupirika pa kulalikidwa kwa Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. "Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyerera monga mwa kalilore ulumerero wa Ambuye, tisandulika m'chithunzithunzi chomwechi kuchokera ku ulemerero kumka ku ulemerero, monga ngati kuchokera kwa Ambuye Mzimu." (2 Akorinto 3:18). Pomwe chikondi cha Mulungu chiwalitsidwa mwa Ambuye Yesu, payenera kuti pakhale kuonetseredwa kwa chikondi ichi m'moyo wa okhulupurira aliyense. Kodi izi ziri choncho ndi miyoyo yathu, kuyambira pa aliyense payekha komanso m'mipingo? Kodi timakhulupirirana kuchokera pansi pa mtima? Ambuye atipatse chisomo chakuyenda mu chilimbikitso, kuopa kuti chitsanzo chathu chingakhale chitonzo ku dzina la Yesu Khristu. "Okondedwa tikondane wina ndi mnzake, chifukwa kuti chikondi chichokera kwa Mulungu, ndipo yense amene akonda, abadwa kuchokera kwa Mulungu, namzindikira Mulungu. Iye wosakonda sazindikira Mulungu; chifukwa Mulungu ndiye chikondi." (1 Yohane 4:7-8).

Yesu Wansembe Wamkulu wathu.

Ngakhale chovala chomwe Ambuye Yesu anavala popita pa mtanda chimatsimikizira kuti Iye ndiye Wansembe Wamkulu. "Pamenepo asirikali, m'mene adapachika Yesu anatenga zovala zake, nadula panayi, natenga wina china, wina china, ndiponso maraya; koma maraya anaombedwa monsemo kuyambira pamwamba pake, analibe msoko. Chifukwa chake anati wina kwa mnzake, Tisang'ambe awa, koma tichite maere, awa akhale a yani; kuti lembo likwaniritsidwe limene linena, Anagawana zovala zanga mwa iwo okha, ndi pa maraya anga anachita maere." (Yohane 19:23-24). Chilungamo cha Khristu ndi changwiro, cholukidwa "chopanda msoko;" Moyo wake unali wangwiro ndi wopanda chimo. Koma tiyeni tifananize za

maraya omwe Yesu anavala ndi maraya a Aroni, wansembe wamkulu. “Ndipo polowa mutu pakhale pakati pake; pakhale mkawo pozungulira polowa pake, wa ntchito yoomba, ngati polowa pa malaya ochinjiriza, pangang’ambike.” (Eksodo 28:32). Izi zinalembedwa chifukwa cha chilangizo chathu. Zimaonetsa umodzi wa ulemerero wa Mau a Mulungu pokhazikitsa udindo wa unsembe wa Ambuye Yesu Khristu.

Tiyeni tipitirire poona za chapachifuwa chomwe Aroni anavala monga wansembe wamkulu. “Ndipo Aroni azinyamula maina a ana a Israeli pa chapachifuwa cha chiweruzo pamtima pake, pakulowa iye m’malo opatulika, akhale chikumbutso pankhope pa Yehova kosalekeza.” (Eksodo 28:29). Pomwe nthawi ino tikulingalira za Yesu monga Wansembe Wamkulu woposa yemwe anakwaniritsa zifanizo za Chipangano Chakale, tikuona kuti Yesu akutenga maina a okondedwa Ake pa mtima wake, iwo amene chifukwa cha iwo anavutika ndiponso kukhetsa mwazi wake wa mtengo wapatali.

Ambuye Yesu anasenza ululu wopweteka kwambiri pa mtanda mwachipiriro. Chikondi ichi chomwe pa umunthu ndi chosatheka kuzindikirika. Mzimu Woyera alole kuvumbulutsa zambiri za ukulu wa chikondi cha Khristu ndi chisomo kwa ochimwa moipitsitsa. Paulo analemba za Yesu kuti: “Yesu, ameneyo, chifukwa cha chimwemwe choikidwacho pamaso pake, anapirira mtanda, nanyoza manyazi, nakhala pa dzanja lamanja la mpando wachifumu wa Mulungu. Pakuti talingalirani Iye amene adapirira ndi ochimwa otsutsana naye kotere, kuti mungaleme ndi kokumoka m’moyo mwanu.” (Ahebri 12:2-3). Pamenepo ndi pomwe timaona kuzunzika kwathu kuti ndi kwakung’ono kuyerekeza ndi kwa Ambuye Yesu. Koma pomwe pavumbulutsidwa kwa ife kuti Khristu anazunzika chifukwa cha machimo athu, timakhala ndi chiyanjano ndi Iye m’mazunzo Ake. (Afilipi 3:10).

Mbava yomwe Imamwalira pa Mtanda.

Tiyeni tione mwapadera kuchititsidwa manyazi kwa kupachikidwa pa mtanda kwa Ambuye Yesu komwe anamuchitira akulu ansembe, alembi ndi akulu, omwe anati, “Anapulumutsa ena, sangathe kudzipulumutsa yekha. Ndiye Mfumu ya Ayuda; atsike tsopano pamtandapo, ndipo tidzamukhulupirira Iye. Amakhulupirira Mulungu; Iye ampulumutse tsopano, ngati amfuna; pakuti anati, Ine ndine Mwana wa Mulungu. Ndiponso achifwambawo opachikidwa pamodzi ndi Iye anamlalatira Iye mau amodzimodzi.” (Mateyu 27:42-44). Atsogoleri odzikuza a chipembedzo anamuda Ambuye, chifukwa anagubuduza ziyembekezo za dziko la pansi komanso chipembedzo cha kuthupi. Sanaone chiri chonse mwa Mpulumutsi wopachikdwa ndi wokhetsa mwazi.

Komatu patapita ka nthawi pang’ono timawerenga mau a mtundu wina omwe mbava imodzi inalankhula. M’malo molalatira Ambuye, mphamvu ya Mzimu Woyera inamufikitsa ku kulapa.

Kenaka mbava yomwe imamwalira pa mtanda inayang'ana kuzunzika kwa Ambuye Yesu, osati ndi diso la umunthu chabe, koma ndi diso la chikhulupiriro.

Zonse zomwe amayembekeza zinapita, machimo ake anali pamaso pake ofiira ngati kapezi, chiweruzo chomwe amaganizira kuti achilandire chinali pamaso pake. Komabe, mphamvu ya Mzimu inatsegula mtima wake, ndipo mu kudzera mu chikondi cha Mulungu wapatsidwa chikhululukiro ndipo anapempha kuti alandire chifundo. Iyeyu anapachikidwa ku thupi ndi ku uzimu pamodzi ndi Khristu. "Ndipo m'modzi wa ochita zoipa anapachikidwawo anamchitira Iye mwano nanena, Kodi suli Khristu Iwe? Udzipulumutse wekha ndi ife. Koma winayo anayankha, namdzudzula iye, nati, Kodi suopa Mulungu, poona uli m'kulangika komweku? Ndipo ifetu kuyenera; pakuti tirikulandira zoyenera zimene tinazichita: koma munthu uyu sanachita kanthu kolakwa. Ndipo ananena, Yesu ndikumbukireni m'mene mulowa Ufumu wanu. Ndipo Iye ananena naye, Indetu, ndinena ndi iwe, Lero lino udzakhala ndine m'Paradaiso." (Luka 23:39-43).

Motero ichi chimakhazikitsa kupembedzera ndi chisamaliro chapadera cha Ambuye Yesu, yemwe tsopano anauka kwa akufa ndi kukwera kunka kumwamba, kwa iwo onse omwe moona mtima ndi mwauzimu amalapa machimo awo, napempha chifundo m'dzina lake. Tiloledwe kuti monga mbava yomwe imamwalira pa mtanda, inadza molimba mtima osalingalira zopempha china chiri chonse koma kulilira chifundo cha umulungu. Pomwe tikulingalira pa Ambuye Yesu, tilole mzimu Woyera atipatse kuona kosatchingika mwa chikhulupiriro za chikondi cha Mulungu Atate. "Pakuti Mulungu amene anati, kuunika kudzawala kuturuka mumdima, ndiye amene anawala m'mitima yathu kutipatsa chiwalitsiro cha chidziwitso cha ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Khristu." (2 Akorinto 4:6).

Wolemba ndakatulo akutipatsa mwaubwino kwambiri chikondi cha chisomo cha Ambuye ndi chisamaliro cha moyo wa mbava yolapayo, ngakhale inali mkati mwa ululu waukulu kwambiri ndi kuzunzika pa mtanda.

Anaona Mpulumutsi akumwalira,

Pambali pake pa mtengo

Komatu, pa mau ake anadalira,

Anaona kuti apereke pempho lake.

Kulapa machimo onse

Mwa khungu anachita ichi

Anatembenuka kuchoka kwa Satana

Nakonda ndi kutumikira Mwana wa Mulungu.

Ndi mu Yuda ndiponso wa mitundu kukanidwa poyera.

Komanso onse odutsa

Mwa udani anakuwa ndiponso kusokosera

Iye sanayankhepo kanthu.

Komwe anamva pemphero

La moyo wolapa

Ngakhale amamwalira akumva ululu.

Anafulumiza kumvera chisoni.

Chikondi chanu cha mphamvu ndi chosalephera.

Mwachangu kulira kwake anamva.

Posamalira wolakwa uyu

Koposa chosowa chanu chachikulu.

Chikondi chimenecho chikhalabe.

Ndipo sichidzatha.

Tipeza mwa Inu, womkhulupurira.

Inu muli yemweyo lero.

(Hallgri'mur Pe'tursson).

Apatu timaphunzira kuti Ambuye Yesu sadzayankha anthu achipembedzo odzikweza, kapena osalungama. Komabe munthu wochimwa yemwe ali pafupi kufa, amene alibe china chiri chonse kupatula pemphero lake lopempha chifundo, adzalandira chifundo. Munthu wotereyu ndiye amene Ambuye adzamukhululukira, mokoma mtima amamumvera ndiponso kumusamalira, inde kounjezera apo kudzitengera kwa Iye Yesu mwini mapeto ake Ulemerero. Mau a Mulungu atero, "Inu nonse, inu akumva ludzu, idzani kumadzi; ndi osowa ndarama adzani inu mugule

mudye; inde idzani, mugule vinyo ndi mkaka opanda ndarama ndi opanda mtengo wake. Tcherani khutu lanu, mudze kwa Ine, imvani, mzimu wanu nudzakhala ndi moyo; ndipo ndidzapangana nanu chipangano chosatha, ndicho zifundo zoona za Davide." (Yesaya 55:1,3). Zoonadi zikhoza kunenedwa kwa munthu yemwe adza kwa Ambuye moyenera: "Pakuti zonsezi mkono wanga wazilenga, momwemo zonsezi zidzaoneka, ati Yehova; koma ndidzayang'anira munthu uyu amene ali waumphawi, ndi wa mzimu wosweka, nanthunthumira ndi mau anga." (Yesaya 66:2).

Tiyeni tikumbukire mwa chisoni za mbava ina ija, yomwe inamwalira wosalapa ndipo idapita komwe ilikumva zowawa ku Gahena. Anthu kawirikawiri amadzinamiza kuti akhoza kuchita zonse zofuna za moyo uno, ndi kuti adzalapa pambuyo. Koma Mulungu sanganamizidwe. Mtima umanka ukumaumiraumirabe pansi pa chinyengo cha chimo, ndiponso chikumbu mtima chimaumitsidwa zaka zikamapita. Ambiri amakalamba kufikira posatha kumakumbukira bwinobwino. Ena amamasulidwa mwadzidzidzi popanda kuchenjezedwa. Tiyeni tigonjere ku fanizo la wachuma woposa, yemwe anati. "Ndipo ndidzati kwa moyo wanga, Moyo iwe, uli nacho chuma chambiri chosungika kufikira zaka zambiri; tapumatu, nudye, numwe, nukondwere. Koma Mulungu anati kwa iye, Wopusa iwe, usiku womwe uno udzafunidwa moyo wako; ndipo zinthu zimene unazikonza zidzakhala za yani?" (Luka 12:19-20). Koma ngati tiri mwa Khristu Yesu, kaya ndi kufooka kwa malingaliro kapena kumwalira mwadzidzidzi, zomwe zimatiyembekeza, ife tiri wotetezedwa kwa muyaya mwa Iye.

Mdima.

Timawerenga kenekanso za mdima womwe unafika, "Ndipo ora lake pamenepo linali ngati lachisanu ndi chimodzi. Ndipo panali mdima pa dziko lonse kufikira ora lachisanu ndi chinayi, ndipo dzuwa linada." (Luka 23:44). Izi zimaonetsa za mdima womwe Yesu Mwana wamuyaya wa Mulungu anadutsamo mu umunthu Wake chifukwa cha machimo a anthu Ake pomwe amazunzika pa mtanda, anasiyidwa ndi Atate Wake wakumwamba. Mu kuvutika kwakukulu kwa moyo, atasenza mkwiyo chifukwa cha machimo a anthu Ake, Ambuye Yesu analira kuti, "Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji Ine?" (Mateyu 27:46). Ndani amene angathe kuzindikira kuzama kwa zomwe Yesu amadutsamo mwa chikondi cha kwa anthu Ake kuti awombole iwo? Mazunzo amenewa a thupi lake anali akulu, koma taonani mazunzo osaneneka a moyo Wake woyera!

Tiyeni ndi kunthunthumira tilingalire za kuwawa kwa Gahena, komwe kukuyembekeza iwo omwe sadziwa za mwazi woombola komanso chipulumutso mwa Yesu. Gahena ndi malo amene mkwiyo wa Mulungu ndi udani wa chimo umatsanulidwa kotheratu kwamuyaya, malo omwe kuli mdima osaneneka ndiponso malo opanda chiyembekezo. Mulungu ndi moto wonyeketsa kunja kwa Khristu Mpulumutsiyo.

Kuzunzika kuli konse komwe tikumana nako m'moyo uno, ngakhale kutakhala kwakukulu kwambiri, timakhala ndi chiyembekezo china chake kuti kuzunzikako kufika kumapeto (ngakhale mutakhala mu imfa), kapena kuti kuvutikako kuchepetsedwa. Koma chilango chosatha cha ku Gahena sichidzatha, komanso moyo sudzaonongeka. (Mateyu 25:46). Yesu analengeza (ponena mau opezeka ku Yesaya 66:24), 'Komwe mphutsi yawo siidzafa, ndi moto siuzimitsidwa". (Marko 9:44). Zokhudza munthu wa chuma yemwe ankakhala m'moyo wamataya, komanso wosamalira aumphawi, Yesu anati, "ndipo mwini chumayo adafanso, naikidwa m'manda. Ndipo m'Hade anakweza maso ake, pokhala nao mazunzo," Luka 16:22-23). Chifukwa "kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa chiweruziro." (Ahebri 9:27).

Zoonadi chiphunzitso choposa mu Mau a Mulungu chokhudza Gahena chinachokera pakamwa pa Muomboli. Koma Iye analawa chilango mthupi ndi moyo wake, chomwe chinayenera kufikira anthu ake, pamene anali pa mtanda wa Kalvari. Pokhapo pomwe anali mu umodzi ndi umulungu wake ndi pomwe akanatha kusenza katundu wolemera kwambiriyo. "Kotero Khristunso ataperekedwa nsembe kamodzi kukasenza machimo a ambiri, adzaonekera pa nthawi yachiwiri, wopanda uchimo, kwa iwo amene anamlindira, kufikira chipulumutso." (Ahebri 9:28).

Timawerenga kuti, "Ndipo nsaru yochinga ya m'Kachisi inang'ambika pakati." (Luka 23:45). Ichi chinachitika kuti kudzera mu mazunzo a Khristu njira ipangidwe yofika mu malo oyeretsetsa. Malo eni eniwo omwe amaimira kupezeka kwa msanga kwa Mulungu. Wansembe wamkulu yekha kamodzi pa chaka pansi pa chilamulo ndiye amaloledwa kulowa. Koma kudzera mu nsembe ya ulemerero ya Khristu chinsaru cha M'Kachisi chinang'ambika pakati. Mu umodzi ndi Khristu, yemwe ndi Wansembe Wamkulu wa Chipangano Chatsopano, anthu Ake owomboledwa amalowa mu kupezeka kwa chikondi kwa Mulungu. Palibenso chotchinga china, chifukwa chimo lachotesdwa ndiponso kutetezeredwa.

Ambuye Yesu anagonjetsa mphamvu zonse za Gahena ndi mdima. Chikole chotani ichi kwa anthu a Ambuye pomwe ayenda mu mavuto akulu! Angathe kuopsyezedwa ndi mantha a imfa, mayesero a Satana, kapena machimo akale omwe iwo awakumbukira; ndi kuti izi amazunguzika nazo mwa iwo okha. Umboni uwu ndi wakuti Davide analipo ndithu, pomwe ananena kuti, "Ndipulumutseni Mulungu; Pakuti madzi afikira moyo wanga."(Masalmo 69:1). Komatu kumapeto kwa Salmolo, Davide akupereka matamando, "Ndidzalemekeza dzina la Mulungu ndi kuliyimbira. Ndipo ndidzamubukitsa ndi kumyamika." (Masalmo 69:30). Kodi ndi akhristu angati omwe anatsimikiza kuti mu kulambira Ambuye kamba ka ubwino ndi chifundo chake, ndi kukhulupirira kuti kudzera mu chikhulupiriro pa Mwana wa Mulungu yemwe anapambana, iwo amasulidwa kulowa mu kuunika kwa ulemerero kwa Uthenga Wabwino. Pamene Paulo ndi Sila anapemphera ndi kuyimba matamando kwa Ambuye pakati pa usiku mkatikati mwa ndende, ndi pomwe Ambuye mwa ulemerero anawamasula iwo. (Machitidwe 16).

Pomwe tikuyenda kudutsa mu mdima waukulu m'miyoyo yathu, ndi kumaona ngati tasiyidwa ku chiyembekezo chathu ndiponso ngakhale kuyesedwa kuganiza kuti Mulungu watisiya ife, pamemepo tiyeni tilingalire za Yesu. Mazunzo ake anali akulu koposa "mazunzo athu ang'ono". Tikadziyang'ana ife eni ndi kuyang'ana pansi, timaona kuti tiri pa chizunzo chachikulu, koma pomwe tiyang'ana kwa Yesu ndi kudziwa chiyanjano chathu ndi Iye mu mazunzo Ake (Afilipi 3:10), zoonadi timamudziwa Iye ndipo kudzera mwa Mzimu timadzazidwa ndi chiyembekezo, chimwemwe ndi mtendere pakukhulupirira. Pamenepo tingathe kunena kuti, "Pakuti chisautso chathu chopepuka kanthawi chitichitira ife kulemera koposa kwakukulu ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyerera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha." (2 Akorinto 4:17-18).

Pokghala olumikizidwa kwa Yesu kudzera mwa Mzimu, tikhoza kunena moona pamodzi ndi wolemba Masalmo kuti; "Ndipo ndikati, Koma mdima undiphimbe, ndi kuunika kondizinga kukhale usiku:" (Masalmo 139:11). Izi ndiye nyengo zokoma ndi dalitso pomwe tidziwa ndi kukondwera mu malonjezano oposa ndi akulu awa, omwe ali eya ndi amen mwa Khristu Yesu Ambuyeyo. Mwa chikhulupiriro chotero, chomwe chiri mphatso ya mtengo wapatali ya Mulungu timamudziwa moona mtima mu zinthu zonse.

Chokhumba cha Ambuye pa Anthu Ake.

Timawerenga za kulira kwa Ambuye pa mtanda, "Ndimva ludzu" (Yohane 19:28). Izi sizikuonetsera mazunzo oopsya a kupachikidwa pa mtanda, komanso kukhumba kwa chikondi cha Ambuye kupita kwa anthu Ake omwe Iye anawaperekera moyo wake. Timawerenga za chikondi cha chisomo mu bukhu la Nyimbo ya Solomo, pomwe Mwana wa Mulungu analankhula mu uneneri wa mpingo. "Walanda mtima wanga, mlongo wanga, mkwatibwi; walanda mtima wanga ndi diso lako limodzi, ndi chinganga chimodzi cha pakhosi pako. Ha, chikondi chako nchokongola, mlongo wanga, mkwatibwi! Kodi chikondi chako sichiposa vinyo? Kunukhira kwa kwa mphoka yako ndi koposa zonunkhiritsa za mitundu mitundu!" "Nyimbo ya Solomo 4:9-10). Mpingo ndi kulankhula kuti; "Ndine wa wokondedwa wanga mnyamatayo, Ndine amene andifunayo." (Nyimbo ya Solomo 7:10). Wolemba ndakatulo akulemba izi bwino lomwe.

Thupi lake la umunthu

Linali lonse moto

Ndi ululu wakupachikidwa

Mwina mwake koipitsitsa

Ludzu lalikulu,

Monga pomwepo, wotembereredwa,

Anapachikidwa mu ululu waukulu.

Ndipo tsopano taonani,

Inu munauzidwa

Mudzisungire nthawi zonse pamaso panu!

Ludzu linakulirakulira

Kuti inu, akubwezeretseni,

Anakhumba kuti athire

Madzi ake amoyo pa iwe.

Lingalira, inde moyo wanga

Kuti wathunthu ukhale

Chinali chikhumbo chake chozama.

Iwe kodi ungakwaniritse

Kunyoza chisamaliro chake,

Chisomo chake chosaleka

Ukoma mtima wake ukanidwa?

Iwe kuti ukondwere

Kuti umve mau ake

Mkwati wa Kumwamba akuitana.

“Yenda pa mbali pa ine!

Ndikhumba ndikutsogolere

Mkwatibwi wanga wa dziko la pansi.

Zoopsya zake zonse kuzigonjetsa”.

Chifukwa cha mlomo wake woona

Osayerekeza kuinyika

Chinkhupule chako mu chinyengo chachabe,

Tembenukira ku Mau Ake

Omwe iwe wawamva,

Ndi omwe avundula

Mtima ku chikondi choona.

Ine ndiyankha,

Ambuye Mau anu akumwalira

Ngakhale kudzera m’misonzi yanga,

Mpulumutsi wanga,

“Za anthu zoipitsitsazo,

Ndimamvanso ludzu

La chisomo chanu ndi kukondera.”

Matamando apite kwa Inu,

Tsopano ndine mfulu,

Mfulu pa mtanda Wanu waululu

Imfa ilibe mbola,

Tsopano ndidzayimba

Kwa Inu, Mfumu yanga,

Osatinso mu ludzu kuti muzunzike.

(Hallgri'mur Pe'tursson)

Kwatha.

Poyankha ku kulira kwa Yesu kwakuti, "Ndimva ludzu," tikouna chochitika chomaliza cha nkhanza, kumuchepetsa ndi kumunyoza Yesu. "Kunaikidwako chotengera chodzala ndi vinyo wosasayo pa phesi la hisope, nachifikitsa kukamwa kwake. Pamene Yesu tsono adalandira vinyo wosasayo anati, Kwatha; ndipo anawerama mutu, napereka mzimu." (Yohane 19:29-30). Komatu mau amene anawalankhulawa ndi a ulemerero, pomwe analira "Kwatha". Mazunzo a Yesu tsopano anatha, ntchito ya chiombolo yamalizika ndiponso uchimo watetezeredwa. Sanagonjetsedwe ndi imfa, koma kuti anapereka moyo wake ndipo anagonjetsa imfa ndi Gahena. "Chifukwa cha ichi Atate andikonda Ine, chifukwa nditaya Ine moyo wanga, kuti ndikautengenso. Palibe wina andichotsera uwu, koma ndiutaya Ine ndekha. Ndiri nayo mphamvu yakuutaya, ndi yakuutenganso; lamulo ili ndinalindalira kwa Atate wanga." (Yohane 10:17-18).

"Kwatha" Ochimwa, amamva ichi,

Ndiko kulira kwa Wogonjetsa akumwalira;

"Kwatha!" Angelo anachilandira ichi,

Senzani choonadi chosangalatsa m'mwamba;

"Kwatha!"

Fotokozerani dziko lonse ndi kuthambo!

Chilungamo, kuchokera pa malo oyipa,

Mtendere wa ochimwa osatchingikanso

Chilungamo chimaona ndi chitsimikizo

Zomwe Mpulumutsi anachita ndi kusenza,

Chisomo ndi chifundo

Tsopano zionetsera masomphenya opanda malire.

Imvani Ambuye mwini akulengeza

Zonse anachita zomwe anabwerera,

Ochimwa, mwa inu nokha osinkhasinkha,

Iyi ndi nkhani yokondweretsa kwa Inu

Yesu amalankhula ichi

Ake ndi mau akukhulupirika ndi oona.

"Kwatha!" Zonse zatha;

Inde, chikho cha mkwiyo chatsanulidwa;

Choonadi ichi mau awa azindikira,

Apo chigonjetso chinapezeka;

Ndi chigonjetso

Palibe wina koma Yesu yekha akadapindula.

Vekani korona Mgonjetsi wamphamvu, vekani Iye,

Iye amene adani a anthu ake anagonjetsa!

M'mwambamwamba anapatsidwa mpando wachifumu!

Anthu ndi angelo, amafuula za kutchuka kwake!

Waukulu ndiye ulemerero wake!

Yesu anatenga dzina loposa onse.

(Kelly)

Mbali Yovulazidwa ya Yesu.

Pomaliza tiyeni tilingalire za kulasidwa m'nthiti kwa Yesu "Koma pofika kwa Yesu m'mene anamuona Iye, kuti wafa kale, sanathyola miyendo yake; koma m'modzi wa asirikali anangwaza ndi nthungo m'nthiti yake, ndipo panaturuka pomwepo mwazi ndi madzi."(Yohane 19:33-34). Izi zikukhazikitsa mwazi kuti utetezere pa chimo ndi madzi kuti ayeretse, madzi amoyo omwe aturuka kuchokera mu mtima wa Yesu.

Tikumbukirenso kuti mkwatibwi wa Adamu yemwe ndi Hava anatengedwa m'nthiti mwa Adamu (Genesis 2:21-24). Chimodzimodzinso, tiyeni tione mwa chikhulupiriro madalitso amuyaya omwe amaturuka kuchokera mu nthiti molasidwa mwa Yesu, opita kwa mkwatibwi wake, yemwe ndi mpingo woomboledwa.

Adamu payekha anazindikira,

Mulungu anamulengera mkwatibwi

Tulo tofa nato ululu wotsitsimutsa,

Anamtenga kuchokera ku nthiti zake zolasidwa.

Kwa mwamuna wake nthawi zonse anadziphatika.

Kukhala ndi iye nthawi zonse.

Kotero kwa Khristu mkwatibwi wake anapatsidwa,

Wotengedwa mu nthiti mwake molasidwa.

Ndi mkondo mnthiti mwake anang'ambidwa.

Kumasula funde loyeretsa.

Kotero machimo ake onse anakhululukidwa,

Mkwatibwi nthawi zonse apatulidwa.

Onani, moyo wanga! Ndi masomphenya kumwamba

Mwazi ndi madzi inu mudziwa

Kwa iwe Mulungu wakukwaniritsira,

Wobatizidwa mu mwazi woyenda woyeretsa.

Chikhulupiriro chivomereza kuzindikirika,

Za chisomo chomwe iye amapereka.

Popeza Ambuye wachisomo walola,

Tomasi wokaika akokedwa pafupi

Mwa kukhudza kodabwitsika

Kotero agonjera kuyandikira Iye sindingaloledwe Ine?

Zikaiko ndi mantha zonse zagonjetsedwa

Pomwe kuvulazidwa Kwake ndinakuonera patali.

Kuchokera mu mtima wake mitsinje ya machiritso,

Yokhetsedwa kuti apulumutse anthu Ake, inayenda;

Chisamaliro chonse cha Mulungu ndi chikondi zivumbulutsidwa,

Chisomo chake chonse pa ife chinaperekedwa,

Pomwe, ufulu wakuomboledwa unasindikizidwa,

Anapereka ngongole yomwe tinali nayo.

Kuti ndithe kuona bwino lomwe,

Muyeso wathunthu wa chisomo chake,

Amavumbulutsa mabala Ake bwino lomwe,

Chimandibweretsa kwa Iye maso ndi maso,

Kuti mapazi Ake ine moona mtima,

Ndi modzichepetsa ndithe kukumbatira.

(Hallgri’mur Pe’tursson).

Mtumwi Yohane analemba (potenga mau a Zakariya 12:10) “Adzayang’ana Iye amene anampyoza.” (Yohane 19:37). Pomwe titengeredwa ku kulapa, komwe ndi mphatso ya mtengo wapatali yochokera kwa Mulungu (Machitidwe 5:31), wochimwa amayang’ana mwa chikhulupiriro ku mabala omwe Yesu analandira ndiponso mwazi wolemera wotetezera womwe unaturuka. Wochimwa amalira mwa iye mwini, “chifukwa chiyani ine, chifukwa chiyani ine? Chifukwa chiyani m’modzi woipitsitsa ndi wopanda phindu, yemwe machimo ake apyoza. Ambuye wozunzika pa mtandayo!” Koma Muomboli alankhula mu chifundo kudzera mwa Mzimu, kuti zonse ndi chifukwa cha chisomo chonse. Kuti ulemerero ndi ulemu wa Mulungu zithe kuonetsedwa, ku matamando a ulemerero wake. (Aefeso 1:12) Kuti kumwamba owomboledwa a Ambuye athe kupereka matamando a muyaya kwa Mwana wa Nkhosa yemwe anaphedwa ponena kuti, “ Kwa Iye wakukhala pa mpando wachifumu, ndi kwa Mwana wa nkhosa zikhale chiyamiko, ndi ulemu, ndi ulemerero, ndi ufumu, kufikira nthawi za nthawi.” (Chivumbulutso 5:13).

MUTU 6

MUWOMBOLI WOUKA KWA AKUFA NDI WOPATSIDWA ULEMERERO

Yesu Adzivumbulutsa Yekha.

Mtumwi Paulo analemba kuti, “Ndipo ngati Khristu sanaukitsidwa, chikhulupiriro chanu chiri chopanda pake, muli chikhalire m’machimo anu.” (1 Akorinto 15:17) Ichi ndi chofunikira kwambiri pa chipulumutso chathu kuti, Khristu sadangomwalira kokha, komanso kuti anauka kwa akufa nakwera kupita kumwamba; kuonjezera apo ali Muombli waulemerero wopembedzera mpingo ndipo ali ku dzanja la manja la Mulungu Atate.

Tiyeni tiyambe ndi zomwe zinalembedwa m,Mau a Mulungu za amai obwera ku manda omwe thupi la Yesu linaikidwamo atapachikidwa pa mtanda nafa. “Koma tsiku loyamba la sabata, mbanda kucha, anadza kumanda atatenga zonunkhira adazikonza. Ndipo anapeza mwala unakunkhunizidwa kuuchotsa pa manda, ndipo m’mene analowa sanapeza mtembo wa Am,buye Yesu. Ndipo kunali, m’mene anathedwa nzeru nacho, taonani amuna awiri animirira pafupi pao atavala zonyezimira; ndipo m’mene anakhala ndi mantha naweramira pansi nkhope zao, anati kwa iwo, Mufuniranji wamoyo pa akufa? Palibe kuno Iye, komatu anuka; kumbukirani muja adalankhula nanu pamene analinso m’Galileya.” (Luka 24:1-6). Taonani nkhani ya ulemerero ndi ya chimwemwe iyi! Komatu ophunzira a Yesu anaona ngati zonenedwazo ndi

“nkhani zachabe ndipo sanamvera akaziwo.” (Luka 24:11). Sanazindikire mwa uzimu zochitika za kupachikidwa kwa Yesu pa mtanda.

Komabe, pamene tiwerenga mopitirira mu nkhani za Uthenga Wabwino, timaona chikondi ndi chipiriro chomwe Ambuye anaonetsa kwa ophunzira. Patapita ka nthawi tsiku lomwelo awiri a ophunzira ake ankayenda pa njira ya ku Emmau. Amasinkhasinkha za kupachikidwa kwa Yesu pa mtanda komanso kuti m’manda m’mene anamugonekamo munalibe, komatu sanafikira pa kuimariza nkhaniyi. (Luka 24:13-24). Kulingalira kwa umunthu wao kunalephereka. Koma Ambuye Yesu anawayandikira pafupi, nawamvetsera iwo ndipo mwa chikondi anawadzudzula iwo. Anaonetsa kuti zochitika izi, kuphatikizapo kuuka kwa akufa, zinachitika kukwaniritsa uneneri wa Chipangano Chakale. (Hosea 6:2, Masalmo 16:10).

Pomwe amamvetsa mau a iye yemwe amoneka kuti ndi mlendo (chifukwa Yesu anali asanavumbulitsire yekha kwa iwo), mitima yawo imatentha mwa iwo pomwe Yesu amalakhula ndi iwo, ndipo anapempha Iye kuti akhale nawo. Ndipo pamene Ambuye ananyema mkate pamaso pawo, maso awo anatseguka. Anazindikira kuti ndi Yesu Mpulumutsi wawo, ndipo chimwemwe chinadzaza mitima yawo. (Luka 24:30-35). Zoonadi ndi chokhumba chodala cha wokhulupirira aliyense, kuti angathe kumva liu la Yesu komanso kudziwa kupezeka kwake.

Ataonekera pa njira ya ku Emmau, Ambuye anonekera kwa ophunzira ake. Koma m’modzi wa iwo Tomasi yemwe panalibepo, anakana kukhulupirira umboni wawo wa kuuka kwa akufa kwa Yesu. (Yohane 20:25). Koma ngakhale Yesu anadza kwa Tomasi namuonetsa iye manja amabala ndi munthiti mwake. Tomasi anfuula modabwa ndi mozizwa, Mbuye wanga ndi Mulungu wanga”. Yesu ndipo analengeza, “Tomasi, Chifukwa wandiona Ine, wakhulupirira; odala iwo akukhulupirira angakhale sanaona.” (Yohane 20:28-29). Tiyeni potero tilingalire pa zinthu izi mopitirira pang’ono.

Ophunzira a Yesu anali ndi ganizo lawo la ntchito ya Yesu monga Messia. Ganizo ili limayenera kugwetsedwa kuti athe kudziwa njira za Mulungu ndi zolinga zake zamuyaya. Ambuye analengeza mu uneneri kuti, “Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova. Pakuti monga kumwamba kuli kutari ndi dziko la pansi, monga njira zanga ziri zazitari kupambana njira zanu ndi maganizo anga kupambana maganizo anu.” (Yesaya 55:8-9). Mosiyana ndi ophunzira, adani a Ambuye Yesu adaoneka ngati amakumbukira mau a Ambuye okhudzana ndi kuukanso kwake kwa akufa, kotero kuti anaika alonda kuti asunge manda. (Mateyu 27:62-66). Koma ichi chinali chidziwitso cha m’malingaliro chabe; anadana naye Ambuye Yesu ndipo “sakadalola kuti Munthu uyu alamulire” iwo.

Pali dalitso polingalira kuti Ambuye wouka kwa akufa anaonekera kwa Maria wa Magdala, awiri omwe amayenda pa njira ya ku Emmau komanso ophunzira ngakhale anali ndi zikaiko, ngakhale Petro atamukana, ngakhale anali ndi machimo awo onse; chifukwa anakondedwa ndi chikondi

chosatha kuyambira nthawi zosayamba. Yesu anali atakhetsa mwazi Wake wa mtengo wapatali ndi kuwaombola iwo, kotero panali chiyanjano chomwe sichikanatha kuthetsedwa. Kotero kuti, Ambuye ayenera kuti awonekere kwa iwo ndi kuvumbulutsidwa ndi mphamvu ya ulemerero. Ophunzira a Yesu ayenera kukhala mboni zomwe zinaona ndi maso za kuuka kwa thupi kwa Ambuye Yesu, pokhala ndi choonadi chodziwitsidwa mwa vumbulutso la umulungu, kuti iwo pamenepo athe kulalikira Uthenga Wabwino kufikira malekezero a dziko.

Timawerenga za nthawi zina zomwe ophunzira a Yesu kuti poyamba samamuzindikira Ambuye atangouka kwa akufa. Chomwechonso awiri oyenda pa njira ya ku Emmau, panali Maria Magdala (Yohane 20:15) ndiponso ophunzira akuwedza nsomba mu Nyanja ya Galileya. (Yohane 21:4). Koma pamene Ambuye anawalankhula, ndi pomwe anamuzindikira. Izi zikusonyeza kuti Yesu Muomboli wa ulemerero ndi Mwana wa Mulungu samaoneka ndi maso aku thupi, koma ndi chikhulupiriro chopatsidwa ndi Mulungu. Yesu anaphunzitsa kuti, "Palibe munthu angadze kwa Ine, koma ngati kupatsidwa kwa Iye ndi Atate." (Yohane 6:65. Werenganinso Yohane 6:44 ndi Luka 10:22). Pomwe Yesu yemwe ali "chizindikiro cheni cheni" cha munthu wa Mulungu Atate (Ahebri 1:3), analankhula ndi mphamvu, ndipo mitima yawo inatentha mwa iwo ndipo anadzazidwa ndi chimwemwe.

Tiyeni tikumbukire kuti Yesu ali "yemweyo dzulo, ndi lero, ndi ku nthawi zonse." (Ahebri 13:8). Yesu ali wodzala ndi chifundo ndiponso wokonzeka nthawi kutithandiza ife mzofooka zathu. Sanasinthe chiyambire cha masiku a chipangano chatsopano, chifukwa ali chimodzimodzi kwa muyaya. Mu masikuwa a Uthenga Wabwino, kuyambira kukwera kumwamba kwa Ambuye, Ambuye Yesu amavumbulutsidwa kwa wokhulupirira ali yense kudzera mwa Mulungu Mzimu Woyera. Patangotsala pang'ono kuti Iye apachikidwe, Ambuye anafotokoza momwe akadadzionetsera yekha. "Ngati wina akonda Ine, adzasunga mau anga; ndipo Atate wanga adzamkonda, ndipo tidzadza kwa iye, ndipo tidzayesa kwa iye mokhalamo. Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, Iyeyo adzaphunzitsa inu zinthu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu." Yohane 14:23,26). Kotero kuti, tiyeni tidze kwa Iye mwa chikhulupiriro kumudandaulira za malonjezano oposa ndi a mtengo wapatali.

Kufunikira kwa Kuukanso kwa Akufa.

Tisanafike pa nthawi ya kukwera kumwamba kwa Ambuye Yesu, tiyeni tione mwachifatse za chifukwa chomwe Ambuye Yesu ayenera kuuka kwa akufa. Paulo akufotokoza kuti Yesu "anatsimikidwa ndi mphamvu kuti ndiye Mwana wa Mulungu monga mwa Mzimu wa chiyero, ndi kuuka kwa akufa; ndiye Yesu Khristu Ambye wathu." (Aroma 1:4). Kotero kuti kuuka kwa akufa ndi chitsimikizo cha ulemerero cha ulamuliro wake wa Umulungu ndi umwana wamuyaya.

Pa chiyambi pa utumiki wa Yesu wa pa dziko la pansi anayeretsa Kachisi kwa iwo omwe anasandutsa Kachisiyo kukhala “nyumba ya malonda”. Olamulira a chi Yuda anakhumudwa kuti m’Galileya yemwe sankadziwika kuti akhoza kudzudzula boma lawo poyera chifukwa cha Kachisi. Ayuda ananena kwa Yesu kuti, “Chifukwa chake Ayuda anayankha nati kwa Iye, mutionetsera ife chizindikiro chanji, pakuti muchita izi? Yesu anayankha nati kwa iwo, Pasulani Kachisi uyu, ndipo masiku atatu ndidzamuutsa. Pamenepo Ayuda anati, Zaka makumi anai ndi zisanu ndi chimodzi analimkumanga Kachisiyu, kodi inu mudzamuutsa masiku atatu? Koma Iye anlikunena za kachisi wa thupi lake. Chifukwa chake atauka kwa akufa, akuphunzira ake anakumbukira kuti ananena ichi; ndipo anakhulupirira cholemba, ndi mau amene Yesu ananena.” (Yohane 2:18-22). Kuukanso kwa akufa kwa Ambuye, komwe kunachitidwa umboni ndi ambiri, zimatsimikiza kuti zoona mau ake ndi Mau a Mulungu, ndi kutinso ali mzimu ndiponso ndi moyo. (Yohane 6:63). Kuukanso kwa akufa ndi chizindikiro chakuti ulamuliro wonse wapatsidwa kwa Yesu monga mutu wa mpingo.

Kotero kuti, mtumwi Paulo anapemphera kuti mpingo wa ku Efeso uthe kudziwa za kuposa kwa mphamvu za Yesu ndi Umulungu wake pa mpingo. Izi zikuonetsedwa ndi kuukanso kwa akufa, pomwe Mulungu Atate “anamuukitsa kwa akufa, namkhazikitsa pa dzanja lake la manja m’zakumwamba pamwamba ukulu wonse, ndi ulamuliro, ndi mphamvu, ndi ufumu, ndi dzina liri lonse lotchedwa, si m’nyengo yino ya pansi pano yokha, komanso mwa iyo ikudza; ndipo anakonza zonse pansi pa mapazi ake, nampatsa Iye akhale mutu pamutu pa zonse.” (Aefeso 1:20-22).

Kuukanso kwa akufa ndi chitsimikizo cha ulemerero kuti Yesu anagonjetsa imfa, ndi kuti nsembe yake ya ulemerero inalandiridwa ndi Mulungu. Yesu “amene anaperekedwa chifukwa cha zolakwa zathu, naukitsidwa chifukwa cha kutiyesa ife olungama.”(Aroma 4:25). Patatha apo, “m’zonsezi, ife tilakatu, mwa Iye amene anatikonda.” (Aroma8:37). Adani athu onse anagonjetsedwa kwamuyaya. Wolemba Masalmo analengeza mu uneneri, “Auke Mulungu, abalalike adani ake.” (Masalmo 68:1).

Ambuye amatsogolera anthu Ake kudzera mu njira yoyenera, kupita patsogolo pawo mu zinthu zonse. Iye ndi “njira, ndi choonadi, ndi moyo.” (Yohane 14:6). Ali Mpulumutsi wouka kwa akufa komanso ali ndi moyo, yemwe akukhalabe ndi moyo kuti abweretse anthu okondedwa Ake ku ulemerero kumwamba. Wokhulupirira alimbikitsidwe kwambiri ndi kufunafuna mwa ulemerero kuukutsidwa kwamuyaya pamodzi ndi Khristu. “Iye amene anaukitsa Ambuye adzaukitsa ifenso pamodzi ndi Yesu, nadzatifikitsa pamodzi ndi inu.” (2 Akorinto 4:14). Izi ziwonetsera ulemerero wa chikondi cha Mulungu. “Koma Mulungu, wolemera chifundo, chifukwa cha chikondi chake chachikulu chimene anatikonda nacho, tingakhale tinali akufa m’zolakwa zathu, anatipatsa moyo pamodzi ndi Khristu (muli opulumutsidwa ndi chisomo), ndipo anatiukitsa pamodzi, natikhazikitsa pamodzi m’zakumwamba mwa Khristu Yesu.” (Aefeso 2:4-7). Pali kufunafuna uku

kwa kumwamba kwa okhulupirira, pokhala womasulidwa ku thupi ili la dziko la pansi la uchimo ndi imfa, ndi kukhala wotengedwa kuchoka ku kusafa kunka kukakhala pamodzi ndi Yesu mu ngwiro. (1 Akorinto 15:42-58, 1 Yohane 3:2, Afilipi 3:20=21).

Kudzera mu kuukanso kwa akufa tinabadwanso kwatsopano kwa mzimu kuti tithe kulambira Khristu wamoyo osati wakufa. Tiri ndi chiyembekezo chamoyo mwa Khristu. "Wodalitsika Mulungu ndiye Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, Iye amene, monga mwa chifundo chake chachikulu, anatibalanso ku chiyembekezo cha moyo, mwa kuuka kwa akufa kwa Yesu Khristu." (1 Petro 1:3). Chikondi cha Mulungu ndi chotero kuti m'mayesero athu akulu, mzimu amativumbulutsira Khristu ife. Paulo analengeza, "koma tokha tinakhala nacho chitsutso cha mwa ife tokha, kuti tisalimbike pa ife tokha, koma pa Mulungu wakuukitsa akufa."(2 Akorinto 1:9). Wolemba Masalmo ali mu masautso akulu adaona ichi mwa chikhulupiriro ndipo anatonthozedwa: "Inu mudzauka, ndi kuchita nsoni Ziyoni, Popeza yafika nyengo yakumuchitira chifundo, nyengo yoikika." (Masalmo 102:13).

Tilole kutsogozedwa kuti tilingalire moposera pa za kuukanso kwa akufa, ndi kuti kuukanso kwa akufa, ndi kuti tipemphere kuti Mau a Mulungu atsegulidwe kuti tiwazindikre, kuti tikhoza kuyanjana tsiku ndi tsiku ndi Yesu Wamoyo. Tiyenera kudziwa zambiri za mphamvu ya kuukanso kwa akufa Kwake. Ichi chinali chokhumba chokoma cha Mtumwi Paulo. (Afilipi 3:10-11). Mzisautso zathu tingathe kuphunzitsika mozama kwambiri za masautso osaneneka a Ambuye Yesu chifukwa cha anthu ake okondedwa, komatu ndi kuyang'ana kwa Ambuye Yesu wouka kwa akufa mwa chikhulupiriro, kupemphera kuti Mulungu athe kutikweza mwamphamvu pamwamba pa zinthu za moyo uno. Timagonjetsa kudzera mwa Khristu, yemwe anagonjetsa dziko lapansi. (Yohane 16:33). Chigonjetsochi ndi chathu kudzera mwa Yesu, monga Mtumwi Yohane analemba. "Koma ndani iye wolilaka dziko la pansi, koma iye amene akhulupirira kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu." {1 Yohane 5:5).

Kukwera Kumwamba.

Atauka kwa akufa Ambuye Yesu, Mau a Mulungu amalankhula momveka bwino za kukwera kwake mu thupi kwa kumwamba. Yesu anatsogolera ophunzira ake "Ndipo anaturuka nawo kufikira ku Betaniya, nakweza manja ake, nawadalitsa. Ndipo kunali pakuwadalitsa Iye analekana nawo, natengedwa kunka Kumwamba. Ndipo anamlambira ku Yerusalemu ndi chimwemwe chachikulu." (Luka 24:50-52). Momwenso lero tiyeni mwa chimwemwe tilingalire pa madalitso ndi ulemerero wa kukwera kumwamba kwa Ambuye Yesu.

Yesu ayenera kulowa kumwamba kumeneko mu thupi lomwelo limene Iye anakhalamo ndi kufa kuti ayimirire zomuyenereza matamando a nsembe yake yangwiro, kumeneko kuti apembedzere anthu Ake akondedwa pamaso pa Mulungu. Analowa malo oyeretsetsa amuyaya ndiponso a kumwamba, amene chihema cha dziko la pansi chinali chithunzithunzi chake. "Koma

atafika Khristu, Mkulu Wansembe wa zokoma zirinkudza, mwa chihema chachikulu ndi changwiro choposa, chosamangika ndi manja, ndiko kunena kuti, chosati cha chilengedwe ichi, kapena mwa mwazi wa mbuzi ndi ana a ng'ombe, koma mwa mwazi wa Iye yekha, analowa kamodzi ku malo opatulika, atalandirapo chiombolo chosatha. Pakuti Khristu sanalowa m'malo opatulika omangika ndi manja, akutsanza oonawo; komatu m'Mwamba momwe, kuonekera tsopano pamaso pa Mulungu chifukwa cha ife" Ahebri 9:11-12,24).

Kuchokera ku kulowa kumwamba kwa Khristu ndi pomwe Mzimu Woyera waperekedwa. Chionetsero chapadera pa tsiku la Pentekoste, (phwando la zoyambirira kucha) mwa ka nthawi kochepa zanatsatiridwa pambuyo pake ndi kukwera kumwamba kwa Khristu, monga adalonjezera Iye kwa ophunzira ake asanapachikidwe pa mtanda. "Koma ndinena Ine choonadi ndi inu; kuyenera kwa inu kuti ndichoke Ine; pakuti ngati sindichoka, Nkhosweyo sadzadza kwa inu; koma ngati ndipita ndidzamutuma Iye kwa inu." (Yohane 16:7).

Mzimu Woyera amavumbulutsa choonadi mwa Yesu komanso kupereka ulemerero kwa Khristu m'mitima ya mpingo. "Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa choonadi, adzatsogolera inu m'choonadi chonse; pakuti sadzalankhula za Iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulakirani. Iyeyo adzalemekeza Ine; chifukwa adzatenga za mwa Ine, nadzalalikira kwa inu." (Yohane 16:13-14). Dziko losakhulupirilali silingalandire Mzimu Woyera Nkhosweyo, koma amakhala kwamuyaya ndi anthu akondedwa ake a Ambuye. Kudzera mwa Mzimu Ambuye Yesu wouka kwa akufa ndi wokwera kumwamba amadza nakhala ndi wokhulupirira woona mtima. (Yohane 14:16-18).

Wolemba Masalmo Davide ananena za mphatso yodalitsika iyi ya Mzimu kwa ochimwa yomwe sanayenera kuilandira koma pokhapo ngati ali opulumutsidwa mwa Muomboli, yotsika kuchokera mwa kukwera kwake kwa kumwamba kwa Ambuye Yesu. "Inu munakwera kunka kumwamba, munapita nawo undende kuuyesa undende; Munalandira zaufulu mwa anthu, Ngakhale mwa opikisana nanu, kuti Yehova Mulungu akakhale nawo. Wolemekezeka Ambuye, tsiku ndi tsiku atisenzera katundu, ndiye Mulungu wa chipulumutso chathu."(Masalmo 68:18-19). Ulemerero wotani uwu womwe chikondi cha Mulungu wakuti atumize Mzimu Woyera Nkhosweyo kwa anthu osayenera otere ndiponso ochimwitsitsa, omwe sayenera china chiri chonse koma Gahena! Dalitso ili ndi losaneneka kuti Yesu anafa, anaukanso kwa akufa ndi kukwera kulowa kumwamba, kuti ziwalo za thupi lake zobisika, zomwe ndi mpingo, zikhale mokhalamo mwa Mulungu kudzera mwa Mzimu Woyera. (Aefeso 2:22).

Mu Mau a Mulungu, Mzimu Woyera amatchulidwanso kuti "Mzimu wa Khristu" komanso "Mzimu wa Mulungu" (Aroma 8:9), pamenepo kupereka umboni winanso wa umulungu wa Ambuye Yesu Khristu. Mzimu amakhala mkati mwa wokhulupirira ndi kupereka umboni wa ulemerero wa umwana wathu ku miyoyo yathu. "Pakuti onse amene atsogozedwa ndi mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu; Pakuti inu simunalandira mzimu wa ukapolo

kuchitanso mantha; koma munalandira mzimu wa umwana, umene tifuula nawo, kuti Abba, Atate. Mzimu yekha achita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu."(Aroma 8:14-16). Chomwe chichitidwa mu moyo chimabereka chipatso m'moyo wa okhulupprira woona. Miyoyo yawo imapatulidwa kupereka ulemu, ulemerero ndi kutumukira Mulungu Atate wawo wa kumwamba. Izi sizimachitika mwa mantha kapena ndi mtima wa ntchito, chifukwa mphamvu ya Mzimu imapangitsa chikondi chotere kwa Mulungu m'mitima mwawo kotero kuti amakondwera kutumikira Iye. Komatu zomvetsa chisoni kuti, mkhristu pomwe ali m'moyo uno amakhalabe m'moyo wa thupi la dothi. Munthu watsopano wa chisomo nthawi zonse amatsutsana ndi munthu wakale wa chimo, ndipo nkhondo yake nthawi zambiri imakhala yoopsya. (Aroma 7). Ndiye tiyeni tiyang'ane m'mwamba ndi chikhulupiriro, chifukwa Muomboli wathu walowa kumwamba komweko ndi kuti atipembedzera ife kumeneko pamaso pa Atate. Mwa umodzi ndi Ambuye Yesu wouka kwa akufa, chipulumutso chathu ndi chokhazikika kwa muyaya.

Kudzera mu mphamvu ya Mzimu yowonetsedwa mwa chikhulupiriro chopatsidwa ndi Mulungu, chomwe ndi chikhazikitso cha zinthu zoyembekezeka, ndi momwe tidziwira chikondi cha Mulungu. Mtumwi Paulo anaonetsa chokhumba chake mwa pemphero, "Kuti Khristu akhale chikhalire mwa chikhulupiriro m'mitima yanu; kuti ozika mizu ndi otsendereka m'chikondi, mukakhozetu kuzindikira pamodzi ndi oyera mtima onse, kupingasa, ndi utali, ndi kukwera, ndi kuzama nchiyani; ndi kuzindikira chikondi cha Khristu, chakuposa mazindikiridwe, kuti mukadzazidwe, kufikira chidzalo chonse cha Mulungu." (Aefeso 3:17-19).

Muomboli Wopatsidwa Ulemerero.

Mu mitu yomwe yapitayi tinakhazikika pa Mwana wamuyaya wa Mulungu kuti anadziweramitsira pansi modzichepetsa kuti atenge umunthu ndiponso kuti azunzike ndi kufa, ataphimba ulemerero Wake wamuyaya pamene adakhala monga munthu, Khristu Yesu. Tiyenera tsopano kulingalira mopitirira za nkhani yokhudza kukwera kumwamba kwa Ambuye Yesu, kunena za kulowa kwa ulemerero kwa kumwamba mwa chipambano. Wolemba Masalmo akukondwera za ichi mu uneneri. "Weramutsani mitu yanu, zipata inu; Ndipo kwezani inu, zitseko zosatha: Kuti Mfumu ya ulemerero ilowe." (Masalmo 24:7). Yesu wavekedwa kolona naikidwa pa mpando wachifumu mu ulemerero monga mutu wa mpingo, kupembedzera nthawi zonse kwa Mulungu Atate.

Mau a Mulungu amakhazikitsa mphatso zodala zomwe zimachokera ku ichi, chifukwa Yesu. "Mulungu anamukweza ndi dzanja lake la manja, akhale Mtsogoleri ndi Mpulumutsi, kuti kuti apatse kwa Israeli kulapa, ndi chikhululukiro cha machimo." (Machitidwe 5:31). Zodala ndi zosoweka koposa mphatso izi! Kodi wochimwa wa mtima wouma, yemwe sasamalira china chiri chonse cha zinthu za uzimu, akadatheka bwanji kubweretsedwa modzichepetsa pa mapazi a Yesu ndi kulapa machimo awo? Kuonjezera apo, mu nthawi ya zochitika za mphamvu ya

umulungu amalandira payekha lonjezo la mtengo wapatali la chikhululukiro lomwe lalankhulidwa kudzera mwa Mzimu ku miyoyo yawo.

Pali kusungidwiratu kwa chiwalo chili chonse cha mpingo Wake wa dziko la pansi chilinganizo cha kuti atamwalira adzapatsidwe ulemerero pamodzi ndi Khristu kumwamba. Mtumwi Paulo analemba: “Mzimu yekha achita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana aMulungu; ndipo ngati ana, pomweponso olowa nyumba; inde olowa nyumba ake a Mulungu, ndi olowa anzake a Khristu; ngatitu ife timva zowawa pamodzi naye, kuti tikalandirenso ulemerero pamodzi ndi Iye.’ (Aroma 8:16-17). Paulo analembanso za chitsimikizo chodala kuti chitilimbikitse mu nthawi yoipa ino ya dziko la pansi: “Khristu mwa inu, chiyembekezo cha ulemerero.” (Akolose 1:27).

Ichi ndicho chipatso chodala cha pemphero la Ambuye kwa Mulungu Atate la anthu Ake asanapereke moyo wake pa mtanda. “Ndipo ulemerero umene mwandipatsa Ine ndapatsa iwo, kuti akhale amodzi monga ife tiri amodzi; Ine mwa iwo, ndi Inu mwa Ine, kuti akhale angwiro mwa m’modzi.”(Yohane 17:22-23). Pemphero la Khristu limaonetsera chikondi chamuyaya cha Mulungu Atate kwa Mwana wake wamuyaya, ndi kuti Ambuye Yesu ataye moyo wake kuti chikondi ichi ndi ulemerero zithe kukwaniritsidwa pa anthu Ake awomboledwa. Cholinga chamuyaya cha Ambuye ndi chakuti owomboledwa apereke malemekezo kwa muyaya pa mpando wake wa chifumu. (Chivumbulutso 14:17). Monga Mlengi wamuyaya ndi wamphamvu yonse wa kumwamba ndi dziko la pansi, “palibe woletsa dzanja lake, kapena wakunena naye, Muchitanji?” (Danieli 4:35). Kotero kuti, palibe chomwe chingalekanitse anthu a Ambuye “ ndi chikondi cha Mulungu, chimene chiri mwa Khristu Yesu Ambuye wathu.”(Aroma 8:39). Wokhulupirira angathe kunena pamodzi ndi mtumwi, “Tikonda ife, chifukwa anayamba ndi Iye kutikonda.” (1 Yohane 4:19). Taonani, chikondi cha Mulungu!

Zotsatira m’Moyo wa Wokhulupirira.

Tiyeni tsopano tiyang’ane kumwamba mwa chikhulupiriro, chikondi ndi chimwemwe kwa kufunafuna kwa kumwamba, kutsogolera miyoyo yomwe ipereka ulemu, yodzala ndi zipatso za Mzimu. “Taonani, chikondicho Atate watipatsa, kuti titchedwa ana a Mulungu; ndipo tiri ife otere. Mwa ichi dziko la pansi silizindikira Iye. Okendedwa, tsopano tiri ana a Mulungu, ndipo sizinaoneke chimene tidzakhala. Tidziwa kuti, pa kuoneka Iye, tidzakhala ofanana ndi Iye. Pakuti tidzamuona Iye monga ali. Ndipo yense wakukhala nacho chiyembekezo ichi pa Iye, adziyeretsa yekha, monga Iyeyu ali Woyera.” (1 Yohane 3:1-3).

Tiyeni tilingalire monga momwe zinthu za dziko la pansi zikhalira, yemwe amene timkonda ndi amene timakhumba kukhala ndi kulankhula naye. Kodi izi ndi zoona chimodzimodzi ku uzimu ndi zinthu zamuyaya? Kodi timayenda motero ndi Yesu Khristu, kufunafuna mau Ake ndi kupemphera kwa Iye, moona mtima kukhumba kumva liu lake kudzera mwa Mzimu Woyera?

Kawiri kawiri tikamasinkhasinkha za izi, tizidzimvera manyazi poganizira za chimo ndi chidetso, ndi kulira pamodzi ndi mtumwi Paulo kuti: “Munthu wosauka ine; adzandilekanitsa ndani m’thupi la imfa iyi? Ndiyamika Mulungu, mwa Yesu Khristu Ambuye wathu. Ndipo chotero ine ndekha ndi mtimatu nditumikira chilamulo cha Mulungu; koma ndi thupi nditumukira lamulo la uchimo.” (Aroma 7:24-25).

Chipulumutso chathu ndi kusungidwa kwathu m’moyo uno kumapezeka pa choonadi cha ulemerero chakuti Mulungu amakonda anthu ake ndi chikondi chonka muyaya. (Yeremiya 31:3). Kotero kuti ndi cholinga chake chamuyaya kuti awakokere kwa Iye mwini ndi ukoma mtima ndi kuwadalitsa iwo ndithu. Chilimbikitso chotani chotere kuti tithe kupemphera ndi kulindira pa mayankho a mtendere! Mulungu ndi wamphamvu yonse, ndipo chifuniro chake chidzakwaniritsidwa ndithu. Komabe, nthawi zina sitimazindikira za machitachita ake, ndipo kawiri kawiri Ambuye amatilanga ndi kutidzudzula ife. Koma zonsezi amazichita mu chikondi. Mtumwi Paulo analemba kuti, “ Mwana wanga, usayese chopepuka kulanga kwa Ambuye, kapena usakomoke podzudzulidwa ndi Iye: pakuti iye amene Ambuye amkonda amlanga, nakwapula mwana ali yense amlandira.” (Ahebri 12:5-6). Pemphero lathu nthawi zonse likhale lakuti, “Ambuye mutionjezere chikhulupiriro chathu!”

Ngati kuli kwakuti tikhulupirire munthu, tidzakhumudwa nthawi zonse mu ulemu wina wake, chifukwa chikondi cha munthu sichili changwiro. Ngati tingasankhe kulankhula ndi wina wake wofunika, atha kukhalanso ndi ena ambiri okhumba kulankhula ndi iye, kotero kuti amachotsdwa chidwi pa inu kapena akhoza kukhala kuti watanganidwa kwambiri. Koma ngakhale patakhala okhulupirira ambiri enanso ofunafuna Mulungu Atate, kumudandaulira mu dzina la Ambuye Yesu kudzera mwa Mzimu Woyera, palibe malire aliwonse otero, kapena zotchinga. Amamva wina aliyense payekha ndipo amadziwa zowadandaulitsa ndi zosowa zawo. “Asanaitane Ine, ndidzayankha; ndipo ali chilankhulire Ine ndidzamva.” (Yesaya 65:24). Ambuye wamphamvu yonse amamva ndi kulankhula mwachisomo kwa wina aliyense, amadziwa zosowa zawo ndi kuwasamalira iwo. Tisaope ngati Ambuye akuoneka ngati akuchedwa, chifukwa ndi wanzeru zonse ndipo amadikira kuyankha pemphero. “Chifukwa chake Yehova adzadikira, kuti akukomereni mtima, ndipo chifukwa chake Iye adzakuzidwa, kuti akuchitireni inu chifundo; pakuti Yehova ndiye Mulungu wa chiweruziro; odala ali onse amene amdikira Iye.” (Yesaya 30:18).

Tiyeni ife aliyense payekha tidzisanthule tokha, kuti mwina tingaperewere pa chidziwitso chakupumulutsa cha Khristu. Maonekedwe omvetsa chisoni a Ambuye Yesu wopatsidwa ulemerero, anafotokozedwa ndi mtumwi Yohane. Uwu unali ulemerero wokwezekedwa kuti Yohane anagwa pa mapazi ake. Yohane analemba; “Ndipo tsitsi la pamutu pake linali loyera ngati ubweya woyera, ngati chipale chofewa; ndi maso ake ngati lawi la moto; ndi mapazi ake ngati mkuwa wonyezimira, ngati woyengeka m’ng’anjo; ndi mau ake ngati mkokomo wa madzi

ambiri. Ndipo mdzanja lake la manja munali nyenyezi zisanu ndi ziwiri; ndi m'kamwa mwake mudaturuka lupanga lakuthwa konse konse; ndipo nkhope yake ngati dzuwa lowala mu mphamvu yake. Ndipo pamene ndimuona Iye, ndinagwa pa mapazi ake ngati wakufa; ndipo anaika dzanja lake la manja pa ine, nati, Usaope, Ine ndine woyamba ndi wotsiriza, ndi Wamoyoyo; ndipo ndinali wakufa, ndipo taona, ndiri wamoyo kufikira nthawi za nthawi, ndipo ndiri nazo zofungulira za imfa ndi Hade."(Chivumbulutso 1 :14-18).

Tiyenera kufufuza maonekedwe oyenera ndi auzimu a chikondi cha Khristu. Pali anthu ambiri lero omwe amakamba za chikondi cha Khristu, koma samadziwa kuti ndi oyera, waulemerero komanso wamphamvu yonse, ali yekhayo wolamulira wa mpingo. Mau a Mulungu amafotokoza kuti Yesu anapanga "chikwapu cha zingwe zazing'ono" naturutsa osintha ndalama ndi ogulitsa ng'ombe, nkhosa ndi nkhunda, zomwe zimadetsa Kachisi, anatembenuza magome awo. (Yohane 2:13-17). Paulo analembanso za kuonekera kochititsa mantha kwa kubweranso kwachiwiri komwe kudachititsa manyazi ndi chionongeko kwa ochimwa. "ndi kwa inu akumva chisautso mpumulo pamodzi ndi ife, pa vumbulutso la Ambuye Yesu wochokera Kumwamba pamodzi ndi angelo a mphamvu yake, m'lawi la moto, ndi kubwezera chilango kwa iwo osamdziwa Mulungu, ndi iwo osamvera Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu amene adzamva chilango, ndicho chionongeko chosatha chowasiyanitsa ku nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemerero wa mphamvu yake, pamene adzadza kudzalemekezedwa mwa oyera mtima ake, ndi kukhala wodabwizitsa mwa onse akukhulupirira (popeza munakhulupirira umboni wathu wa kwa inu) m'tsiku lija." (2 Atesalonika 1:7-10).

Ambuye adzaonetsetsa kuti anthu Ake ayengeke mu moto ndi kupangidwa akuti agwiritsidwe ntchito ndi Iye. Kusalungama ndi kukonda kwa dziko la pansi sizingakhale pomwe ntchito ya Mzimu yadziwidwa moona mu mtima. Koma pomwe pali mantha a umulungu, pamakhala chipulumutso. Wolemba Masalmo analemba kuti. "Indedi chipulumutso chake chiri pafupi ndi iwo akumuopa Iye: Kuti m'dziko mwathu mukhale ulemu. Chifundo ndi choonadi zakomanizana; chilungamo ndi mtendere zapsyopsyonana." (Masalmo 85:9-10). Kwa anthu a Ambuye pali ulemerero ndi mphamvu zolumukizidwa ndi chikondi mwa Muomboli wodala, yemwe wasambitsa iwo mu mwazi wake wamtengo wapatali. Chikondwerero chake chiri ndi mkwatibwi wake, mpingo. (Nyimbo ya Solomo 4:9-10 ndi 7:10).

Lemekezni Ambuye wa Ulemerwero.

Tiyeni tipemphere kuti tithe kudzazidwa ndi chikondi cha Khristu, chikondi chomwe chaonetsedwa m'miyoyo yathu ku ulemu ndi ulemerero wake; chikondi kwa Mulungu m'modzi mwa Atatu ndi chikondi kwa wina ndi mzake. Pamenepo ndipo tidzalemekeza Mulungu mu mau ndi mu ntchito, monga wolemba ndakatulo anafotokozera.

Idzani, inu omwe mudziwa ndi kumuopa Ambuye,

Ndi kukweza miyoyo yawo kumwamba;

Mtima uliwonse ndi liu lomwe,

Kuti ayimbe kuti Mulungu ndiye chikondi.

Choonadi cha mtengo wapatali ichi mau ake alengeza,

Ndi zifundo zake zonse zitsimikiza;

Yesu, Mphatso ya mphatso iwonekera,

Kuti awonetse kuti Mulungu ndiye chikondi.

Taonani chipiriro chake chitalikitsidwa,

Kwa iwo omwe kuchokera kwa Iye ayenda kuti apeze kofikira;

Ndi mayendedwe awo onse, kuyambira poyamba mpaka mapeto,

Zimalengeza kuti Mulungu ndiye chikondi!

Ife tonse, pomwe tiri pansi pano,

Dalitso loposa ili tilitsimikiza;

Kufikira mitima yofunda m'mayiko owala,

Idzafuula kuti Mulungu ndiye chikondi!

(Burder).

Dalitso liri lonse limatsikira kwa ife kudzera mwa Ambuye Yesu ndi chisomo chake cha ulemerero. Mulungu Atate chifukwa cha chikondi anatuma Mwana kubwera ku dziko ili lotembereredwa ndi uchimo kuti awombole mpingo. Mulungu Mzimu Woyera ndiye yemwe amavumbulutsa Khristu ku miyoyo ya anthu. Apa tikuona magwiridwe ntchito a Mulungu mwa Utatu wake poonetsera chikondi cha Mulungu. Mulungu m'modzi mwa Atatu ndi chiphunzitso chodzala ndi dalitso komanso lofunika ku chipulumutso. (I Yohane 5:1-7).

Mau a mtumwi Paulo pomaliza kalata yake yolembera mpingo wa ku Akorinto ndiwo kumalizitsa kwabwino kwa chokhumba cha mtumiki woona wa Uthenga Wabwino. Pamene tikufika ku mapeto kwa bukhu ili, wolemba bukhuli akukhumbanso moona mtima chimodzimodzi monga Paulo. Pakhale kukhazikitsika ndi kupangidwa kwa ngwiro (uku ndi kukhwima mu mayendedwe athu monga Mkhristu, ngakhale tiri ochimwa koma opulumutsidwa mwa chisomo) komwe kuli kosowekera mu mpingo. Paulo analemba kuti: “Chotsalira abale, kondwerani. Muchitidwe angwiro; mutonthozedwe; khalani mumtendere; ndipo Mulungu wa chikondi ndi mtendere akhale pamodzi ndi inu. Lankhulanani ndi chipsyopsyono chopatulika. Oyera mtima onse alankhula inu. Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu, ndi chikondi cha Mulungu, ndi chiyanjano cha Mzimu Woyera zikhale ndi inu nonse.” (2 Akorinto 13:11-14).

CHIKONDI CHA MULUNGU.

Bukhu ili limakhazikitsa chiphunzitso cha Mau a Mulungu chokhudza chikondi cha Mulungu, chomwe, chinaonetsedwa mu moyo, imfa ndi kuuka kwa akufa kwa Ambuye Yesu, chovumbulutsidwa ndi Mzimu Woyera.

Wolemba bukhu ili akunena kuti chikondi cha Mulungu sichaulere kokha, komanso chopanda banga ndi choyera. Pomwe chikondi cha Mulungu chazindikirika moonadi, payenera kukhala zitsimikizo zooneka bwino m'moyo ndi chikhalidwe cha okhulupirira. Chikondi cha Mulungu chimakokera ochimwa kwa Khristu, ndi kudzera mu mphamzu ya Mzimu, amafikitsidwa ku kulapa ndi chikhulupiriro chopulumutsidwa nacho. Izi sizidzakhala za pamwambamwamba chabe, koma idzakhala ntchito ya mphamvu ya Mulungu Mzimu Woyera mu mtima, kumukonzekeretsa okhulupirira ku ulemerero. Mkhristu anaitanidwa kutsata Yesu, yemwe mu chikondi anavutika mosatheka kuneneka, anataya moyo wake ndipo anakhetsa mwazi wake wa mtengo wapatali kuwombola ndi kuyeretsa kuchokera ku chimo ndi chidetso.

Yesu ayenera kukhala alefa ndi omega, woyamba ndi womaliza m'miyoyo yathu, chipembedzo ndi mipingo. Chokhumba mwa pemphero cha wolemba bukhuli ndi chakuti Yesu akwezekedwe ndiponso owerenga adalitsidwe m'miyoyo yawo kudzera mwa Mzimu Woyera povumbulutsa chikondi cha Mulungu.

Dr Ian Sadler (B Ss, Ph D, D Lit), ndi membala wa mpingo wa Strict Baptist Church. Anaphunzira ntchito ya kafukufuku wa za Sayansi, koma akugwira ntchito mu Madera a Zaumoyo ndi Chitetezo cha Thanzi. Ali pa banja laling'ono. Analembanso mabukhu a *Chinsinsi, Babulo Woposa,* ndi *Yesu Ndiye njira.*

HELPFUL INFORMATION

1. THE FIRST PAGE IS THE FRONT COVER OF THE BOOK.

2. THE LAST PAGE IS THE BACK COVER OF THE BOOK.

3. THE PAGES INDICATING THE PLACE WHERE THE CHAPTERS ARE FOUND ARE WRITTEN FOR THE SAKE OF THOSE WHO MAY ONLY READ THE TYPED INFORMATION. THIS MEANS THAT THE PRINTERS OF THE BOOK WILL INDICATE THE PAGES ACCORDING TO THEIR PRINT SETTING.

4. THE PAGES MAY ALSO HELP THOSE WHO MAY READ FROM THE INTERNET WHEN IT IS PUT IN THE WEBSITE.

5. THE SPACING BETWEEN THE LINES OF THE EACH PARAGRAPH OF THE POEMS MAY BE REDUCED IF IT MAY BE REQUIRED TO BE SO.